



# **Nkhani za Kuyandikira ndi Kutalikirana zochokera ku Central-Eastern Europe ndi South-Eastern Africa**

## **Nsalu Yolukidwa ndi Zikhalidwe Zosiyanasiyana**

Yamasuliridwa ndi Justin Mwale ndikukonzedwa ndi Marita Banda.

Kumasulira ndi kukonza kwa bukuli m'chiNyanja kwatheka chifukwa cha thandizo ndi mgwirizano wa Women's History Museum (WHM), Art Transparent ndi Pro Progressione.

Akonzi:

Dr Urszula Markowska-Manista  
Natasha Omokhodion-Kalulu Banda



## **MAWU OTHOKOZA**

Kufalitsidwa kwa bukuli ndi zotsatira za ntchito ya anthu ambiri. Tikufuna kupereka kuthokoza kwathu kwa anzathu a ku Women's History Museum ku Zambia, Nafasi Art Space ku Tanzania, Pro Progressione ku Hungary, International Theatre Institute ku Germany ndi Institute of Transmedia Design ku Slovenia komanso mgwirizano wonse wa Deconfining chifukwa cha thandizo lawo losiyanasiyana.

Kuthokoza kwathu kwakukulu kukupitanso kwa olemba onse omwe ali ndi zolemba zawo mu msonkhanowu. Mawu alionse omwe ali m'bukuli ndi apadera, osati kungopereka malo atsopano olingalira komanso kuwulula tizidutswa ta miyoyo ya olemba ndi kulumikizana kwawo ndi luso m'malo ndi mipata yosiyanasiyana.

Tikuthokozanso anthu onse ndi mabungwe omwe adathandizira ndalama ntchito yapaderayi, kuphatikizapo European Union Creative Europe program, Ministry of Culture and National Heritage ya dziko la Poland ndi mamembala a Bosch Alumni Network.



DECONFINING Arts, Culture & Policies in Europe & Africa 3

### M'NDANDANDA WA ZOMWE ZILI M'BUKULI

|  |     |
|--|-----|
| <i>Urszula Markowska-Manista, Natasha Omokhodion-Kalulu Banda</i><br>Mawu Oyamba                     | 4   |
| <i>Art Transparent</i><br>Za polojekiti ya Deconfining   | 9   |
| <i>Karolina Bieniek &amp; Kamil Kawalec</i><br>Zizindikiro Zodbawitsa                                | 10  |
| <i>Shilika Chisoko</i><br>Kumasula Mfundo za Malo ndi Mpata  | 19  |
| <i>Chiteu Kasongo</i><br>Ulusi wa Umodzi   | 30  |
| <i>Karolina Marcinkowska</i><br>Kupita ku Chidziwitso Chokhudza Thupi                                | 55  |
| <i>Mwaka Siluonde</i><br>Omangidwa Mwauzimu  | 75  |
| <i>Suzyika Nymbili</i><br>Malo a sewero ngati njira yosungira zikumbukiro                            | 91  |
| <i>Klara Wojtkowska</i><br>Momwe ndinaphunzirira kupemphera  | 101 |
| <i>Karolina Bieniek, Urszula Markowska-Manista, Paulina Brelińska-Garszka</i><br>Luso ngati Kukumana | 124 |
| Mbiri ya Olemba  | 140 |



**Kulenga zinthu ndiye chidziwitso chomwe chimapezeka pampambano ya luso ndi sayansi, zomwe ife timazimvetisa ngati sitepe yolowera ku kuwerenga zomwe ndi zofanana: matanthauzo akale ndi atsopano.**

## **MAWU OYAMBA**

Pakusonkhanitsa pamodzi ojambula, akatswiri ndi ogwira ntchito kuchokera m'malo ndi mayiko osiyanasiyana (Slovakia, Hungary, Poland, Czechia, Uganda, Tanzania, ndi Zambia) omwe amafufuza mfundo zofanana ndi kulumikizana m'mbiri ya maiko osiyanasiyana, zikumbukiro, luso, sayansi ndi zolemba zapamwamba, tinali kufunafuna njira zatsopano zowonera zinthu zomwe zili pafupi ndi zomwe zili kutali. Tikuchita izi pamene tikufufuza dziko la Central ndi Eastern Europe (monga Czechia, Hungary, Poland, Slovakia) ndi South-Eastern Africa (monga Uganda, Tanzania, Zambia).

Kuti tipite limodzi paulendo wapakati pa maiko-ikowa, tinaitana ojambula omwe amadziwa bwino zinthu zomwe zili m'malire a kulingalira, kuchita zinthu, ndi kuwonetsa luso. Magulu kapena magawo awa akuphatikizapo: kuyandikira ndi kutalikirana—malo ndi malo—komanso nkhani ya nthawi—zakale, zamakono ndi zamtsogolo mkati ndi pakati pa South-East Africa ndi Central ndi Eastern Europe. Kukhala ndi chidwi pa kusiyana-siyana kwa maguluwa kumathandiza—kudzera mu luso—kumvetsetsa dziko ndi malire ake.

Zimatithandiza kupeza zomwe sizinapezedwe, nzeru zachibadwidwe zozama za m'madera mwathu ngati mlatho womvetsetsana. Nthawi yomweyo, zimapangitsa kuti tithe kumasulira zochitika za anthu, kuwonetsa kuthekera ndi tanthauzo la zinthu, kuwonetsa matanthauzo atsopano ndi mbali za miyambo kuno ndi uko, komanso "pakati". Chifukwa chake, kulenga ndi chidziwitso pampambano ya luso ndi sayansi, zomwe timazimvetisa ngati sitepe yolowera ku kuwerenga zomwe ndi zofanana, m'matanthauzo akale ndi atsopano.

M'zaka za m'ma 21st century, sizophweka kupinda kapena kusintha m'mene timaonera malo ndi nthawi (space-time) mwa fanizo, ndikupanga uthenga wa zolemba kukhala uthenga waluso womwe anthu osiyanasiyana angawumvetse, ndikuwulula phindu la zikhalidwe zosiyanasiyana. Luso ndi zolemba zimayendetsedwa ndi malamulo awoawo. Ndiye chifukwa chake tinaitana olemba omwe amadzimva kukhala pafupi ndi zikhalidwe izi ndipo amadzifotokoza okha m'mapulatifomu osiyanasiyana ndi atsopano, ndi njira zowonetsera.

Chiyambireni cha nthawi, ntchito ya luso yakhala kutulutsa zakukhosi kwa munthu, zokhumba, zolinga, mapulani, zisankho zovuta, maloto ndi maganizo



m'chilengedwe ndi chikhalidwe. Luso limasinthiratu ndi kumasula (decolonise) njira zowonera, kuganiza ndi kuchita zinthu. Pokhala injini ya kusintha, imathandizira kutenga nawo mbali ndi kudzuka kwa anthu pawokha ndi magulu.

Tonsefe—olemba komanso ife monga akonzi—tathira zomwe zimapanga dziko lathu lachezeredwe pamasamba ano. Kudzera munjira zomwe tasankha kufotokozero, tawonetsa zomwe dzikoli limatanthauza kwa ife popenda momwe timaganizira, ndi chifukwa chake timaganizira choncho, pamodzi ndi malingaliro, zikhulupiriro ndi zomwe timaganizira kale (prejudices).

Umu ndi momwe bukuli linapangidwira. Kutengera zikhulupiriro zomwe timagawana ndi zisankho za munthu aliyense pamutu, zomwe zili mkati ndi njira yofotokozero ya wolemba aliyense, zawulula momwe timaganizira, kumva ndi kulenga limodzi ngati opanga a m'deralo—nzika za dziko lapansi.

Msonkhanowu wa zolemba (anthology) ukuyembekeza kukulitsa kumvetsetsa kwathunthu ndi kuphunzira za kulumikizana ndi kutalikirana mukuwona, kuganiza ndi kufotokoza za maiko omwe ali pafupi ndi akutali, omwe malo awo amawulula kuthekera kwawo kwaukadaulo, sayansi, ndi zolemba. Tikufunafuna nkhani zapadera zomwe zimasokoneza malingaliro wamba, kumasula ku utsamunda (decolonise), ndi kubweretsa chidziwitso ndi machitidwe pafupi.

Tinaitana zolemba zotsatirazi: nkhani zaumwini (essays), nkhani zotsutsana ndi zomwe zimadziwika (zipeko ndi zowona), zikumbukiro (mbali ya dayale), zolemba zamaphunziro, ndi nthano zosimbidwanso. Bukuli lili ndi zolemba zisanu ndi zitatu. Chilichonse mwachiwo chiri ngati kachidutswa ka masewera olumikiza zithunzi (jigsaw puzzle). Mawu aliwonse ndi mawu a wolemba, yemwe, potenga nawo mbali munjira yapadera yofotokozero, waluka uthenga wapadera womwe ukugwirizana ndi mfundo za luso lopanda malire.

Zolembazi, zomwe zimasiyana pamapangidwe ndi mphamvu ya kalfotokozedwe, zinalembedwa ndi olemba ochokera m'magulu osiyanasiyana ndipo akuimira magawo osiyanasiyana a luso ndi sayansi. Olembawo ndi osiyanasiyana malinga ndi zokonda zawo zaluso ndi zochitika, zaka, zokhumba, malo omwe amachokera ndi malo omwe adalumikiza zolemba zawo.

Tikukhulupirira kuti msonkhanowu wa zolemba udzakhala wotheadiza kwa owerenga ochokera mbali zonse za dziko lapansi ngati mawu osiyanasiyana (polyphony) omwe amatilola kutanthauzira ndi kutanthauziranso kulumikizana ndi zizindikiro za tanthauzo pakati pa Central ndi Eastern Europe ndi South-Eastern Africa.



Kwa ife akonzi—kugwira ntchito pa zidutswa za msonkhanowu kwakhala gwero lofunika la chidziwitso cha zomwe sitinkazidziwa ndi chilimbikitso cha ntchito yamtsogolo yomwe tidzaphatikiza mizimu iwiri: luso ndi sayansi.

### **MAWU OYAMBA PA KAPANGIDWE NDI MITU YA BUKULI**

Msonkhanowu wolembedwa uli ndi magawo owonjezera a mitu yoperekedwa ndi olemba ochokera m'malo osiyanasiyana, a m'maiko osiyanasiyana a luso, chikhalidwe ndi sayansi, ndipo ali osiyanasiyana malinga ndi zokonda, zaka, zomwe akwaniritsa ndi zochitika.

Zolembazi zimayang'ana kwambiri nkhani zokhudzana ndi nkhani za olemba kutengera zochitika zawo ndi malingaliro awo. Ndikofunikira kutsindika kulemera kwa njira zofotokozerana ndi kuchuluka kwa magawo ofufuza omwe amapanga madera omwe ali ndi chidwi kwa munthu aliyense, komanso mitu yomwe ili kutali ndi yapafupi yomwe ili mbali ya maziko a msonkhanowu. Olemba apanga magulu awo apadera ndi masitaelo ofufuza, omwe amayang'ana pafupi ndi patali, kuyeza zenizeni zosiyanasiyana za Central ndi Eastern Europe ndi South-East Africa, ndikulowa mu nkhani yaukoloni wapadziko lonse ndi chilankhulo cha luso kapena chilankhulo cha sayansi. Zolembazi zimawulula mphamvu ndi kusowa kwa nkhani, zochitika ndi zinthu zomwe zafotokozedwa, komanso zochitika zosayembekezereka ndi phindu logawana malingaliro.

Mu zolemba zoyamba: *Bizarre Tropes* (Zizindikiro Zodabwitsa), Kamil Kawalec ali ndi zokambirana ndi Karolina Bieniek, mkulu wa bungwe la Art Transparent Foundation, za mgwirizano wapadziko lonse m'munda wa luso latsopano pakati pa mabungwe a European Union ndi Africa kutengera zochitika zomwe Karolina adapeza pamaulendo ake m'maiko ambiri a mu Africa. Amakambirana zovuta zokhudzana ndi malingaliro olakwika (stereotypes), kusintha kwa maparadimu (paradigms) ndi kusintha kwa chikhalidwe komwe Karolina wawona pazaka makumi awiri za kafukufuku wake. Amatchulanso zolemba za tsiku ndi tsiku (diaries) za Anna Szpakowska-Kujawska ndi zolemba za Ewa Szumańska, motero kutanthauziranso udindo wa mayi ngati woyenda ndi wojambula, nthawi ndi nthawi amakumbukira nkhani za mayiko a mu Africa kuchokera mbali ya amayi.

Pambuyo pake, Shilika Chisoko m'zolemba zake *Undoing the Knots of Place and Space* (Kumasula Mfundo za Malo ndi Mpata), amabweretsa zipeko za ku Zambia zatsopano mu maphunziro apamwamba mothandizidwa ndi chiphunzitsotso cha European post-colonial chazaka zapakati kuti akambirane. Njira yake ikuwonetsa mutu wa kuyandikira ndi kutalikirana monga momwe zasonyezedwera mu mutu wake woyenera. Kusankha kwake kwapadera kwa zolemba (references) pakupanga maziko a zolembazi kumapangitsa kusanthula kwake kukhala



kodabwitsa, kokakamiza ndi kwatsopano. Katswiri wa ku Slovenia Slavoj Žižek, Maria Pia Lara adaphunzira ku Berlin pomwe adabwera ndi lingaliro la "public spheres" ngati zongopeka za anthu, ndipo pamodzi ndi Ranka Primorac, yemwe ntchito yake imayang'ana ku Southern Africa, amabweretsedwa pafupi ndi zopeka zokhudza amayi kuchokera kwa olemba ngati Mubanga Kalimamukwento. Ntchito yake imatikumbutsa kuti zochitika za pambuyo pa utsamunda (post-colonial contexts) zimawonetsa machitidwe obwereza mosasamala kanthu za malo omwe ali.

Mu gawo lotsatira la msonkhanowu, Chiteu Kasongo akuluka kafukufuku wandakatulo wa kuyandikira ndi kutalikirana wotchedwa *Threads of Unity* (Ulusi wa Umodzi). Wolembayo akufotokoza ndakatulo zake ngati kukulitsa kumvetsetsa kwakuya kwa kulumikizana ndi mipata yomwe imapanga zochitika, malingaliro ndi nkhani mu malo a kuyandikira ndi kutalikirana. Chidutsa chilichonse cha ntchito yandakatuloyi chimalola kutulukira ndi kutanthauzira mu nkhani komanso kulingalira ndi kumira mu ndakatulo ya chidziwitso ndi machitidwe.

M'zolemba zake *Towards a Body-Conscious Knowledge* (Kupita ku Chidziwitso Chokhudza Thupi), Karolina Marcinkowska akuthana ndi nkhani zingapo zokhudzana ndi zovuta zochita kafukufuku ngati wofufuza wamkazi mu chikhalidwe chachilendo. Kusanthula kwake pamzere wa chidziwitso ndi zochitika kuchokera kumadera osiyanasiyana a Africa ndi Europe kumapereka poyambira kulingalira mitu monga zochitika zaumwini, kafukufuku ndi kukhudzidwa kwa malo pa wofufuza wamkazi. Nkhaniyi imatchulanso lingaliro la herstory (mbiri ya amayi) ngati maziko amalingaliro ake owunikira nkhani.

Zophunzitsa ndi zosangalatsa, nkhani ya Mwaka Siluonde yakuti *Spiritually Yoked* (Omangidwa Mwauzimu) imabweretsa zopeka zakale kukhala ndi moyo kudzera mu kuyandikira kwa omwe ali nkhaninyi ndi nkhani yozama. Tikutsatira nkhani ya Sister Mulenga, sisitere paulendo yemwe amatitenga mu zikumbukiro zake zozama mkati mwa zaka za m'ma 1970 moyang'anizana ndi chochitika cha mbiri yakale pa ngozi ya ku mgodi wa Roan ku Zambia. Ndi kulimba mtima kosagwedezeka, Siluonde akufufuza mwaluso mitu ya nkhanza za m'banja, kusamuka kuchoka kumudzi kupita kutawuni, mtundu (race) ndi magulu a anthu (class).

Mu mutu wake: *The place of theatre as a medium of memory* (Malo a sewero ngati njira yosungira zikumbukiro), Nyimbili Suzyika akugwiritsa ntchito mlingo wa Stuart Spencer pa kasimbidwe ka nkhani kuti afotokoze mphamvu ya sewero pa omvera, pamene akulungamitsa ubwino wapadera wa sewero pakubweretsa ndi kufunsa mafunso pa zikumbukiro. Wolembayo akuzindikira sewero ngati chida chofunikira kutanthauzira ndi kufufuza zikumbukiro. Potengera kusanthula



masewero awiri ochokera ku Hungary ndi Zambia, wolembayo akugawana zomwe wakumana nazo ndi kumvetsetsa kwake kwa kuyandikira kudzera mu diso la sewero.

Zopeka ndi mbiri ya moyo (memoir) zaphatikizidwa mu ntchito ya Klara Wojtkowska yakuti *How I Learned to Pray* (Momwe ndinaphunzirira kupemphera) yomwe ndi yokhudza mtima kwambiri ndiponso yotseguka poyera. Ya onse komanso yaumwini nthawi imodzi, ntchito ya Wojtkowska ndi nsalu yolukidwa modabwitsa ya zikumbukiro, zomwe zimalola kuyenda ngati nyimbo. Iye amafufuza mitu yovuta yamasiku ano monga kukhala mlendo, zauzimu ndi kukhala m'gulu ndi chikondi ndi kuzama. Yolukidwa mwaluso. Yokhudza mtima, yafika patali: Wojtkowska amatitenga paulendo ndi kudzionana momveka bwino ndi kuthwa kwa kuwona zinthu.

Mawu omaliza ndi a mawu a amayi osiyanasiyana omwe ali ndi mutu wakuti: *Art as an Encounter* (Luso ngati Kukumana) – *narrative paths of closure and opening to new* (njira zofotokozera zotsekera ndi kutsegulira zatsopano). Fomu yomwe yasankhidwa kufotokozera si mwangozi, popeza kuchuluka kwa nkhani kumalola kuwona mbali zambiri ndi kugwira magulu omwe ali amoyo pa mutu wa luso ndi chidziwitso ndi kufunikira kwawo pa chitukuko cha anthu ndi chilungamo cha anthu pamlingo wapadziko lonse. Ikumaliza bukuli pozindikira phindu la zoyesayesa zamaphunziro ndi zaluso ndi udindo wofunikira wa mphamvu za amayi m'njira zopangira ndi kupanganso chidziwitso chothandiza anthu.

Akonzi, Poland & Zambia,

December 2023



## ZA POLOJEKITI YA DECONFINING

Polojekiti ya DECONFINING ili ndi cholinga chopanga ubale wabwino ndi wachilungamo wa chikhalidwe pakati pa Europe ndi Africa popanga chitsanzo chokhazikika cha mgwirizano chomwe pambuyo pake chidzafalitsidwa kumadera ena a dziko lapansi. Pomangira pa mgwirizano wapamtima pakati pa makontinenti awiriwa ndi kuphatikizidwa kwa mapulogalamu awo a Capitals of Culture (Mizinda Ikuluikulu ya Chikhalidwe), polojekitiyi idzabweretsa pamodzi ochita zantchito zaluso, opanga ndondomeko, ojambula ndi ochita masewero, mayunivesite omwe ali m'munda wa ntchito ndi omvera kuchokera ku makontinenti onse awiri. Cholinga ndi kufufuza ndi kuwonetsa njira zatsopano za mgwirizano wa luso ndi chikhalidwe (ndi ndondomeko zake) pakati pa makontinenti, komanso kuthandizira kumvetsetsa bwino za kukhala otsekerezedwa (confinement patterns) kuchokera m'malo osiyanasiyana. Zonsezi zikuchitika n'cholinga chofuna kuthawa kapena kumasuka ku maganizo odziona ngati bwana ndi a utsamunda (paternalistic and colonial views) ndikulimbikitsa mzimu wamphamvu wotenga nawo mbali, ndikupereka mwayi wabwino ndi chidziwitso cha mayendedwe pakati pa makontinenti ndi kulenga zinthu limodzi pakati pa maiko.

Polojekitiyi idapangidwa ndipo imatsogoleredwa ndi othandizana nawo khumi ndi awiri kuchokera ku mayiko khumi ndi limodzi a ku Europe ndi dziko limodzi la ku Africa. Polojekitiyi idzakhala ndi misonkhano inayi ikuluikulu, timisonkhano tina tanayi tating'ono, pulatifomu yoyendera (mobility platform), zida za ndondomeko (policy toolkit), buku la pa intaneti (ebook) la zolemba za DECONFINING; ndi zojambulajambula zatsopano, kuphatikizapo ziwonetsero, mbali za podcast makumi awiri zowonetsa machitidwe aluso, maulendo khumi ndi awiri a zaluso, ndi nkhokwe yolemera ya digito yotseguka kwa onse.

Mgwirizano wa DECONFINING umapangidwa ndi opanga zantchito zachikhalidwe, mabungwe ofufuza, mabungwe a boma a zachikhalidwe ndi bungwe limodzi losagwirizana ndi boma (private NGO), kubweretsa pamodzi ndi kuthandizana ndi ukatswiri womwe wafotokozedwa mu polojekitiyi. Othandizana nawo pa polojekiti ndi mabungwe a Intercontinental Co-operation Organisations kuchokera ku Europe ndi Africa akugwira ntchito limodzi pa ntchitoyi.

Monga gawo la Work Package No. 4 la polojekiti ya DECONFINING, a Art Transparent (Poland) ndi a Pro Progressione (Hungary) akugwirizana ndi mabungwe ochokera ku Tanzania ndi Zambia. Cholinga chathu ndi kuyesa maubwenzi atsopano ndikupanga zochitika zaluso, zomwe bukuli ndi gawo lake.



**Momwe njira zathu zaku Central European zowonera East Africa zimasianirana ndi njira zaku Western zomwe zimalamulira nkhani zapa media.**

Kamil Kawalec, Karolina Bieniek

**ZIZINDIKIRO ZODABWITSA**

**Zizindikiro Zodabwitsa: Kukambirana ndi Karolina Bieniek, Mkulu wa Art Transparent Foundation**

**1. Kodi muli ndi zokumana nazo zotani pa nkhani ya mgwirizano waluso ndi Tanzania?**

Mwayi utangopezeka m'moyo wanga wantchito woti ndigwire ntchito padziko lonse lapansi ndi bungwe lohandizana nawo ku Africa, maganizo anga nthawi yomweyo anatembenukira ku Tanzania. Ndili ndi ubale wapadera ndi dzikoli. Kuyambira chaka cha 2005, ndakhala ndikuchita nawo zochitika zosiyanasiyana zachinsinsi ndi zantchito kumeneko. Kuthekera kwa mgwirizano wanthawi yayitali ndi kusinthana kwa chikhalidwe ndi luso loperekedwa ndi polojekiti ya zaka zinayi ya Deconfining kunkandilimbikitsa kuti ndifufuze bungwe lohandizana nawo lomwe lingathe kukwaniritsa zovuta za ntchito yaikulu ndi yovutayi. Zaka zambiri zakuchita ntchito kunja kwa Europe komanso kumakontinenti ena zandiphunzitsa kuti muzochitika zotere, ndi bwino kudalira zomwe anthu ena akunena ndi malingaliro ochokera kwa omwe amakufunirani zabwino komanso misonkhano ya maso ndi maso.

Mwamwayi, ndinali nditagwirapo ntchito m'dera la African Great Lakes, ndikuchita kafukufuku komanso kukhazikitsa ntchito zothandiza. Chifukwa chake, pankhani ya Deconfining, ndinadalira anthu omwe amadziwa bwino momwe zinthu zilili ku Dar es Salaam kuposa ine—omwe kale anali okhala mumzinda wachiwiri waukulu wa Tanzania. Chifukwa cha Helena Goldon, ndinaphunzira za Nafasi Art Space—bungwe labwino kwambiri la NGO lomwe mbiri yake (profile) ndi yofanana kwambiri ndi ya Art Transparent. Pamodzi ndi Rebecca Yeong Ae Corey ndi Lilian Hipolyte, tinakhala ndi misonkhano ingapo pa intaneti ndikukambirana zomwe zingatheke pa mgwirizano. Poyamba, sizinali zoonekeratu kuti ntchitoyi itimanga kwa zaka zambiri.



Dongosolo la mgwirizano ndi Zambia linali lofanana kwambiri. Ndinkadziwa kuti Karolina Łągiewka ankakhala ndikugwira ntchito kumeneko—tinali titagwirapo ntchito kale pokhazikitsa zochitika zothandizira zokhudzana ndi UNESCO World Book Capital Conakry 2017. Ndi Karolina amene anandidziwitsa kwa Samba Yonga ndi Natasha Omokhodion a ku Women’s History Museum ku Lusaka, omwe tikugwira nawo ntchito pa buku ngati gawo la polojekitiyi.

**2. Kodi mukuona bwanji momwe mgwirizanowu ukuyendera? Kodi mwakwanitsa kuchita zochulukwa bwanji ndipo ndi zochulukwa bwanji zomwe zikufunikabe kugwiridwa?**

Tinayamba kugwira ntchito pa polojekiti ya Deconfining ndi gulu lalikulu kwambiri la ma NGO ochokera kumakontinenti onse awiri. Inali mu June 2019 pamene, ngati gawo la mapulogalamu okonzekera European Capital of Culture Rijeka 2020, Sylvia Amann anatiitana ku msonkhano wa malingaliro a maukonde a European-African. Popeza ife monga Art Transparent tinali titachita kale zochitika m'derali, mwachitsanzo ngati gawo la UNESCO World Book Capital Conakry 2017 yomwe yatchulidwa kale, tinali ndi zifukwa zambiri zogawana zomwe takumana nazo.

Chotsatira chinali kukonzekera pempho (application) poyankha kuyitana kwa mapulojekiti akuluakulu ndi mgwirizano mkati mwa pulogalamu ya Creative Europe, yomwe inatengera mgwirizano wathu (consortium) miyezi yoposa isanu ndi umodzi. Pamapeto pake, tinapereka pempho lovutali mu 2021, ndipo tinali ndi mwayi wothe kuyamba kukhazikitsa polojekitiyi mu June 2022. Ndi ndondomeko yayitali kwambiri, koma pokhapokha mapangano onse atasainidwa ndipo gawo lovuta kwambiri la kayendetsedwe ka zinthu litatha m'pamene tinatha kupita ku gawo losangalatsa kwambiri la ntchitoyi, lomwe linali ndipo liri kukhazikitsa zolinga za mgwirizanowu.

Tsopano tili (pa nthawi ya kuyankhulana kumeneku) m'chaka choyamba cha mgwirizano wa zaka zinayi (2022–2026). Monga othandizana nawo pa polojekiti, tachita zopempha ziwiri zotseguka (open calls): imodzi ya zolembe zoti zifalitsidwe pamodzi ndi Women’s History Museum Zambia, ndi ina ya malo okhala (residencies) ku Poland ndi Tanzania. Zotsatira zake ndi zochititsa chidwi. Tikugwira ntchito ndi anthu ambiri osangalatsa kwambiri. Ndikuona kuti tikumanga milatho pakati pa mipata, kulumikiza mfundo pakati pa madera athu a dziko lapansi, ngakhale kuti tikadali pachiyambi cha ulendowu.



**3. Imodzi mwamagwero a chilimbikitso cha kafukufuku wanu ndi buku la Bizary lolembedwa ndi Ewa Szumańska. Kodi ubale wa mayiko a ku Africa ndi Europe wasintha bwanji kuchokera ku zomwe Szumańska amafotokoza?**

Ndinatengeka maganizo kapena "kuyambukiridwa" ndi zolembe za Ewa Szumańska pamene ndinkachita zochitika zingapo zokhudzana ndi Profesa Leon Podsiadły wa Academy of Art and Design ku Wrocław, yemwe anali atakhala zaka zisanu akugwira ntchito ngati mphunzitsi ku Conakry, Guinea. Profesa nthawi zonse anali pafupi ndi zoyeserera zathu ndipo, monga membala wa Gulu la Wrocław, nthawi zambiri ankachezera nyumba yosungiramo zojambulajambula ya Mieszkanie Gepperta yoyendetsedwa ndi Art Transparent.

Pakutsegulira ziwonetsero ndi misonkhano yambiri m'nyumba mwake ndi ku studio, anatiuza nkhani zochititsa chidwi za anthu olumikizidwa ndi Wrocław omwe anapereka gawo la miyoyo yawo ndi ntchito kumadera osiyanasiyana a Africa. Komabe, nkhani zomwe ndimakonda kwambiri zinali zokhudzana ndi zomwe adakumana nazo posiya zenizeni za Poland ya chikomyunizimu kupita ku Guinea-Conakry, yomwe inali pafupi kupezanso ufulu wake; ntchito yake pasukulu yakumaloko ya zaluso ndi ntchito zamanja, ubale wake ndi ophunzira a ku Guinea ndipo, potsiriza, kufufuza kwake kwa Polish-Guinean kwa likulu la Ufumu wa Mali.

Mu 2017, ndinakumana ndi buku lalikulu lofalitsidwa ndi nyumba yosindikiza ya ku Wrocław yotchedwa *Warstwy—Bizary* la Ewa Szumańska. Ndinkadziwa nkhani ya pulogalamu yailesi yotchuka ya "Studio 202" ndi mndandanda wa zaka zambiri wa Szumańska "From the Diary of a Young Doctor" (Kuchokera ku Dayale ya Dokotala Wachinyamata), koma ngakhale zinali choncho, sindinkadziwa nkomwe kuti iye anali woyamba komanso woyendayenda wodzipereka. Ndinachita chidwi ndi njira yake yowonera dziko, kuzindikira kwake ndi malingaliro ake achifundo pa Africa, omwe anali ofanana ndi a Podsiadły.

Kulingalira pa nkhani ziwirizi kunatsogolera ku funso la momwe madera awiri akutali a dziko lapansi, Central Europe ndi East Africa, amawonerana ndi kumvetsana. Funsoli likubwerezedwa m'mutu wa buku lomwe ndi gawo la polojekiti ya *Deconfining: Narratives of Closeness and Distance From Central-Eastern Europe and South-Eastern Africa – A Multicontextual Patchwork* (Nkhani za Kuyandikira ndi Kutalikirana zochokera ku Central-Eastern Europe ndi South-Eastern Africa – Nsalu Yolukidwa ndi Zikhalidwe Zosiyanasiyana), lomwe likukonedwa pansu pa utsoholeri wa Dr Urszula Markowska-Manista ndi Natasha Omokhodion.



#### **4. Kodi mukukumbukira nkhani iliyonse yomwe Profesa Podsiadły anakuuzani?**

Inde, ankalankhula kwambiri za m'ma 1960. Nkhani zake zinali zodzaza ndi anthu otchuka ochokera ku Wrocław, monga ochita masewero Zbyszek Cybulski ndi Feliks Podsiadły, mchimwene wake wa Leon. Tinalimba za iwo mu kabuku (catalogue) kofalitsidwa ndi Art Transparent pambuyo pa chiwonetsero cha *Bel Air* ku nyumba yosungiramo zojambulajambula ya Mieszkanie Gepperta [*Bel Air, Leon Podsiadły*, 2020, Wrocław]. Ndinachita chidwi kwambiri ndi nkhani ya kupangidwa kwa filimu ya Stanisław Lenartowicz yotchedwa Full Ahead. Wotsogolera filimuyo, mogwirizana ndi Ewa Szumańska, anajambula filimuyo paulendo wapamadzi pa sitima ya Poland kuchokera ku Szczecin, ndikuyima ku Canary Islands, Dakar ndi zilumba zozungulira Conakry, pakati pa ena.

Podsiadły analankhula za kulimba mtima kwa Zbigniew Cybulski wodziwika bwino ku Conakry ndi kukongola kwa Teresa Tuszyńska. Tisasiye kukumbukira kuti inali nthawi yomwe kupanga mafilimu m'malo akutali chonchi sikunali kophweka! Nkhani ina inali yokhudza mgwirizano wa asayansi a ku Poland ochokera ku Szczecin, Maprofesa Władysław Filipowiak ndi Bogusław Szerniewicz, ndi Profesa Djibril Tamsir Niane pokonzekera maulendo a ofukula zinthu zakale (archaeological expeditions) pofufuza likulu la Ufumu wa Mali (1962, 1964–65, 1967–68, 1973–74, 1978). M'maulendo amenewa, luso lojambula la mchimwene wake wa Leon, Feliks, linayamikiridwa makamaka ndi ofufuza. Ojambulawo anali ndi udindo wolembe ndi kusunga zinthu zakale (artefacts) zomwe zinapezeka panthawi yofukula. Mwa njira, Leon ndi mchimwene wake Feliks nthawi zina ankayenda kupita mkati mwa dziko ndi asayansi a ku Poland ndi Guinea, mwachitsanzo kuti akonzekere chiwonetsero ku Conakry choperekedwa ku zikhalidwe za ku Guinea.

Pali nkhani zambiri zotere. Mpaka lero, anthu okhala m'malo amenewa amakumbukira bwino aphunzitsi a ku Poland ndi Central Europe, aphunzitsi a payunivesite, okonza matauni ndi mainjiniya omwe, mu theka lachiwiri la zaka za m'ma 20, anachita mapulojekiti a maphunziro ndi malonda m'malo ambiri a Africa.

#### **5. Kodi mukuganiza kuti malingaliro athu amasiku ano pa ubale wa Africa ndi Europe ndi otani? Kodi tikadali ndi malingaliro olakwika ofanana (stereotypes) okhudza Africa kapena asintha?**



Ndikuganiza kuti malingaliro athu okhudza wina ndi mnzake akadali ozikidwa pa malingaliro olakwika, omwe mwamwayi ayamba kutsutsidwa. Komabe, ndikufuna kutsindika kuti kupanga malingaliro olakwika sikuli ku mbali ya Central Europe powona Africa pokha—kumagwira ntchito mbali zonse ziwiri. Mulimonsemo, ngati mukufuna kuyang'ana pa malingaliro olakwika, muyenera kudziwa kuti ndi zachilengedwe kwa munthu aliyense amene ayenera kukhala mwanjira ina m'dziko lovuta kwambiri.

Komabe, ndikufuna kukhulupirira kuti njira za kulumikizana kwa mayiko (globalisation) zikutipatsa mwayi wa kusintha kwakukulu, ndipo kuti luso lamakono likupanga mwayi womwe sunachitikepo wodziwana, kugwirizana mwachindunji, ndipo motero kutsutsana ndi malingaliro olakwika. Izi ndi zomwe mapulojekiti ngati Deconfining ali nazo. Mabuku, misonkhano, ntchito za mavidiyo, kusewera ndi potsiriza ma podcasts kapena zoyankhulana—zimapatsa omvera mwayi wowona madera omwe ali kutali kuchokera ku malingaliro angapo osiyanasiyana.

**6. Anna Szpakowska-Kujawska nayenso ankasunga dayale panthawi yomwe ankayenda ku Africa. Kodi tingaphunzire chiyani kuchokera ku zolemba zake?**

Pamene tinatsegula chiwonetsero cha Bel Air mu nyumba yathu yosungiramo zojambulajambula ya Mieszkanie Gepperta mu 2017, ndinapemphedwa ndi Mayi Anna Szpakowska-Kujawska, wojambula wabwino kwambiri wochokera ku Wrocław, yemwense anali membala wa Gulu la Wrocław, yemwe anati, monga Podsiadły, anali atakhala pafupifupi zaka zisanu ndi ziwiri za moyo wake ku West Africa. Anandiuza za buku lomwe analemba ndi kudzifalitsa yekha pambuyo pokhala kumeneko lotchedwa *Ekundayo czyli Droga* [Ekundayo kapena Njira], koma sanatchulepo za madayale ake oyenda.

Sizinali mpaka 2023, pamene chiwonetsero chake chinali kukonzedwa ku Mieszkanie Gepperta, pomwe adavomereza kuti akadali ndi madayale ake osasindikizidwa a kukhala kwake ku Nigeria ndi maulendo ake opita kumayiko oyandikana nawo. Pamene Anna anachezera ofesi ya Foundation tsiku lina, tinalandira kope la zolemba zochititsa chidwi izi, zodzaza ndi mafotokozedwe a Africa yomwe kulibenso, popeza yasintha kwambiri pazaka makumi asanu zapitazi. Chomwe ndinachipeza kukhala chokongola kwambiri mu nkhani ya Szpakowska-Kujawska chinali chidwi chake kwa anthu, makamaka amayi omwe adakumana nawo ku Nigeria, komanso chikhalidwe ndi luso la ku Nigeria. Mu voliyumu yachiwiri ya madayale, ndinakumananso ndi nkhani ya ulendo wake wopita ku Tanzania,



chidwi chake ndi dzikolo ndi ulendo wake wodabwitsa wopita kumunsi kwa phiri la Kilimanjaro.

Ndinaganiza za zizindikiro zonse za chikhalidwe zomwe zimadziwika kuchokera ku mabuku otchuka ndi sinema – kuyambira *A Farewell to Africa* ya Karen Blixen mpaka *The White Masai* ya Corinne Hofmann – zomwe ndizofala kwa ife ku Europe, kuphatikizapo Eastern Europe. Ndinayamba kudabwa za chidwi ichi ndi East Africa mkati mwa chikhalidwe cha ku Europe ndi kulandiridwa kwake mbali ina ya equator. Izi zinayambitsa funso la momwe njira zathu zaku Central European zowonera East Africa zimasiyanirana ndi njira zaku Western, zomwe zimalamulira nkhani zapa media.

**7. Nkhani za Szumańska kapena Szpakowska-Kujawska zikuwoneka kuti zikugwirizana mwachindunji ndi zomwe mwakumana nazo poyenda. Kodi mukuganiza kuti ndi chiyani chomwe chiyenera kuwunikiridwa apa?**

Koposa zonse, chomwe chimandigwira mtima ndichakuti tonse atatu ndife apaulendo ochokera ku Wrocław, kuchokera pantima wa Central Europe, omwe amapita kumalo omwe amawoneka osazolowerika ndipo timakonda kulankhula za iwo. Ndikufuna kuganiza kuti nkhani zathu ndi za dziko lapansi monga momwe timakumanirana nalo, mosiyana ndi momwe zilili masiku ano zolankhula za ife eni tikamayenda. Ndili ndi ulemu waukulu pa nkhani za amayi apaulendo, popeza amakonda kuwonetsa chidwi chosiyana kwambiri ndi nkhani za amuna-ogonjetsa (men-conquerors).

Potsiriza, ndimachita chidwi ndi mbiri ya Szumańska ndi Szpakowska-Kujawska—amayni omwe, panthawi yomwe kukhala ndi pasipoti ndi njira zoyendera kutali sizinali zophweka, adatha kuchita ntchito zovuta chotere. Ndikofunika kudziwa kuti, ngakhale tinkakonda maulendo akutali, tonsefe tinalumikiza miyoyo yathu yantchito ndi chikhalidwe ndi luso.

Chithunzi cha ulendo wa Szpakowska-Kujawska kupita ku mudzi wa polojekiti ya wojambula wa Austrian-Nigerian Susanne Wenger sichichoka m'maganizo mwanga. Chifukwa cha ntchito ya Wenger, dera lofunika kwambiri ku chikhalidwe cha Yoruba linapululumutsidwa. Kutenga nawo mbali kwake pa chikhalidwe ndi luso kunatsogolera ku chitetezo cha mahekitala makumi asanu ndi awiri mphambu asanu a nkhalango zopatulika ndi malo ang'onoang'ono opatulika operekedwa kwa milungu yakumaloko. Polojekiti yake inakhala moyo wake. Izi zisanachitike, sindinkadziwa



nkomwe kuti wina wochokera m'dera langa lapafupi adawona ntchito zaluso yodabwitsa iyi m'mudzi wa Yoruba.

China chomwe chiri chofunikira kwa ine ndi chidwi changa ndi momwe amayi amaonera dziko. Palibe amene amafotokoza amayi omwe amakumana nawo ngati olemba awiriwa. Nkhani za momwe ankakhalira ndi kukonda, nkhani zokhudza zolinga, tanthauzo ndi kupita, zandikhudza kwambiri. Kuwonjezera pamenepo, wothandizana naye mu polojekitiyi ndi Women's History Museum ku Lusaka. Tikudziwabe zochepa kwambiri za mayiko a ku Africa ndi herstories (mbiri ya amayi) ya ku Poland ndi Africa. Ndikukhulupirira kuti tikhoza kusintha zimenezo.

**8. Mukulankhula za nkhani zambiri zosangalatsa zolumikiza gawo lathu la Europe ndi mayiko osiyanasiyana a ku Africa. Pokonzekera polojekiti ya Deconfining, kodi munaganiziranso za kusiyana kulikonse kapena mikangano yomwe ingabuke panthawi yokhazikitsa?**

Ndikuganiza kuti tikungoyamba kumene kupeza zimenezo. Pulojekitiyi yalengedwa kuti tidziwane mwachitapo kanthu. Aliyense wowerenga pempho (application) lathu, lomwe linapambana ndalama kuchokera ku pulogalamu ya Creative Europe, adzakhala atazindikira kuti verebu (mawu ochita) "kuyesa" (test) ikubwerezedwa kwambiri. Zimenezi si mwangozi. Choyamba, ndikofunikira kuzindikira kuti mfundo yakuti sitikudziwa momwe tingathanirane ndi kusiyana komwe kungakhalepo chifukwa cha kusowa kwa chidziwitso chokwanira chokhudza wina ndi mnzake.

M'zikalata zovomerezeka, kusiyana kumeneku nthawi zonse kumaperekedwa monga mavuto kapena mikangano, osati monga kusiyana ndi mgwirizano. Chifukwa chake lingaliro loyandikira nkhani ya mgwirizano munjira ina, yomwe imabweretsa zovuta zambiri. Mwamwayi, kusalingana kumabuka ngakhale pofunsira ndalama, pamene zikuwoneka kuti mwa mayiko makumi asanu ndi atatu mphambu asanu ndi awiri (57) a ku Africa, awiri okha ndi omwe ali oyenera kutenga nawo mbali. Zotsatira zake, tinathera nthawi yochulukika tikuyesera kupanga chitsanzo cha polojekiti chomwe chingakwaniritse zofunikira za wopereka ndalama.

**9. Monga gawo la polojekiti ya Deconfining, Art Transparent Foundation mogwirizana ndi Nafasi Art Space asankha gulu la ojambula asanu ndi limodzi ochokera ku Europe ndi Africa omwe tidzakumana nawo pa kope la 22 la SURVIVAL Art Review ku Wroclaw. Kodi tingayembekezere mitu yanji m'ntchito zawo za mavidyo? Kodi ntchito**



**zawo ndi zokhudza kudziwika (identity), ndale, zachilengedwe (ecology)? Kodi malingaliro awa akuwonetsedwa bwanji?**

Pamene tikulankhula, gawo ili la polojekitiyi likudza. Tikudziwa mayina a ojambula omwe asankhidwa kudzera mu pempho lotseguka la malo okhala ku Poland ndi Tanzania. Bukuli lidzakhala mlangizi wawo. Ojambula asanu ndi limodzi awa ochokera ku East Africa ndi Central Europe adzapanga ntchito zatsopano za mavidiyo zomwe zimafufuza kulumikizana pakati pa mayiko omwe kale anali a chikomyunizimu (former communist bloc countries) ndi maboma a ku Africa a nthawi imeneyo, zomwe sizikuwonekera bwino kuchokera ku malingaliro amasiku ano.

Zizindikiro za kulumikizana kumeneku zingapezeke, mwachitsanzo, m'zipilala za zomangamanga zomwe zilipobe mpaka lero, monga ku Tanzania. Ena mwa ojambula adzayang'ana kusiyana ndi kufanana m'munda wa chikhalidwe—mwachitsanzo, m'ntchito zamanja kapena kuvina m'madera onse awiri a dziko lapansi. Ena adzayang'ana pa nkhani za anthu, monga ufulu wa amayi kapena thanzi ndi ukhondo.

Chifukwa chiyani tinasankha njira ya luso la kanema (video art)? Chifukwa chake nchakuti chimodzi mwa zopinga zofalitsira ntchito zaluso padziko lonse lapansi ndi mtengo wake waukulu. Podziwa kuti mayendedwe apadziko lonse lapansi a zinthu zaluso ndi njira yovuta kwambiri, tinaganiza ndi osunga (curators) kuti kuti polojekitiyi iyende bwino tichepetse njira yomwe tigwiritse ntchito. Tikukhulupirira kuti ntchito za mavidiyo zomwe zidzatuluke zidzatilola kuyang'anana ndi kudziwana bwino, koma koposa zonse—kuti zidzakhala zosavuta kupezeka kwa anthu onse.

**10. Zikuwoneka kwa ine kuti lingaliro la "wina" (the other) ponena za mayiko a ku Africa latha ntchito. Kodi tingalilowe m'malo ndi kulingalira momwe tingamangire "zofanana"?**

Nzosangalatsa kuti luso lochokera ku East Africa silikupozeka ku Poland, pamene nthawi yomweyo luso lochokera ku Central ndi Eastern Europe silikudziwika ndipo silikuwoneka ku Africa. Sitikudziwa zambiri za wina ndi mnzake, ngakhale kuti, monga mukuonera, tili ndi ubale wanthawi yayitali. Ndingatchule anthu ochepa chabe, zoyeserera zofunika kapena mapulojekiti omwe akufuna kusintha momwe zinthu zilili—ndipo tikukhala m'dziko lalikulu la ku Europe. Chifukwa chake cholinga cha polojekiti ngati Deconfining ndikufufuza malingaliro awiriwa.

Monga anzathu ochokera m'mizinda ina ya ku Europe (monga Bad Ischl [at], Bodo [n], Budapest [hu], Kaunas [lt] kapena Rijeka [hr]), tikugwira ntchito ndi anzathu a ku Tanzania ndi Zambia kuti tipwanye



nthano (myths) ndikumanga maubwenzi okhazikika pakati pa mabungwe athu achikhalidwe. Tikufuna kudziwa zokambirana za ku Africa zomwe zilipo panopa, choncho timakonza maulendo ophunzira amodzi ndi amodzi ndi misonkhano ya pa intaneti kuti tidziwe nkhani zomwe luso la masiku ano la ku Kenya, Tanzania ndi Rwanda likukamba. Kuchokera pamenepo timayesera kuthana ndi funso la kuyandikira ndi kutalikirana.

Pamene ndinayamba kuwuluka kupita ku East Africa mu 2005, si ambiri anali atamvapo za Poland, ndipo ngati wina aliyense ankatyanjanitsa ndi chilichonse, chinali ndi kugwa kwa chikomyunizimu ndi Lech Wałęsa. Chithunzi chimenecho chasintha pazaka zapitazi. Lero, m'mphepete mwa nyanja ya Zanzibar, chilankhulo cha Polish nchofala monga English kapena German.

Komabe, kodi tikudziwa chiyani za wina ndi mnzake? Ana m'masukulu a ku Poland amamva zambiri za Staś ndi Nel [otuluka m'mabuku opeka a ana a H. Sienkiewicz, In Desert and Wilderness] ndi Afryka Kazika [buku la Ł. Wierzbicki]—zozambulajambula zamabuku za kontinenti ya Africa kuyambira zaka zana limodzi kapena kuposerapo zapitazo—kuposa za mavuto enieni a kontinenti yachichepere kwambiri masiku ano, kumene opitilira theka la anthu biliyoni limodzi ali ndi zaka zosakwana khumi ndi zisanu ndi zitatu. Ndi kontinenti yomwe ili pachiwopsezo kwambiri cha kusintha kwa nyengo, ndipo komabe ikuwoneka kuti ndiyokhazikika komanso yosadabwitsa, mosiyana ndi malingaliro olakwika omwe alipo. Tikufuna kubwera ndi nkhani zopanda tsankho zomwe zingatibweretse pamodzi—kuno ku Central Europe ndi kumeneko ku East Africa.

#### **MNDANDANDA WA ZOLEMBA**

Szumańska, Ewa. Bizary. Warstwy, 2014.

Szpakowska-Kujawska, Anna. Ekundayu 1, ... albo droga. Journals. Selfpublishing.

Szpakowska-Kujawska, Anna. Ekundayu 2, ... albo droga. Journals. Selfpublishing.



Shilika Chisoko

### **KUMASULA MFUNDO ZA MALO NDI MPATA**

#### **Kufufuza zotheka zomwe zimabwera chifukwa cha zithunzi za chiwawa mu nkhani zopeka zazifupi za ku Zambia.**

Mbiriyakale, dziko la Zambia lakhala likusowa kupanga zolembe komanso kusanthula zolembe (literary criticism). Katswiri wa zolembe Ranka Primorac wanena kuti izi zimachitika chifukwa cha zomwe amazitcha "kulemba kwa nthawi yamavuto" (literariness of crisis), ndikunena kuti kuyambira pomwe dzikolo linayamba, "zikhalidwe zolembe zaku Zambia zakula m'mavuto osiyanasiyana." Izi zinapangitsa kuti dziko la Zambia likhale ndi mwambo wolembe womwe unasiyana ndi mndandanda wamabuku ambiri a mu Africa (African canon). Kuphatikiza apo, Leonard Chirwa akuti "makampani osindikiza mabuku ku Zambia amakhudzidwanso kwambiri ndi mitengo yokwera yosindikiza yomwe imapangitsa kuti mabuku omwe amapangidwa azikhala okwera mtengo kwambiri kwa munthu wamba wa ku Zambia."

Ngakhale pali zopinga izi, kwakhala kuwonjezeka kwa kupanga nkhani zopeka m'zaka zaposachedwa ndipo ndikulumikiza izi ndi kumasuka kufalitsa komwe digito media (apa intaneti) imapereka kwa olemba aku Zambia. Kuphatikiza pa izi, kwakhalanso kuwonjezeka kwa kutenga nawo mbali kwa olemba achikazi komanso chizolowezi chowonetsa miyoyo ya amayi mwanjira inayake. Poganizira mfundo zomwe tazitchulazi, nkhani yotsatirayi ikukhudza khalidwe lofanana lomwe likupezeka pakati pa gulu losankhidwa la nkhani zazifupi za ku Zambia zolembedwa ndi amayi masiku ano: "zosokoneza zachiwawa" (violent interruptions) zomwe zimawopseza miyoyo ya amayi omwe akuimiridwa m'nkhani zopekazo.

Nkhanizi ndi *A Hand to Hold* (2018) yolembedwa ndi Mali Kambandu, *All to Love* (2019) yolembedwa ndi Lydia Ngoma ndi *Thandiwe* (2022) yolembedwa ndi Mubanga Kalimamukwento. Pofuna kutsimikizira zimenezi, ndikubwereka mawu a Mbembe ndi Roitman akuti anthu okhala m'mayiko omwe kale anali pansu pa utsamunda (post-colony) amapanga "njira zolamulira momwe munthu amadzionera" (regimes of subjectivity) kuti athane ndi zotsatira za kukhala ndi mantha osatha a chiwawa chadzidzidzi.

Kuchokera pamenepa, mtsutso wanga ndi wakuti kuphulika kwa chiwawa kumeneku kukuwonetsa gulu la anthu lomwe ladziwika ndi chiwawa m'kati mwake. Ndikutsutsa kuti chiwawa choyambirira ichi ndi cha m'dongosolo (structural violence), pogwiritsa ntchito ntchito za akatswiri monga Slavoj Žižek ndi ena omwe amanena za kulimbikira kwa chiwawa chotere. Kupatula kuwulula malo atsopano



kwa olemba amasiku ano, digito media imapereka mwayi watsopano kwa otsutsa zolemba (literary critics) amasiku ano ngati ine. Ndikhoza kufikira nkhozwe zamaphunziro kuchokera padziko lonse lapansi. Mfundo yakuti ntchito ya Žižek ndi Primorac, akatswiri awiri a ku Eastern Europe, ndi maziko omwe ndikuchitira kusanthula kwanga, ikulankhula za mphamvu ya digito media.

Komanso, ndikupeza kuti ndizosangalatsa kuti ntchito yanga ikukwatitsa malingaliro ochokera ku Africa ndi Eastern Europe, zigawo ziwiri zomwe zakhala zosadziwika kwa nthawi yayitali chifukwa cha mbiri ya chiwawa ndi kugonjetsedwa. Mwa njira iyi, ndimawona digito media ngati ili ndi "mphamvu yomasula" (deconfining capacity)—kulola anthu kumasula mfundo za m'maganizo za malo ndi mpata (knots of place and space). Izi zimalimbikitsa kusinthana kwa chikhalidwe, kuwonetsera nkhani zomwe kale zinali zobisika ndi kukhazikitsa malo a munthu padziko lapansi.

Kuphatikiza apo, m'nkhanayi ndikuwonetsa zomwe zimapanga zosokoneza zachiwawa mu nkhani zopeka zosankhidwa. Ndiyerekeza *The Heart of a Woman* ndi nkhani zazifupi zosankhidwa kuti ndiwonetse kupita patsogolo kwa nkhani zazikulu mkati mwa nkhani zazifupi za ku Zambia zolembidwa ndi amayi. Kenako ndidzatsutsa kuti kusintha kumeneku (poyang'ana zochitika zachiwawa) kungathe kuimbidwa mlandu kapena kuperekedwa ku njira yomwe nkhani zopekazo zimafalitsidwira—mapulatifomu a digito media. Nkhanayi idzafufuzanso zomwe mawonekedwe a nkhani yafupi ndi pulatifomu yomwe nkhanizo zimafalitsidwira zimapereka.

Pomaliza, ndidzafufuza mphamvu yotsatizana ya kuyimira amayi mu zopeka zosankhidwa posintha malingaliro a anthu pa nkhani zosiyanasiyana za m'gulu. Potengera chitsanzo kuchokera ku ntchito ya Maria Pia Lara pa nkhani za ufulu wa amayi m'bwalo la anthu (public sphere), ndidzatsutsa kuti pongopereka nkhani za amayi ngati zopeka, nkhani zamakonozi zikufuna kuzindikira nkhani izi ndipo zili ndi mphamvu yochita ngati "mphamvu zokhudza anthu" (illocutionary forces). Pomaliza, ndikutsutsa kuti nkhani zazifupi si chabe nkhani zotsutsana ndi zomwe zimadziwika (counternarratives) koma zimagwira ntchito ngati magalimoto owonetsera chikhalidwe "choterera" (slippery nature) choyenda mu moyo wa ku Zambia ngati mkazi.

Pamene ndinkasonkhanitsa zida zomwe zingapange maziko amalingaliro (theoretical framework) a nkhanayi, ndinapanga chisankho chosadziwa chogwiritsa ntchito ntchito ya Žižek ndi Primorac. Woyamba chifukwa cha malingaliro omwe anaperekedwa kwa ine, ndipo wachiwiri chifukwa ntchito yake ndi ndemanga yosanthula yomwe imapezeka mosavuta pa zolemba za ku Zambia. Polingalira za mutu wa bukuli, ndimawona kuphatikiza kwanga kosakonzekera kwa Žižek ndi



Primorac ngati chizindikiro cha njira zomwe kusinthana kwa chikhalidwe kukuchitikira pakati pa Southern Africa ndi Eastern Europe. Ngakhale sindingathe kunena kuti kusinthanaku n'kofala, chilengedwe chomwe ndinakumana nawo akatswiriwa ndi momwe maphunziro awo 'amakwanirira' bwino mtsutso wanga zikuwonetsa kufanana kwakukulu kuposa kusiyana pakati pa Southern Africa ndi Eastern Europe. Chifukwa chake, ndikuyamba kusanthula kwanga ndi lingaliro lakuti zikutumikiranso ngati kufufuza momwe zolembe kuchokera ku Southern Africa ndi Eastern Europe zingawerengedwere limodzi.

Kutchulidwa kwa mawu akuti 'chiwawa' kumabweretsa chithunzi cha kumenyedwa kwa thupi ndi munthu mmodzi kapena angapo kwa wina (kapena ena). Judith Butler akuwona kuti "chithunzi cha nkhonya chakonza mwakachetechete mikangano yayikulu pa nkhani ya chiwawa, kusonyeza kuti chiwawa ndi chinthu chomwe chimachitika pakati pa magulu awiri pokumana mwaukali." Ngakhale zili choncho, Butler amavomereza chikhalidwe choletsa cha maguluwa, ndikutchula momwe chiwawa chimagwirira ntchito panso pa dongosolo la anthu amasiku ano. Iye amatsutsa kuti "popanda kutsutsa chiwawa cha nkhonya yeniyeni, tikhoza kulimbikira kuti mapangidwe a anthu kapena machitidwe, kuphatikizapo tsankho la m'dongosolo (systemic racism), ndiachiwawa." Mofananamo, Slavoj Žižek amachenjeza za kuyesedwa kofuna kumasulira chiwawa ngati chinthu chokhacho chomwe chimawoneka. Iye akutsindika kuti ndikofunikira "kuzindikira mizere ya maziko omwe amatulutsa kuphulika koteroko. Kubwerera m'mbuyo kumatithandiza kuzindikira chiwawa chomwe chimachirikiza kuyesetsa kwathu kulimbana ndi chiwawa ndikulimbikitsa kulolerana." Kugwiritsa ntchito kwa Žižek mawu akuti "kuphulika" (outbursts) n'kofunika kwambiri, popeza kukuwonetsa kukhalapo kwa dongosolo la chiwawa lomwe linalipo kale lomwe limapangitsa kuphulika kumeneku kukhala kotheka.

"Zosokoneza zachiwawa" (Violent interruptions) ndi mawu omwe amagwiritsidwa ntchito ndi Ranka Primorac kufotokoza kusiyana kwa nkhani zovuta zokhudzana ndi "amakono a pambuyo pa utsamunda" (monga HIV/AIDS, kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha, matenda a maganizo ndi ufiti) zowonetsedwa mu msonkhano wa nkhani zopeka zazifupi za ku Zambia zotchedwa *The Heart of a Woman*, ndi mphamvu yawo yoyambitsa chipwirikiti m'miyoyo ya anthu a m'nkhaniyo tsiku ndi tsiku. Zimachitika m'malo osiyanasiyana m'nkhani zazifupi zosankhidwa. Mwachitsanzo, "Ndikhoza kumutchula chilichonse chomwe ndikufuna (whatever the fuck I want)," akutero Misozi mokwiya poyankha mlongo wake yemwe amamuwunika. Kutsutsaku sikungochitika chifukwa cha kukwiya kwa Misozi poyenda kuchoka ku America kupita ku Zambia kusamalira amayi ake omwe akudwala. M'malo mwake, kukuwonetsa kuwawidwa mtima kwakukulu kwa Misozi kwa amayi ake ndi zovuta za ubale wawo.



Thandiwe ya Mubanga Kalimamukwento ndi nkhani yomwe imafotokoza za kubwerera ku Zambia kuchokera ku diaspora kwa mayi wotchedwa Misozi kusamalira amayi ake omwe akudwala. Nkhaniyi ili ndi nkhani zosiyanasiyana, kuyambira kudziona ngati munthu wapadziko lonse mpaka "msonkho wakuda" (black tax). Komabe, chidwi chachikulu mu nkhaniyi ndi momwe zochitika izi zimachitikira. Polamulidwa ndi mlongo wake, Misozi amakakamizika kubwerera kunyumba. Kubwerera kumeneku kuli pawiri: mwathupi, m'lingaliro lakuti ayenera kusiya nyumba yake ku diasporakupita ku Zambia, ndi m'maganizo, m'mene amakakamizika kubwereza zoopsa (trauma) zomwe adakumana nazo ali mwana. Misozi sakusangalala, ayenera kuyimitsa moyo wake ku USA chifukwa cha amayi ake omwe akudwala, kumukakamiza kuthana ndi vuto lake nthawi yomweyo.

Mofanana ndi Misozi, Kunda akukumbutsidwa za chikhalidwe cha chipwirikiti cha ubale wake ndi amayi ake mu *A Hand to Hold*. Mfundo zazikulu za nkhani ya Mali Kambandu ya 2018 ndi msonkhano wokhudza zokonzekera ukwati wa Kunda ndi zochitika zisanachitike ndi pambuyo pake. Apa, kapangidwe ka nkhaniyi kamathandizira kukulitsa zochitika zomwe 'zimasokoneza' moyo wa Kunda. Nkhaniyi imayamba ndi mafotokozedwe omveka bwino a zochitika ku komboni ya Ngombe ku Lusaka, yomwe imachepera ku chithunzi cha mayi wofooka komanso wowoneka ngati akudwala akupuma pa bedi.

Pamene chithunzi cha mayiyo chikungoyamba kuwoneka, amasiyidwa mofulumira, ndipo nkhaniyi imasintha kupita kwa Kunda akuyendetsa galimoto kudutsa mu komboni. Kachiwiri, zochitikazo zimasintha, ndipo Kunda amapita ku chipinda chochezera cha amayi ake. Atazunguliridwa ndi amayi osiyanasiyana, Kunda "amayang'ana patebulo ndipo sakumbukira mphindi imodzi yosangalatsa ndi amayi awa omwe akuthandiza amayi ake kukonzekera mphindi zosangalatsa kwambiri pamoyo wake." Zowululidwa pambuyo pake m'nkhaniyi zikuwonetsa kuti Kunda ali ndi ubale wotalikirana ndi amayi ake ndipo m'malo mwake ali pafupi ndi wantchito wawo wakale, Reeda Mwale. Kuchokera ku machitidwe a Kunda ndi magulu onse awiri, zikuwonekeratu kuti sali womasuka ndi woyambayo ndipo amakonda kukhala ndi womalizayo. Komabe, Maggie amauza Kunda kuti sayenera kuyanjana ndi mayi yemwe amamupatsa chithonhozo chifukwa chosowa ubale wamagazi. Kumvetsetsa kumeneku kumakakamiza Kunda kuthana ndi malingaliro oipa omwe ali mkati mwake ndipo mosakayikira izi zimapanga zosokoneza zachiwawa.

*All to Love* yolembedwa ndi Lydia Ngoma imaperekedwa kuchokera ku malingaliro a anthu atatu: alongo Enala ndi Judy pamodzi ndi mwana wamkazi wa Judy, Chola. Magawo awo amapereka mayankho ku kufika kwa Enala kunyumba kwa Judy ku Lusaka kuchokera ku tawuni ya ku Zambia yotchedwa Chinsali. Enala akuwoneka kuti sakumva bwino, atayenda ulendo wopita ku Lusaka kukalandira



chithandizo chamankhwala. Kukambirana pakati pa alongo awiriwa kukuwonetsa kuti Enala ali ndi kachilombo ka HIV, ndipo mbali zina za nkhaniyi zikutsimikizira kuti mwamuna wa Enala, Onesmus, amamuzunza. Komabe, mwamuna wake amapita ku Lusaka kukamutenga, kumuopseza ndi chisudzulo ngati akhala kutali ndi nyumba yawo nthawi yayitali. Onesmus amauza Enala kuti, “Sindikukakamiza kutiubwerere... koma usadabwe pamene udzasinthidwa.” Kufika kwadzidzidzi kwa Enala ndi zotsatira zake zimapanga zosokoneza zachiwawa, kukakamiza munthu aliyense kuthana ndi momwe zinthu zilili.

Primorac akuwona kuti *The Heart of a Woman* imapanga lingaliro la “mzinda” (cityness) logwirizana ndi njira yodziwonera yomwe imalola anthu kuzemba kapena kuthana ndi izi, ndiko kuti, “khalidwe” m'malo mwa kudziwika kokhazikika kapena mbali ina ya malo. Zoonadi, zomwezo zinganenedwe pa nkhani zazifupi zosankhidwa. Anthu m'nkhani izi amakhala m'malo osiyanasiyana (Zambia yakumudzi, Lusaka, USA, ndi zina zotero). Komabe, kuthekera kwawo kuthana ndi zopinga zawo kumatanthauza mkhalidwe wamaganizo—m'malo mwa mayankho okhudzana ndi malo ndi chikhalidwe. Mwachitsanzo, Enala akuganiza zobwerera kwa mwamuna wake ndi banja lake, nati “adzipereka zonse ku chikondi” (giving it all to love). Amanyalanyaza kufunikira kwake kwa chisamaliro chamankhwala choyenera ndipo m'malo mwake amachita gawo lake lokonzedweratu ndi anthu.

M'nkhani iliyonse mwa nkhani zazifupi, anthuwo amadzilimbitsa okha chifukwa cha zovuta zomwe zili patsogolo. Misozi amakana kuchita nawo zotheka zomwe zimabwera chifukwa cha chidziwitso chomwe amachipeza pazokambirana zosakhazikika ndi amayi ake, monga momwe akuwonetsera pamene akunena kuti, “ine? Ndikuti, fuck chifundo; ndimanyamula chikwama changa ndikutulukira padzuwa lomwe likudikirira.” Kutuluka kuchokera ku khalidwe losinthika lowonetsedwa ndi anthuwa ndiko kusonyeza gulu la anthu lomwe ladzaza ndi chiwawa, lomwe nthawi zonse limawopseza kusokoneza mkhalidwe wa munthuyo.

Kulumikiza mitima ndi miyoyo, kupanga zibwenzi zomwe zidakula.  
Mu msonkhanowu, lolani mawu athu asakanikirane ndi kugwirizana,  
Kupanga chigamba cha zikhalidwe zambiri, chosambitsidwa mu kuwala kwa ndakatulo.

Choncho, okonedwa olemba ndakatulo, pitirizani kulola kulenga kwanu kuyende,  
Kupaka zithunzi zomveka bwino ndi mawu omwe amawala.  
Kudzera m'mavesi anu, kumvetsetsa kungabuke,  
Ndi kutibweretsa pafupi, kumene chikondi ndi chifundo zili.

Pitirizani kufufuza, kukankha malire ndi kuwuluka,  
Tulutsani kulingalira kwanu, lolani mawu anu abangule.  
Pakuti mu ndakatulo yanu, muli mphamvu yolimbikitsa,  
Kuyatsa kusintha, kuyatsa dziko moto.

Pitirizani, okonedwa olemba ndakatulo, ndi zolemba zanu zitakwezedwa mmwamba,  
Pakuti mawu anu ali ndi kuthekera kukhudza thambo.  
Mu ulendo wa pakati pa makontinenti uwu, lolani mawu anu amveke,  
Pamene tikukondwerera kukongola kwa mawu aliwonse.

Pitirizani kulemba, kulota, kulenga,  
Kupanga dziko kumene mgwirizano ukuyembekezera.  
Pakuti ndakatulo ili ndi mphamvu yochiritsa ndi kusintha,  
Kugwirizanitsa magawano ndi kupirira mkuntho uliwonse.

Choncho, okonedwa olemba ndakatulo, lolani mawu anu akwere,  
Mu msonkhanowu, lolani mizimu yanu igwirizane.  
Pakuti m'nkhani za kuyandikira ndi kutalikirana zomwe timagawana,  
Tikupeza mphamvu ya ndakatulo, yosayerekezeka.

Pitirizani, ndipo lolani mawu anu avine pa tsamba,  
Mu nsalu ya pakati pa makontinenti iyi, tikuchita nawo.  
Pakuti mu mgwirizano wa zikhalidwe ndi mitima yolumikizana,  
Timapeza maziko a umunthu, ofotokozedwa bwino.



Pitirizani, okonedwa olemba ndakatulo, ndi chilakolako ndi changu,  
Kulandira mphamvu ya kukopa kwa ndakatulo.  
Pakuti m'mawu anu, dziko limapeza chithonhozo ndi mtendere,  
Pamene tikuyenda limodzi, miyoyo yandakatulo yomasulidwa.

Kuchokera ku zigwa za Uganda kupita ku thambo la golide la Tanzania,  
Ulendo wa umodzi, kumene tsogolo limauka,  
Mzimu wa South-Eastern Africa, chisomo cha Central Europe,  
Pamodzi amapanga utopia mu danga.

Atsogoleri ndi mafano akuwuka, kupitilira kugawikana,  
Manja otsogolera a nzeru, akuyenda mbali ndi mbali,  
M'dera la pakati pa makontinenti ili, amagwirizana,  
Kumenyera kusintha, kuphwanya malire ndi mphamvu.

Kutanthauziranso malingaliro, dziko latsopano loti lifufuzidwe,  
Kuyandikira ndi kutalikirana zikusowa, zowona kubwezeretsedwa,  
Mu kukumbatira kwa Central-Eastern Europe ndi kutentha kwa Africa,  
Nkhani zogawana za chiyembekezo, nyimbo ya kubadwanso.

Malire amakhala milatho, nkhani zosafotokozedwa zikuwululidwa,  
Zochitika zolembedwa mu kugunda kwa mtima, zikumbukiro za golide,  
Zakale, zamakono, ndi zamtsogolo zikulumikizana ndi chisomo,  
Pamene kuvina kwamuyaya kwa nthawi kumatenga malo ake.

Mu 'pakati', kumene zikhalidwe zimakumana ndi kusakanikirana,  
Miyeso yatsopano ya miyambo imatuluka, kupitilira mapeto,  
Tanthauzo limaphuka, mu mpweya uliwonse wopatulika,  
Kuwulula maziko a moyo, kupitilira moyo ndi imfa.

Chidziwitso chachibadwidwe chimanong'oneza, zinsinsi za dziko lapansi,  
Nzeru zobisika zimamanga milatho pakati pa mipata, dzanja m'dzanja,  
Kuchokera ku luso kupita ku sayansi, njira yomwe amalumikizana,  
Pamawonekedwe a chowonadi, kumvetsetsa kumawala.

Nyimbo yolemekeza kulumikizana, ku kukumbatira kwa umodzi,  
Chisomo cha Central-Eastern Europe ndi Africa,  
Ulusi wa umodzi, wolukidwa mwamphamvu ndi woona,  
Mu ulendo wa pakati pa makontinenti uwu, mizimu yathu imakonzedwanso.



Choncho, tiyeni tifufuze zapafupi ndi zakutali, popanda kugawikana,  
Omangidwa ndi maloto ogawana, kudutsa makontinenti otakata,  
Ndi mitima yotseguka, timapeza malo athu wamba,  
Mu kulumikizana, chuma chenicheni chimapezeka.

M'dziko lolukidwa ndi kulimba mtima ndi mphamvu,  
Mafano akuwuka, kuonya kuwala kwawo kowala,  
Kudutsa malire ndi zikhalidwe, chikoka chawo chimayenda,  
Kutitsogolera njira zathu, kulikonse kumene moyo umapita.

Władysław Reymont, mawu ake ndi mphatso,  
Cholemba cha wopambana Nobel, mizimu imakwezedwa,  
Kuchokera pantima pa Poland, nkhani zake zimawululidwa,  
Kulemeretsa miyoyo yathu, ngati ngale zamtengo wapatali.

Kuchokera pantima pa Uganda, ulamuliro wa Idi Amin,  
Phunziro la mbiri yakale, nkhani ya zowawa,  
Komabe pakati pa mdima, ena adadzuka,  
Mawu achilungamo, kumene chifundo chimawala.

Mu kukumbatira kwa Tanzania, Nyerere adayimirira motalika,  
Nyali ya umodzi, kuyankha kuitana,  
Nzeru zake ndi masomphenya, wotsogolera wa fuko,  
Kutsogolera ndi chisomo, mbali ndi mbali.

Václav Havel, kuchokera ku dziko la Czechia,  
Wolemba masewero ndi pulezidenti, adatenga malo,  
Kaamba ka ufulu ndi chowonadi, mawu ake adamveka,  
Chizindikiro cha kulimba mtima, chotchuka kwamuyaya.

Cholowa cha Hungary, nyimbo ya Bartók,  
Zolemba zomwe zimamanga milatho ya zikhalidwe ndi mgwirizano,  
Nyimbo zake zimapitilira, kukumbatira zonse,  
Nyimbo yolemekeza umodzi, kupitilira khoma.

Mphatso ya Slovakia, Milan Rastislav Štefánik,  
Katswiri wa zakuthambo, woyendetsa ndege, maloto okongola,  
Iye anafikira nyenyezi, kutsutsana ndi thambo,  
Mzimu wamasomphenya womwe sufa.

Kuchokera ku Zambia, Sylvia Masebo akuwala,



Mtsogoleri yemwe chifukwa cha chilungamo amagwirizana mwamphamvu,  
Kuyimirira kwake kukulira kwa chitetezo,  
Woyang'anira chilengedwe, kuti onse awone.

Mafano awa, osiyanasiyana koma olumikizana,  
M'nkhani zawo, umodzi timapeza,  
Kuchokera kumayiko osiyanasiyana, mizimu yawo imagwirizana,  
Kutitsogolera kutsogolo, ndi nzeru zogawana.

Mu nyimbo ya moyo, kumene zikhalidwe zimakumana,  
Oimba, olemba ndakatulo, ojambula amalumikizana,  
Kuchokera kumayiko osiyanasiyana, mawu awo amakwera,  
Mu mgwirizano ndi kulenga, amafufuza.

Mphatso ya Slovakia, nyimbo ya Eugen Suchoň,  
Mtima wa wolemba nyimbo, kupanga luso lapamwamba,  
Zolemba zake zimamveka ndi mzimu wa Slovak,  
Kulumikizana kosatha, kutipanga kukhala athunthu.

Kuchokera pamtima pa Hungary, cholemba cha Attila József,  
Mavesi a wolemba ndakatulo, ulendo wamkati,  
Mawu ake amadutsa malingaliro ozama,  
Kukhudza mitima, zinsinsi zomwe amasunga.

Chinsalu cha Poland, mtundu wa Tamara de Lempicka,  
Masomphenya a wojambula, matanthauzidwe atsopano,  
Mikwingwirima yake imawulula nkhani, zowala ndi zolimba mtima,  
Cholowa cha luso chomwe chimanenedwa kwamuyaya.

Mu kukumbatira kwa Czechia, nthabwala za Jaroslav Hašek,  
Nthabwala za wolemba, dziko loti liperekedwe,  
Kudzera mu luso la nthabwala la The Good Soldier Švejk,  
Iye amawonetsa zopusa za anthu mwachisamaliro.

Nyimbo za Uganda, nyimbo ya Philly Lutaaya,  
Mawu a woimba, kuyimirira mwamphamvu,  
Nyimbo zake zimalankhula za chikondi ndi nkondo,  
Kulimbikitsa mitima, kuyatsa kuwala.

Kuchokera ku mzimu wa Tanzania, Godfrey Mwampembwa,  
Nthabwala za katswiri wazojambula, kutipangitsa kujambula,



Nthabwala zake zikuwulula zowona zosafotokozedwa,  
Kuputa malingaliro, kuphwanya nkhungu.

Chilimbikitso cha Zambia, Mulenga Kapwepwe,  
Kukhudza kwa wojambula, kulenga mwaufulu,  
Kuwonetsa kwake kumafotokoza nkhani zosalamulirika,  
Kupatsa mphamvu mawu, kusiya mitima ili yoyaka.

Ojambula awa, olemba ndakatulo, oimba achisomo,  
Mu luso lawo, maiko osiyanasiyana amawakumbatira,  
Kuchokera kumakona osiyanasiyana, amakumana,  
Zolengedwa zawo ndi umboni wa chilakolako chathu chogawana.

Mu nyimbo zolukidwa kuchokera ku mtima kupita ku mtima,  
Oimba, olemba ndakatulo, ndi ojambula amapereka,  
Kuchokera ku kukumbatira kwa Slovakia, burashi ya Čiurlionis,  
Mitundu ya mzimu, malingaliro akuthamanga.

Mu dera la Hungary, score ya Bartók,  
Ulendo wanyimbo, kwamuyaya,  
Zolemba zake zimamveka, kudutsa dzikolo,  
Kugwirizanitsa dziko lapansi, ndi dzanja la mphantso.

Kuchokera pansu pa Poland, chisomo cha Chopin,  
Makiyi a piyano akuvina, kukumbatira kosatha,  
Zolemba zake zimalankhula, popanda mawu,  
Chilankhulo chapadziko lonse lapansi chikumveka modekha.  
Chuma cha Czechia, luso la Mucha,  
Kukongola ndi chisomo, iye amapereka,  
Mapangidwe ake ovuta, chisangalalo chowoneka,  
Mlatho wa chikhalidwe, mu usiku wa nyenyezi.

Wofotokoza nkhani wa Uganda, cholemba cha Okot p'Bitek,  
Mawu a miyambo, mobwerezabwereza,  
Mavesi ake akubwereza, nthano za makolo,  
Kulumikiza mitima, kwamuyaya.

Mu kukumbatira kwa Tanzania, nyimbo ya Liyongo,  
Kusunga zakale, kudzera mu mlengalenga ndi nthawi,  
Mawu ake amanyamula nzeru, kuchokera masiku akale,  
Kutitsogolera kutsogolo, munjira zambiri.



Kuchokera ku mzimu wa Zambia, chisomo cha Kapwepwe,  
Wolembe masewero, mtsogoleri, kukumbatira chikhalidwe,  
Mawu ake ndi masomphenya, cholowa chachikulu,  
Kugwirizanitsa anthu, kudutsa dzikolo.

Ojambula awa, olemba ndakatulo, oimba owala kwambiri,  
Wunikirani dziko lathu ndi kuwala kolenga,  
Kuchokera kumayiko osiyanasiyana, mawu awo amalumikizana,  
Mu nsalu ya luso, umodzi umawala.

Mu kusiyana kwa kukumbatira kwa chilengedwe,  
Malo a cholowa amayimirira ndi chisomo chakale,  
Kuchokera ku nsonga za High Tatras za Slovakia zokwera kwambiri,  
Kupita ku Serengeti ya Tanzania kumene nyama zakuthengo zimayendayenda  
kuthambo.

Hortobágy ya Hungary, zigwa zazikulu, zotseguka,  
Kumene crane zimavina ndi nkhani za moyo zimatsalira,  
Český Krumlov ya Czechia, tawuni ya nthano,  
Yolumikizidwa ndi mbiri yakale, kumene maloto amafesedwa.

Nkhalango ya Białowieża ya Poland, chuma chamoyo,  
Nyumba ya njati (bison), mu mgwirizano ndi zosangalatsa,  
Mapiri a Rwenzori a Uganda amakhudza thambo,  
Malo aumulungu kumene nsonga zimakwera mmwamba kwambiri.

Pakati pa chuma cha Zambia, Victoria Falls imayimirira,  
Luso la chilengedwe, chilengedwe chopangidwa ndi manja,  
Mafuko kudutsa malire, ndi nkhani zogawana,  
Nzeru zawo zakale, mu mpweya.

Kuchokera ku Tatras za Slovakia kupita ku mathithi a Zambia,  
Mafuko amakhala mkati mwa makoma a chilengedwe,  
Zikhalidwe zawo, miyambo, nthano za makolo,  
Zolumikizana, kwamuyaya.

Mu zigwa za Hungary ndi Serengeti ya Tanzania,  
Mafuko amapitilira, ndi mphamvu ndi umodzi,  
Matauni a Czechia ndi mapiri a Uganda,  
Cholowa cha mafuko chimayenda ngati akasupe osatha.



Kuchokera ku nkhalango za Poland kupita ku thambo la Zambia,  
Mawu a mafuko akumveka, maubwenzi akale,  
Nsalu zolukidwa za cholowa chachikulu,  
Kulumikizana kogawana, kudutsa dzikolo.



Karolina Marcinkowska

## KUPITA KU CHIDZIWITSO CHOKHUDZA THUPI

### Mbiri ya amayi (herstories) yochokera ku Poland ndi Rwanda

Ndidzayamba kuthira maganizo anga (okopeka kwambiri ndi ndakatulo komanso kalembedwe ka nkhani yaumwini m'malo mwa kukhwima kwa mapepala a maphunziro) ndi ndemanga yotsatirayi: mosasamala kanthu za chikhalidwe chomwe tili nacho, nthawi zonse timakhala omangidwa ndipo mwanjira ina oponderezedwa ndi kawonedwe kathu kozikidwa pa chikhalidwe. Kumasula maganizo athu (*decolonising our minds*) mwa kuwamasula ndikuyesera kupeza anthu osiyanasiyana, nkhani, ndi malo oyandikira, nthawi zonse kudzafuna kuti tigwiritse ntchito chilankhulo chathu, chinthu chomwe chili cholengedwa mwamphamvu ndi chikhalidwe, chozikidwa pa zikhulupiriro zathu, njira zofotokozera dziko monga momwe timatanthauzirira, zomwe zili zochepa malinga ndi chidziwitso chathu, mbiri yaumwini, ndi kumvetsetsa.

Zofunika zanga zazikulu pakufufuza ndi kulemba ndikukhala wodziwa za kupadera kwa chikhalidwe chilichonse ndi munthu aliyense wozama mmenemo. Ndikuchita izi mwaulemu ndi kudzichepetsa. Sindingayerekeze kudziticha ndekha "katswiri" pamutu winawake, chikhalidwe, kapena gawo la maphunziro, chifukwa choti ndinayesa kupeza njira yanga yofufuzira ndikufotokozera nkhani yosankhidwa. Ndiye chifukwa chake ndingakonde kuwerenga zolemba zomwe zimafotokoza poyera khalidwe la mwayi la zisankho zathu, msewu wozungulira wochititsa chidwi wa zochitika zaumwini ndi zochitika mwamwayi. Poyang'ana miyeso yatsopano ya "kuwerenga" ndi kulemba zochitika za anthu, ndimapitiriza kuyesa kupitilira njira zodziwika bwino zasayansi, za anthropology ndi magulu, posankha njira yozama yaumwini, e yomwe ingakhudze madera a ndakatulo, malingaliro obisika ndi osanenedwa (*tacit feelings*), malingaliro ongobwera ndi zolimbikitsa zomasuka.

Pofunafuna njira zatsopano zowonera chikhalidwe changa (ndi ine ndili mkati mwake) komanso zomwe ndakumana nazo pakufufuza m'munda (*field-research*) ngati katswiri wa chikhalidwe cha anthu (*anthropologist*) m'mayiko osiyanasiyana—kuphatikizapo a ku Africa—ndinazindikira kuti njira yokhayo yofufuzira malo akutali ndi otchedwa "kukhala wina" (*otherness*), kungakhale kudalira kuthekera ndi kupadera kwa thupi lomwe lili ndi chidziwitso ndi kumva.

Chifukwa chake, cholinga cha nkhani yotsatirayi ndikufotokoza kudzera m'maganizo omasuka ndi kugwirizana, matanthauzo ena ogawana pakati pa Poland



ndi Rwanda (omwe mwamwayi ndi nkhani ya kafukufuku wanga womaliza), omwe amatuluka mu thupi lomwe limamva. Kenako ndidzayesa kupereka lingaliro la zolemba, kumene thupi - makamaka thupi la mkazi - ndi njira yandakatulo, yolemba mozama mwaumwini, ikhoza kuyimira mlatho wopita ku kumvetsetsana. Mwa kuyika papepala kuyenda kwaulere kwa malingaliro ndi zochitika zaumwini, ndidzayesa kuwonetsa kuti "mlatho" uwu ungagwiritsidwe ntchito ngati chida chofunikira pomvetsetsa ndi kufotokoza mitu ina: Rwanda, Poland ndi malo ena, ndipo nkhani zotchulidwa pano zidzatengedwa chabe ngati zitsanzo.

Kupereka chidziwitso chapadera ku kawonedwe ka amayi kapena kutsindika - kaya kudzera mu luso, sayansi, ndale kapena kungokhala nawo mu zokambirana za tsiku ndi tsiku - zikuwoneka kuti zikadali kuonedwa ngati "chabe" kawonedwe ka *feminist* (omenyera ufulu wa amayi) ndipo monga choncho – nkhani yamphepete, ngakhale yosafunika kwenikweni. Wina anganene zimenezi za dziko langa lachiyambi, Poland, onse mkati mwa ndale zamakono za kumanja ndi maphunziro apamwamba, kumene kuli kuti ngati kugonana kwa amayi kukubwera ngati nkhani m'bwalo la anthu, n'zotsimikizika kuti sikudzavomerezedwa mopanda manyazi ndi kukumbatiridwa ndi gulu lalikulu.

Thupi, koma makamaka thupi la mkazi - ndithudi, lomwe silikusamalidwa, kulingaliridwa, ndi kuwonetsedwa ndi chisamaliro chofanana ndi kumasuka ngati thupi la mwamuna. N'zosadabwitsa kuti kusiyana kumeneku kumakhudzanso gawo lachinsinsi: lomwe tiyenera kutha kumva tokha, kudzera m'matupi athu ndi mphamvu zathu zamaganizo (*senses*). Mosakayikira lingaliro la kugonana kwa mkazi ndi chithunzi chilichonse cha chiwalo cha thupi chokhudzana ndi izo chimapitilira kukhala nkhaniyo yoletsedwa (*taboo*) ku Poland. Izi zimakhala zoopsa pamene zimapitilira kungokhala taboo kapena nkhani "yina" yomwe imakambidwa m'magulu omwe amaonedwa ngati amphepete (ojambula, omenyera ufulu, olemba), m'malo mwake ikachitika, imaletsedwa poyera ndikupondezedwa ndi gulu lamphamvu, lolamulira, losunga miyambo. Kapena izi zimachitidwa ngakhale ndi amayi, pamene ali pakati pawo okha, m'malo omwe akuyenera kukhala achinsinsi ndi otetezeka.

Mu nkhani ya ku Poland, kutalikirana - kapena ndinganene - kusalumikizana ndi matupi athu ndi kugonana, makamaka komwe kumakulitsidwa ndi maziko a Katolika a chikhalidwe ndi banja, kumakhala kochititsa chidwi poyerekeza ndi machitidwe amasiku ano a ku Rwanda a maphunziro osavomerezeka a kugonana ndi momwe amayendera nkhani ya kugonana ndi matanthauzo ake. Kulumikizana kwa anthu ambiri aku Rwanda ku cholowa chakale cha chikhalidwe ndi nthano zoperekedwa pakamwa ndi kwapadera - ngakhale kuti palibe umboni wambiri womwe watsala mpaka nthawi yathu ino. Ndine kutali ndi kunena, komabe, kuti



nkhaniyi ku Rwanda ilibe mikangano. Komabe, pano tikufika pachimake cha nkhani yanga: ndi thupi, thupi la mkazi mu mkhalidwe wake wa kugonana lomwe limalimbikitsidwa kukhala mboni ya kudziwika kwa munthu (wina anganene kuti ngakhale - kudziwika kwa dziko!) ndi maziko a kudzizindikira.

Popeza ndatembenezira chidwi changa ku kuwunika mwanzeru thupi langa ndi zonse zomwe likundiiza, ndatsegulanso ndekha ku chikhulupiriro champhamvu (mosasamala kanthu momwe chingatchulidwire mu chipembedzo chilichonse) kuti palibe chomwe chimachitika popanda cholinga, ndipo moyo ungatengedwe ngati dontho m'nyanja (osati mu ndowa). Kumva komwe kumaphatikizapo ndi kupitilira zonse zomwe chikhalidwe cha munthu chimamupangitsa. Potsatira intuition yanga, ndikukhala wotseguka ku zizindikiro zamitundu yonse, ndinadzipezera ndekha mwayi wopereka *massage* - zomwe ndimazitenga kuyambira pachiyambi ngati njira yodziwika, yauzimu ya kusinkhasinkha (*meditation*) ndi njira yachindunji yolankhulirana ndi munthu wina. Ine - yemwe amadzitanthauzira yekha makamaka ngati mkazi ndipo - mwamsanga pambuyo pake - ngati *Cultural Anthropologist* yemwe akufunafuna kulumikizana kowona ndi kozama ndi Wina (*the Other*), ndinapeza mu kukhudza komvetsera (ndithudi, *Seeing Hands* - Manja Owona - uku ndiko momwe gulu lodabwitsa la ku Rwanda la othandizira a *massage* omwe ali ndi vuto la maso adatchulira kampani yawo) njira yomvera munthu wina ndi ine ndekha popanda mawu ndi oyimira pakati.

Pomvera mawu anga amkati ndikutsatira kuyenda kwanga (*flow*), ndinapatula ndi kukongoletsa chipinda chimodzi chapadera m'nyumba mwanga chifukwa cha "misonkhano ya *massage*" iyi. "Misonkhano" sikutanthauza chabe "*massages*" – ili ndilo tanthauzo lokhalo lomwe limabwera kwa ine ndikaganizira za ubwino wonse wa magawo awa, omwe nthawi zambiri amapita ndi mphamvu yawo kutali ndi kungokhala mchitidwe wokhudza/kupereka *massage*. Osati popanda kumva kudabwa, ndinapeza kuti zithunzi za amayi amaliseche: kuyambira *femme fatales* (amayikokopa) akale mpaka oyera mtima (saints), nyenyezi za porno ndi zidole za chonde za mu Africa, zinayamba kukhala mu spa yanga ndi kudyetsa mwachindunji amayi omwe amandichezera kumeneko. Mwa njira, spa ndi chidule cha '*Sanus per aquam*' – 'thanzi kudzera m'madzi' - zomwe ndizofunikira kwambiri mu nkhani ya zomwe ndidzayesa kufotokoza m'pepala ili.

Posachedwa zinawonekeratu kwa ine kuti pamene munthu apereka chisamaliro chopanda malire, chidwi chachifundo ndi kukhalapo kwenikweni kudzera mu kukhudza, kusamala ndi nthawi yomvetsera komanso "kuperekeza" munthuyo panthawi ndi pambuyo pa *massage*, wolandirayo nthawi zonse adzayandikira kwa iye mwini. Ndi nthawi yochulukirapo ndi kuwonjezeka kwa chiwerengero cha misonkhano ya *massage* yomwe ndapereka, ndinadabwa kwambiri ndi momwe tiliri



ndi chidziwitso chochepa ndi kudzidalira (makamaka amayi—omwe ndi ambiri mwa alendo ku spa yanga), pa mfundo yakuti thupi lathu lakuthupi liri lolumikizana ndi zinthu zonse zomwe timadutsamo ndi kupitilira apo.

“Thupi limasunga zolembe zake” (*The body keeps the score*)—kugwira mawu mutu wa buku la Dr. Bessel van der Kolk, lomwe limanena makamaka za trauma (n’kovuta kusatchula nkhanayi pamene tikukamba za mkhalidwe uliwonse wa maganizo wa anthu a padziko lapansi lero, ndipo ndithudi za Rwanda ndi Poland zamakono—aliyense pamlingo wosiyana ndi zifukwa zosiyana zoposa zomwe zili mu nkhanayi) ndi momwe limasinthira thupi ndi ubongo. Kuphatikiza apo, Van der Kolk akuwululanso mphamvu yodabwitsa ya maubwenzi athu onse kuvulaza ndi kuchiritsa. Chomwe chili choyenera kunena pano ndi chakuti mawu akuti "ubale" (*relationship*) amatanthauza kulumikizana pakati pa anthu, ndi kuyandikira kwachinsinsi, kwachikondi (*tender*) kwa ife tokha, ndi matupi athu.

Potsatira lingaliro la chikhulupiriro changa mu kuyenda kwa moyo, sindikuona ngati kungochitika mwamwayi kuti ndikhoza kuwulula mu nkhanayi lingaliro langa lophatikiza magawo atatu: zochitika zanga ndi zolimbikitsa zomwe ndapeza mu zomwe zimatchedwa "munda" (*field*) (posachedwapa Rwanda), nkhani zosankhidwa zokhudzana ndi zokambirana za amayi kuchokera ku chikhaliidwe changa cha tsiku ndi tsiku ndi luso (Poland), ndi zonse zomwe ndazindikira kudzera mu chilakolako changa: kupereka "misonkhano ya *massage*" kwa amayi.

Monga momwe Wina (*the Other*) nthawi zonse amakhalira wofunika kwa ine, sindidzawona ngati kungochitika mwamwayi nkhani ya yemwe akuthandizira kukwaniritsa polojekiti iliyonse yomwe – kubwerera ku fanizo la madzi - imatumphuka kuchokera pantima. Mnzanga yemwe anandidziwitsa za kuthekera kulemba nkhani yapadera (mwachiyembekezo yomwe mukuwerenga tsopano), yomwe idzapereka "njira zatsopano zowonera zomwe zili pafupi ndi zomwe zili kutali", anali mnzanga wapantima Jakub Kościółek, Pulofesa Wotheadizira ku Institute of Intercultural Studies ya Jagiellonian University ndi Purezidenti wa The Interkulturalni.pl Association. Kamodzi pachaka, ndakhala ndikuitanidwa naye kuti ndipereke phunziro lokhudza kuwerenga kotheka kwa postcolonial kwa zomwe zimatchedwa Luso la mu Africa (*African Art*), ndipo nthawi zonse ndimachita chidwi ndi kumasuka kwake ndi njira yake yachifundo ku njira yanga (ndi mitundu ina ya "anthu odabwitsa" chimodzimodzi) ya kukhala ndi kuwona zinthu. Zikomo Jakub!

Munkhanayi, sizodabwitsa kwa ine kuti ndinapatsidwa mwayi wa kusinthana (barter) (ine kupereka *massage*) kwa mnzanga Urszula Rapacka, yemwe anavomereza pempho langa la kuwerenga ndi kukonza nkhanayi (proof-reading).



Chochitika mwamwayi ichi chikuphatikiza – mwapafanizo ndi mwamachitidwe - maziko a nkhanayi. Zikomo, Ula! (Kuphatikiza apo, kuti nkhani ya zochitika mwamwayi ikhale yodabwitsa kwambiri, ndidzawonjezera kuti Ula nthawi ina anakhala mwini wa chidole cha chonde chomwe ndinachipeza pamsika wina wa luso ku Ghana chomwe chinali chofanana kwambiri ndi iye...!).

### **Zochitika mwamwayi kuchokera pafupi kwambiri ndi kutali—za madzi ndi kudzindikira thupi**

Kuyesa kwanga koyamba kukhala ndi kuwunika kozama kwa kusakanikirana kwa mitu kumeneku kunalimbikitsidwa ndi mutu wa Msonkhano Wadziko wa Zikhalidwe womwe unachitikira mu October 2021 ku Nowy Sącz ku Poland, kumene ndinaitanidwa kuti ndipereke phunziro lozikidwa pamutu wakuti Such source, such water. *Priestesses, sorceresses, temptresses* (Gwero lotere, madzi otere. Ansembe aakazi, amatsenga aakazi, okayezera aakazi). Ndinaganiza pamenepo kuthira mphamvu yapadera pa chizindikiro cha madzi polumikizana ndi ukazi mu miyambo ina yosankhidwa ya mu Africa, zikondwerero, kapena zikhulupiriro. Ndinadziwitsa mwadala kwa anthu zolembe zina za chikhalidwe—machitidwe, zikhulupiriro, zida, ndi makhalidwe, zomwe zikuwulula matanthauzo a chikhalidwe omwe ali amakono komanso ozikidwa mu mwambo. Zonsezi zimaphatikizapo kachidindo (code) kosiyanasiyana, kochulukuka ka kuphwanya matanthauzo onse ndi magulu oikidwa ndi chikhalidwe, omwe nthawi zambiri amaperekedwa ku zikhalidwe izi kuchokera ku utsamunda kapena - m'njira yayikulu - chikhalidwe cha Katolika/amishonale, cholamulidwa ndi amuna (*patriarchal*), choyera.

Chimodzi mwa zolembe za chikhalidwe zomwe ndinatchula chinali gwero lochititsa chidwi la zikhalidwe zosiyanasiyana la chikhulupiriro cha *Mami Wata* (mayi wa m'madzi) kudutsa Africa yonse. Zithunzi zake – mwina zoperekedwa kuchokera ku poster ya ku Germany (!) yosindikizidwa m'ma 1880, yoyimira mnyamata wa ku Samoa (!! ) (womwe anatengedwa ngati mtsikana) ataima ndi njoka – zikuwulula nthawi yomweyo khalidwe lake la mbali zambiri ndi mikangano. Chithunzi chake ndi zizindikiro zake zimanena za kukongola kwake kokopa, komwe kumapereka zonse ziwiri lingaliro la kumwamba ndikulanda otsatira ake zonse zomwe ali nazo ngati sakhala okhulupirika (koposa zonse pakugonana) kwa iye. Malingaliro a madzi, chonde, kugonana ndi mphamvu zosamveka bwino za amayi zikuwonetsedwa pamutuwu.



Potsatira izi, ndinabweretsa zochitika zanga zaumwini zotenga nawo mbali mu 57th International Art Exhibition Biennale ku Venice mu 2017, monga mmodzi wa amayi zana limodzi omwe amapanga nawo chiwonetsero cha wojambula wa ku Nigeria Jelili Atiku. Chiwonetserocho, chokumbutsa mwambo wolemekeza amayi ndi gawo la ukazi (kachiwiri - madzi) cholinga chake chinali "kuyambitsanso chikhalidwe cha munthu" ndi "kumasula malo ku utsamunda" (kugwira mawu wojambulayo) mwa kupereka mawu kwa amayi ngati "amfumukazi" a madzi mu mzinda wachikazi wapamwamba - Venice.

Pomaliza, ndinayambitsa zokambirana pamutu wosangalatsa wa kuwukitsidwa kwa mwambo wa amayi wa *gukuna* ndi nkhani ya kupeza *kunyaza* kapena chisangalalo cha pachimake chogonana kwa amayi (chomwe chimatchedwanso "madzi achikazi" kapena "squirting ejaculation") ku Rwanda. Ndinapambana kukhudza mutu uyu mwachidule panthawi ya kafukufuku waufupi wam'munda yemwe ndinapanga m'malo mwa SWPS University ndi Polish-German Foundation potenga nawo mbali mu polojekiti yasayansi yokhudza magwero a ku Poland ndi Germany ku Rwanda ya nthawi isanayambe utsamunda (*precolonial*).

Mutu wa kafukufuku wanga wa PhD ku Madagascar: mpatuko wa makolo a *tromba* – unaphatikizidwanso mu phunzirolo. Ndi chodabwitsa momwe njira yathu ku mutu winawake ingakulire ndi kupeza matanthauzo atsopano ikawonedwa kudzera mu diso latsopano: kuti ndinapereka chidwi chachikulu ku thupi la mkazi ndi matanthauzo ake, kuwerenga kwatsopano kwa mwambo wa tromba waku Malagasy kunabwera m'maganizo mwanga. Sing'anga (*medium*) wa mzimu wa makolo si mkazi winawake ndi ntchito zake zokhazikitsidwa ndi chikhalidwe, koma kwenikweni thupi lake – chidebe chabwino kwambiri. Mawonekedwe opanda malire, osintha, ngati madzi omwe angathe kukhala ndi mitundu yonse ya matanthauzo ndithudi.

Polankhula za zomwe zimatchedwa zochitika mwamwayi, miyezi ingapo pambuyo pa Msonkhanowo, ndinali ndi mwayi wopereka phunziro lofananalo m'mbali mwa nyanja ya ku Poland, ndi kukhalapo kwachete kwa nyanja yokhayo kumbuyo—mu City Culture Institute ku Gdańsk. Nthawi ino, kunatsatiridwa ndi zokambirana ndi anthu—pakati pawo panali amayi azaka zonse ndi malingaliro osiyanasiyana pa nkhani ya kugonana, komanso anthu omwe ali ndi zikhulupiriro zolimba zozikidwa pa malingaliro olakwika a Africa ngati kontinenti "yamdima ndi yakale" yokhala ndi miyambo ndi makhalidwe "opanda chitukuko" (?).

Ndinadabwa kwambiri pamene–pamene phunzirolo linkapita patsogolo - ndinawona kuti anthu anasonyeza kusokonezeka ndi ngakhale mkwiyo pamene ndinakhudza momwe zinthu zilili panopa ku Poland okhudzana ndi maphunziro a kugonana



(makamaka—kusowa kapena ngale kuletsa kwake) ndi—monga zinatulukira mu zokambirana—kudzindikira kochepe kwa thupi. Chochitika chochititsa chidwi chinali chakuti mwanjira ina ndinamva kukhudzidwa ndi zizindikiro za manyazi ndi khalidwe loonetsa chilakolako chofuna kuthawa/kusowa, ndipo zotsatira zake, mawu anga—monga momwe zimakhallira nthawi zambiri ndikamva kuti ndatuluka mu "kuyenda" kwanga—anayamba kunjenjemera. Zinaonekeratu kuti zomwe zimatchedwa kugonana (*sex*) zomwe tazunguliridwa nazo: zithunzi, mafilimu, mafashoni okopa, zithunzi zotukwana za amayi omwe amangowonedwa ngati zinthu—zilibenso mphamvu, ndipo zimamezedwa ndi ife mwa njira yosasamala ndi yopanda chidwi. Komabe, ngati munthu atchula nyini (*vagina*) ndi dzina lake, kuichitira ngati gawo lachilengedwe la thupi (osati chabe ngati chida cha "ntchito" yobereka) ndikunena za ufulu wa chisangalalo chodziwika ndi chamuyo—zonsezi zidzaputa kusokonezeka kwakukulu.

Wina anganene kuti mwina chinali chifukwa cha "maphunziro", nkhani yovomerezeka ya phunziroli, malo ake (Culture City Institute) kapena mutu wake (wokhudza Africa, madzi, ndi cholowa), kuti manyazi ndi kumva kosasangalatsa kunabuka chifukwa cholephera kukumbatira thupi lathu kwathunthu ngati thupi lachiwerewere, lachilengedwe, lamalingaliro. Komabe, kuwona kusokonezeka wamba ndi kusowa kudzidalira pa mutu wa kugonana kwa amayi kunadzutsa chidwi changa pamene ndinatenga nawo mbali mu misonkhano ingapo ya pa intaneti yokhudza kugonana kwabwino (*positive sexuality*)—kuimira njira yatsopano ya chikhalidwe ndi nzeru ku Poland.

"Tikukuitanani ku dziko kumene kugonana kumawonedwa ngati gawo la ntchito ya munthu - losawopseza munthu, lopanda liwongo ndi lopanda manyazi" - ichi ndi gawo la lingaliro la Sex Positive Institute ku Warsaw. Ngakhale mawonekedwe a pa intaneti amayenera kuwonjezera kudzidalira osati kuwonjezera manyazi kwa otenga nawo mbali, amuna ndi akazi onse (ngakhale ambiri a otenga nawo mbali anali amayi) anasonyeza kusalumikizana kwakukulu ndi nkhanayi - mocheperapo kapena poyera, kuwonjezera *irony* (makamaka amuna) kapena kudzimba mlandu (makamaka amayi). "Kukhala 'sex positive' kumatanthauza kuwona zochitika zonse za kugonana zovomerezeka (zovomerezedwa ndi onse otenga nawo mbali) ngati zathanzi komanso zosangalatsa, zimalimbikitsa kumva chisangalalo cha kugonana ndi kuyesa zatsopano" - wina akhoza kuwerenga pa tsamba la Institute. Poyang'ana tsopano ndandanda ya misonkhano yotsogoleredwa ndi mmodzi wa alangizi a kugonana (*sex coaches*) ndi ophunzitsa - Agnieszka Szeżyńska - ndi kukhala m'maganizo manyazi aakulu omwe analamulira ambiri a otenga nawo mbali achikazi, kutchuka kwa misonkhano wotchedwa: "Zosowa: mchitidwe wofotokoza zosowa ndi kunena 'inde'", sikundidabwitsa.



Marta Niedźwiecka, katswiri wa zamaganizo, mlangizi wa kugonana, ndi wolembe nawo buku la *Slow Sex*. Liberate Loveakuwona kuti pokhala m'maganizo mbiri ya ndale ndi chikhalidwe cha ku Poland, “slow sex (kugonana pang'onopang'ono) ndi za mpweya m'mutu ndi kupezanso kulumikizana ndi thupi, osati kwenikweni – kupeza njira zapamwamba ndi kumira m'zinsinsi za kusamala (*mindfulness*), komwe kukuyamba “kudya mchira wake”. Momwe mungakhalire ndi slow sex ndi maubwenzi opambana pamene mukuyenera kuchita zionetsero m'misewu ndi banneryonena kuti “Ndikuchita mantha kugonana”? Gulu lonse la chitukuko cha munthu payekha lozungulira kugonana, lomwe likupeza chidwi chachikulu ku Poland, mbali imodzi ndi yankho ku kusowa kwakukulu kwa maphunziro a kugonana, koma mbali inayi - njira yopita ku “njira yodzikonzera yekha” ya Foucault (*self-arranging technique*).

Pomvera amayi ambiri omwe amabwera ku misonkhano yanga ya massage ndikuwona zomwe zikuchitika mu chikhalidwe ndi “makampani” a kudzitukula ku Poland, ndikugwirizana ndi Niedźwiecka kuti makamaka amayi akuchulukirachulukira kutenga nawo mbali mu ndondomeko yosatha ndi yosakhutiritsa ya kudzikonza, yomwe cholinga chake ndi kuwonjezera zokolola zawo, popanda kuwapangitsa kukhala omasuka ku chinsinsi, kudzindikira thupi ndi chisangalalo cha kugonana (mu tanthauzo lalikulu la mawuwu). “Kulinganiza ndi kupondereza kugonana kumatenga mitundu yosiyanasiyana – ya malamulo okhwima, zilango zosatsatira, masomphenya a tchimo, kutsutsidwa komwe kumadziwika m'dera ili la ntchito ya munthu. Timaphunzira kuyambira ubwana kuti zinthu ‘kumeneko’ ndi zodetsa, kuti thupi lokha ndilokayikitsa. Kodi tikuyenera kukhulupirira bwanji thupi ndikumanga kulumikizana nalo - zomwe ndizofunikira kuti tikumane ndi kugonana kwathu?” akutero Niedźwiecka (2021). Mwayi wa amayi wotukuka udzakhala wochepe ngati tipitiliza kunyozetsa zakuthupi, kugonana, ndi malingaliro athu omasuka.

“Popanda kudzindikira kumva kwa thupi ndi maganizo, munthu amagawikana kukhala mzimu wopanda thupi ndi thupi lopanda chidwi” - anatero Alexander Lowen (2011), katswiri wa psychotherapy ndi tate wa *Bioenergetics*, yemwe kafukufuku wake ndi malingaliro ake amakhudza kwambiri ubale wanga ndi ntchito ya thupi. Ulamuliro wamphamvu womwe timadzikakamiza tokha ndi matupi athu (omwe nthawi zambiri amawonedwa chabe ngati makina ogwirira ntchito omwe amapangitsa malingaliro athu kugwira ntchito ndikutisunga mwanjira ina pamwamba pa kuyenda kwa moyo – madzi! - kutiteteza ku kumira), kwenikweni kuli kofanana ndi mantha a kugwa. Lowen akupitiliza kunena zotsatirazi: “chifukwa timaopa moyo, timafuna kuwulamulira kapena kuudziwa bwino”. M'buku lake limodzi, adawona kufanana kochititsa chidwi m'mawu a Chingerezi: *falling asleep* (kugona) ndi *falling in love* (kugwa m'chikondi). Ndithudi kuchokera ku



kawonedwe ka thupi, kusintha kuchoka pakukhala maso kupita ku kugona kungafanane ndi kugwa, ndipo monga choncho kumayambitsa nkhwana ndi kusamvana. Ndongomeko yoganiza iyenera kuzimitsidwa ndipo sidzayendetsedwanso ndi malingaliro.

Mphamvu za njira zonse ziwiri (kugona ndi kukonda) ndizofanana – zokhudzana ndi kuzimitsa kwa ulamuliro wa malingaliro ndi thupi. Chinsinsi cha kugwa ndikudzipereka kwa iko, kulola mphamvu kuyenda m'thupi lathu mopanda mantha. Mchitidwe wodzipereka, kapena, kubwerera ku lingaliro lalikulu la nkhanayi—kumva gawo la madzi mwa ife tokha—n'kofunika kwambiri polola ife tokha kumva mitundu yonse ya zosangalatsa: kuchokera ku zomwe zimabwera panthawi ya *massage* yopumula kupita ku zochitika zazikulu za *orgasm* (pachimake pa kugonana). “Kuti timvetsetse chifukwa chake kugwa kuli ndi mphamvu yayikulu, tiyenera kuganizira za moyo ngati kuyenda. Kusayenda ndi imfa” - Lowen (2011) akutero. Iye akupita patsogolo mwa kunena kuti: “Kugonana si chinthu chongochita nthawi yopuma kapena kwakanthawi. Ndi njira yokhalira ndi moyo”.

### **Tiyeni tiyambe kuchokera ku nyini (*vagina*) - yosakwanira kapena yochuluka kwambiri?**

M'buku la *Fuck shame. A history of sexual revolution*, Ewa Wanat akulemba:

"Mukakhala ndi ufulu wa kugonana, thupi laulere, mukadziwa momwe mumagwirira ntchito, mumaphunzira kutchula zakukhosi kwanu, kotero mumasintha kwathunthu malo anu padziko lapansi, mutha kupanga zisankho zosiyanasiyana. Tangodziwa kwa zaka makumi angapo chabe momwe clitoris (kakang'ono) amawonekera zenizeni. Chifukwa chiyani sichikhala chidziwitso wamba? Mwana aliyense amatha kujambula mbolo, koma clitoris? Ngati mayi sakudziwa thupi lake, alibe kulumikizana nalo, alibe chidziwitso nalo, kotero zidzakhala zosavuta kumugwiritsa ntchito. Kumugwiritsa ntchito ngati makina oberekera. Akamadziwa zambiri, m'pamenenso angapange zisankho zokhudza moyo wake."

Jess Zimmerman, wolembe buku lolimbikitsa kwambiri, lomwe posachedwapa lamasuliridwa mu Polish lotchedwa *Women and Other Monsters: Building a New Mythology* (Amayi ndi Zilombo Zina: Kupanga Nthano Yatsopano), amagwiritsa ntchito zitsanzo za nthano pa zochitika zake zaumwini ndikutanthauzira molakwika nthano zowziwika bwino za chi Greek, kuzitcha "nkhanu za ana zosimbidwa ndi ulamuliro wa amuna (*patriarchy*) kwa iwo okha asanagone". Pamaziko awa,



akulimbikitsa amayi kukonda makhalidwe ndi zochita zomwe zimaonedwa ndi chikhalidwe ngati "zosayenera" komanso "zowopsa" kwambiri kwa "jenda lofooka".

Langizo limodzi lomwe amapereka kwa amayi ndikuwunikanso maubwenzi awo ndi makhalidwe osafunika pachikhalidwe monga njala, mkwiyo, kuipa, ndi kukhumbautchuka (*ambition*), komanso kukhala wogonana poyera kapena wosakopa mokwanira.

"Kukhala kunja kwa mwambo", "osakhala achilengedwe" kapena ngakhale owopsa, kwenikweni ndi - Zimmerman akutero - mphamvu zazikulu za amayi. Mwina ndichifukwa chake m'chipinda changa cha spa choperekedwa ku misonkhano ya massage, *femme fatales* onyada ndi osamba dzuwa amaliseche okhala ndi matupi akutali ndi mtundu wa ziboliboli, amakhala mbali ndi mbali. Onsewa ali "m'mphepete" mwa zomwe zimazindikiridwa ndi amuna (komanso zovomerezedwa ndi amayi ambiri) ngati zokopa zopanda vuto kapena zopotoka kwambiri ndipo "zokokomezwa". Amayi amaphunzitsidwa kuchita kusowa kwa malingaliro nthawi zonse ndi "njala ya malingaliro": amalangizidwa nthawi zonse "kufuna zochepe kuti musavutike ndi kusowa" – Zimmerman akulemba. "Chilakolako chilichonse chingatengedwe ngati umbombo ngati chiri choletsedwa - mwachitsanzo, kugonana. Mfundo yakuti amuna ali ndi njala ya kugonana imatengedwa ngati yachilengedwe ndipo imagwiritsidwa ntchito ngati chowiringula. Pamene mkazi akufuna kugonana, timayang'ana kumbali mwa kunyansidwa. Kugwidwa pamene "ukufuna" ndi mtundu woipitsitsa wa chipongwe".

Mu nkhani ya ku Poland, munthu sayenera kuyang'ana patali zitsanzo za chikhulupiriro chotere. Pamene ndinkalemba nkhanayi, nyimbo yatsopano kuchokera ku *album* yotchedwa *Wolne* (zomwe mu chilankhulo cha Polish zikutanthauza onse "amayi aulere" ndi "pang'onopang'ono") yotchedwa *Gadgets* inatulutsidwa ndikuyankhulidwa kwambiri pa intaneti. *Albumyi* inajambulidwa ku SBM Label, kampani yotsogola yujambula nyimbo ya Polish *rap* (yodziwika pakati pa ena chifukwa cha oimba otchuka monga Solar, Bedoes, ndi Mata), yozikidwa mwamphamvu m'nkhani zolamulidwa ndi amuna, zowonetsedwa onse mu chiwerengero cha amuna achinyamata pakati pa anthu kapena - gulu la *rap* ndi ojambula omwe amapanga zolembe zozikidwa pa kawonedwe ka amuna.

Wolembe album ya *Wolne* ndi Dorota Masłowska – wolembe wotchuka komanso wowona wamkulu wa irony wa zenizeni za ku Poland komanso mbuye wa mawu. Polandira mphotho yapamwamba ya magazini ya *Polityka* ngati Mlengi wa Chikhalidwe wa 2022, adati:



“Chikhalidwe ku Poland ndi chotsutsana ndi amayi, ndipo ndinali wozunzidwa, wopindula ndi mboni chabe ya chikhalidwe ichi.”

Mawu khumi ndi awiri a nyimbo pa *albumyi* ndi nyimbo zawo zochepe zomwe zimawazungulira, zikuwonetsa – pakati pa ena - cholinga chofuna kufufuza chilankhulo chomwe chimafotokoza zachiwerewere za amayi ndi mlengalenga wa manyazi/zoletsedwa womwe ukulamulira ku Poland lero womwe umazungulira chilankhulo, zithunzi ndi mafotokozedwe ake. Mawu a nyimbozo komanso *album* yonseyo akhoza kuwonedwa ngati "kufupikitsa zenizeni kukhala piritisi", monga wojambulayo ananenera polungamitsa kusankha kwake kwa mawonekedwe a *rap* m'modzi mwa mafunso, zinaputa kuukira kwakukulu kwa iye (osati koyamba kozikidwa pa zifukwa zomwezo) chifukwa cha njira yake yachindunji yofotokozera zosowa za kugonana za amayi. M'mafunso, Masłowska akutero: “Ndimakonda kwambiri nkhanu yofotokoza za kugonana mu *rap* - pamaziko a zomwe chilankhulo changa chinganene za izo, momwe ndimamvera za izo, zomwe ndingapereke. Mawonekedwe otseguka kwambiri a nyimbo pamutuwa akuwoneka kuti ndi nyimbo zotchuka za ku Poland, zomwe ndingazitchule kuti "zoberekeru", zomwe ndi *disco polo*, zomwe zimavomereza kufotokoza chilakolako kuchokera kwa amuna ndi akazi. Pop ndi yamanyazi: kugonana kumasinthidwa ndi “kukutenga m'manja mwanga” ndi “kudzuka m'mawa.” *Rap* imatenga kugonana momasuka kwambiri ndipo ndiwo umodzi mwa mizimu yake yosokoneza”.

Mosasamala kanthu za mlingo womwe tazunguliridwa ndi zithunzi zachiwawa, zolamulidwa ndi amuna, zachiwerewere ndi chilengedwe (*cosmos*) (ndikugwiritsa ntchito mawuwa mwadala pano), chomwe chimaputa udani ndi kukana ndi kawonedwe ka amayi ndi malingaliro awo okhudza matupi awo, omwe amawonetsedwa poyera kupitilira "ntchito" yawo yomwe imatikakamiza kukhala pa mlingo wa zongopeka za kugonana za amuna, kapena kukhala mu mchitidwe wa chonde ndi umayi. Diso la mwamuna (komanso la mkazi!) lomwe limasinthu munthu kukhala chinthu ndi machitidwe a "momwe amayi ayenera kumvera, kuganiza ndi kuchitira" ku kugonana kwawo, kwenikweni zili ozikidwa mozama m'malingaliro athu odzazidwa ndi chikhalidwe ndipo zili ndi mphamvu pa ife kuposa momwe timaganizira. Chikhulupiriro chomwe ndikufuna kugawana pano, ndichakuti ku Poland lero ife, amayi ndi amuna, sitinakulitsebe zida zovomerezeka ndi chikhalidwe, zomwe zingagwiritsidwe ntchito mwaufulu kufotokoza ndi kukhala ndi chisangalalo m'mithunzi yake yonse ndi kusiyanasiyana kwina osati ufulu wowona ndi kumvera matupi athu mwachidziwitso.

Pano pali kumasulira kwanga kwachidule kwa nyimbo ya Dorota Masłowska "Gadgets":



"Ndinalimba mtima kugula zoseweretsa za kugonana (sexual gadgets) mwakilo, zilibe kanthu ngati zinali zogwiritsidwa ntchito, koma zili bwino kwambiri, zotsika mtengo. (...) Ndatopa ndikudikirira, ndikufuna chisangalalo chopanda malire (...) Ndikutsegula nyumba, anzanga amafunsa zomwe ndili nazo m'chikwama, ndikunama kuti ndi mbatata koma zoseweretsa za kugonana zikutuluka! Chipwirikiti m'nyumba yonse, adzauza abambo, amayi, koma sindikumva manyazi, lero ndikuwuluka mumlengalenga – bye! (...) Au Revoir mbolo, miao miao".

Mwachilungamo, Niko Graczyk, mtolankhani wa magazini ya noizz, anatcha *album* ya Masłowska "kuyesa kosangalatsa kwa chikhalidwe", ndipo anapitiliza, "Kwa okonda SBM Label — achinyamata, koma osunga miyambo panyimbo ndi omwe amalumikizidwa ndi chikhalidwe cha amuna cha *hip-hop* — nyimbo za Dorota zili ngati nsalu yofiira kwa ng'ombe yamphongo. Ndipo *album* yake ya "Wolne" ili bwanji? Ili ngati kukhala ndi agulugufe m'mimba. Kwa anthu ena zimapangitsa kusanza, kwa ena chilakolako chofuna kugwa m'chikondi, ngakhale mwina mosasangalala".

Kufanizira komwe kwatchulidwa kumabweretsa kuyenda kwa maganizo anga pafundo iyi: ngati munthu ayamba kumvera zomwe thupi likunena, mwina adzafika ku chiwonetsero chowona cha zosowa zathu, zokhumba ndi mantha, kuposa zomwe ziri zovomerezeka ndi chikhalidwe (ndipo monga choncho – zoletsedwa ku nthawi ndi chikhalidwe). Ngati titamvera kwenikweni mtundu wa agulugufe kapena nyongolotsi zomwe zikuyendayenda m'mimba mwathu, ngati titalola malingaliro kunjenjemera, ndi kumva mafunde akubwera ndi kupita a mitundu yonse ya ululu, chisangalalo, ndi kusapeza bwino m'malo mowapha nthawi yomweyo kudzera mu mankhwala opha ululu ndi mapiritsi, kapena mwa kuyesa zivute zitani kuti tigwirizane ndi tanthauzo lovomerezeka ndi chikhalidwe kapena chipembedzo la khalidwe loyenera la jenda – tikhoza kufika ku kumvetsetsa kozama kwa ife tokha ndi kulankhulana kodziwa zambiri ndi ena. Tikhoza kulenga chikhalidwe ndi gawo la anthu kuchokera m'mimba.

"Panthawi ya zochitika zakuthupi, kuganiza n'koletsedwa kwambiri" – analemba Michalina Wysłocka, dokotala wa amayi (*gynaecologist*), katswiri wa kugonana (*sexologist*), ndi wolembe buku loyamba la malangizo a moyo wa kugonana pakati pa mayiko a chikomyunizimu lotchedwa *The Art of Loving, A Practical Guide to Marital Bliss*, losindikizidwa mu 1978 ndi kusinthidwa kangapo, lomwe pang'onopang'ono linayambitsa chizolowezi cha kumasuka kwambiri pa nkhani za kugonana ndi moyo wa kugonana ku Poland. Njira iyi ikhoza kukulitsidwa kupitilira moyo wa kugonana: masiku ano tadulidwa ku kukhudzidwa ndi zinthu za thupi. Kumva - ngakhale panthawi ya chinthu chaumwini ngati kulandira *massage* - nthawi zambiri kumawoneka kuti kukugwera mu kugawikana komwe



kwakhazikitsidwa mwamphamvu ndi lingaliro la mzimu wolemekezeka ndi kulingalira (komwe kumawonedwa mwachikhalidwe ngati kwamwamuna) ndi thupi lodetsedwa (lachikazi).

Tataya kulumikizana ndi thupi lathu, ndipo tasuntha kutali ndi kukhulupirika kwa mzimu ndi thupi. Ponena izi kuchokera ku kawonedwe ka wothandizira wa *massage*, ndingathe kunena kuti ambiri a ife tadulidwa kuchokera m'chiuno kupita pansu. Monga mwambi umanenera (kungakhale kovuta ngakhale kufufuza gwero lake la chikhalidwe, popeza ukudziwika m'malo ambiri a dziko lapansi): "Milungu inatengera gawo lapamwamba la thupi lokha, gawo lapansi ndi la satana".

Munthu akhoza kuwona poyambira pa mantha ozama ndi manyazi a thupi la mkazi—makamaka ziwalo zomwe zingamupatse chisangalalo—mu chikhulupiriro chosadziwa cha '*vagina dentata*' (Chilatini cha nyini ya mano). Sezin Koehler, wolemba mabuku ndi wofufuza chikhalidwe wosavomerezeka, anafotokoza kuti nkhani za nthano ya vagina dentata zilipo pafupifupi mu chikhalidwe chilichonse. "Mantha a amuna okhudza kudulidwa (*castration*) (omwe ali) ophatikizidwa ndi chikhulupiriro cholowa cha chikhalidwe cha ufulu wa kugonana amagwira ntchito ngati mizati yoyambira ya umuna, ndipo maulamuliro a amuna amayankha mwa kuyesa kulamulira 'kugonana kowopsa' ndi matupi a amayi" – iye akulemba. Chodabwitsa, ngakhale (kapena – tiyenera kunena - ngakhale aliyense asanawonedwe ngati wasayansi) Freud ankakhulupirira mwamphamvu kuti mantha awa ndi zotsatira zake – "nkhawa ya kudulidwa" - zinapanga osati kugonana kwa amuna kokha komanso kugonana kwa amayi omwe, iye anatsutsa, amadyedwa ndi 'nsanje ya mbolo' (*penis envy*).

Kunyozeza kapena ngale kusonyeza ngati chiwanda chiwalo cha thupi chinachake, kuchiphatikiza mu ndale, kapena kuchichotsa ku makhalidwe oloedwa okhawa, kungawoneke ngati kopusa mu zenizeni za lero, koma kukadalipo. Chinanso – modabwitsa - sichimasiyana kwambiri ndi kupusa kwake kuchokera ku lingaliro la vagina dentata. Kuphatikiza apo, chitsanzo chochititsa chidwi cha kutsutsidwa poyera kotere chinachitika osati kutali kwambiri ndi nyumba yanga ku Warsaw, likulu la dziko la demokalase, lomwe ndi Poland. Osatchula kuti zochitika zonse zinachitika mu nkhani ya luso, mu bwalo la zisudzo (*theatre*), makamaka mu *foyer* ya Dramatic Theatre, yomwe ili mu nyumba yodziwika kwambiri ku Warsaw—Palace of Culture and Science—chizindikiro cha mphamvu ya socialist ndi kunyada kwa People's Republic of Poland.

Pa nthawi yomwe Monika Strzępka anali kukhala mkulu wa bwalo la zisudzo (n'kofunika kudziwa kuti ndiye mkazi woyamba kukhala ndi udindowu!) wojambula Iwona Demko anapanga choikapo chagolide chonyezimira chomwe



chinali mu *foyer* ya zisudzo, chotchedwa ‘Wilgotna Pani’—‘Mayi Wonyowa’—kuti awonetse mphamvu ndi zotsatira za amayi, zonse kukongola ndi kusawoneka kwawo mu gulu la anthu.

Ndisanapitilize, nayi mawu oyamba ochepa kwa ojambula awiriwa: Strzępka wakhala akuzikidwa mu zochitika zoposa zaka makumi awiri za luso pamodzi ndi maphunziro a malingaliro okhudzana ndi – monga akulemba - kuwulula kwa "njira za ulamuliro, mphamvu ndi chiwawa mu zisudzo za ku Poland poganizira kawonedwe ka wotsogolera wamkazi". Demko, wobadwa – monga amakondera kuwonetsa - pa tsiku la chikumbutso cha makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu ndi chimodzi (66th) la kupezeka kwa *Venus of Willendorf* - ndi pulofesa ku Academy of Fine Arts ku Krakow ndipo amadzitcha "wojambula wa nyini" (*vagina artist*). "Ndinkafuna kuti amayi azikonda gawo ili la thupi ndikuyamba kuganiza zabwino za ilo," anatero Demko za ntchito zaluso yopangidwira bwalo la zisudzo. Ndiye chifukwa chake ankafuna kuti nyini ikhale yokongola, yokondweretsa, yowala ndi *sequins* ndi mikanda, zozikongoletsera ndi zinthu zofewa, kuti akumbukire dziko la chisangalalo, kutsekemera ndi zokondweretsa.

Komabe, kawonedwe kameneka kakanalandiridwa mwachangu ndi ndale zambiri za PiS (Law and Justice - chipani chomwe chikulamulira ku Poland), pakati pawo Konstanty Radziwiłł, yemwe panthawiyo anali bwanamkubwa wa chigawo chomwe Warsaw ili. Iye ananena kuti Strzępka mwiniwakeyo anagwiritsa ntchito udindo wake watsopano kulimbikitsa ufulu wa LGBT ndi "feminism yamphamvu yomwe imanyoza ulemu wa amayi", yomwe chizindikiro chake chapamwamba, chochititsa manyazi kwambiri chingakhale – malinga ndi iye - ntchito zaluso ya golide yooneka ngati *almond*. Radziwiłł anatsutsa kuti chibolibolicho, "chimachepetsa amayi mwa kuchepetsa ukazi kukhala mbali chabe ya thupi yomwe imathera ku kukwaniritsa zosowa za kugonana". Pamodzi ndi bungwe lalamulo la ku Poland losunga miyambo kwambiri – Ordo Iuris - iwo adalengeza kuti kafukufuku wokhudza "kuphwanya malingaliro achipembedzo ndi kuwonetsedwa kwa zolaula" ayenera kuchitika, ndipo wotsogolera wamkazi watsopanoyo achotsedwe.

"Anthu ambiri amasiku ano amawona kulambira mbolo ngati chodziwikiratu – tonse tamvapo, masamba masauzande ambiri alembedwa za izo. Nthawi zonse ndakhala ndikuchita chidwi ndi kulambira nyini ndipo sindinathe kuvomereza kuti ziwalo za amayi sizinafike poyamikiridwa" – akulemba Demko m'nkhani yake "Respect the Vagina" (Lemekezani Nyini). M'mafunso okhudza momwe anachitira chidwi ndi nyini, iye akuti: "Ndinazindikira kuti ndinkakhala wosamasuka kutchula mawu akuti 'nyini' mokweza pagulu. Ndinali ndi manyazi. Ndinali kudabwa kuti zikugwirizana ndi chiyani. Chifukwa chiyani izi zikuchitika? Kodi zimachokera



kuti? Kenako ndinawona kuti amuna ali ndi kumasuka kwambiri ku thupi, ndipo amayi mocheperapo".

Ino ndi nthawi yoti tiwunikire mfundo yakuti siziri "chabe" nyini zomwe ine ndi amayi ena ambiri tili nazo chidwi – koma kufunikira kosintha malingaliro okhudza ukazi wamphamvu ndi wowona womwe osavulazidwanso ndi mantha okhazikitsidwa kwa nthawi yayitali a thupi la amayi "la chiwanda". M'malingaliro anga, zonse zomwe Demko anachita, munjira zaluso kwambiri, yachikondi, inali kutikumbutsa kuti amayi ali ndi ndipo kwenikweni ali matupi omwe amafunikira miyambo, chisangalalo choyera ndi ubale wa amayi (*sisterhood*) kuti awathandize kukhala odziwa mphamvu zawo zokhudzana ndi thupi.

### **Madzi opatulika, thupi ndi ubale wa amayi (Sisterhood)**

"Leka ndikuuze nkhani" – ndi mawu awa kumayamba filimu ya "Sacred Water" (Madzi Opatulika), yotsogoleredwa ndi Olivier Jourdans. Mawu odekha mu chilankhulo chokopa cha Kinyarwanda amafotokoza nkhaniyo motere: "Kuchokera m'malo obisika kwambiri, tsiku lina dzuwa likutuluka, mfumukazi ina yanika mphasa yake yomwe inali yonyowa kuchokera usiku. Kugunda pansi, madontho anapanga kamtsinje, komwe kanapanga mtsinje waling'ono. Mtsinje waling'onowo unasintha kukhala waukulu ndipo potsiriza unapanga nyanja, Lake Kivu. Masiku ano amuna amapitiriza kuyandama pa nyanja, usana ndi usiku, kufunafuna gwero la moyo".

N'zochititsa chidwi momwe mu nkhanayi, kayendedwe ka chilengedwe, malo ndi zokhumba za amayi zimaphatikizana—pamodzi ndi ubale wofanana wa zochitika zakale, zamakono ndi zamtsogolo. Maubwenzi ofanana angawonedwe m'njira yomwe kunyaza – kutulutsa madzi achikazi ndi chisangalalo cha pachimake - kumawonedwa ndi amayi ndi amuna onse: monga kunyada ndi ulemu, zomwe zimabweretsa kukhutira ndi kuyanjanitsa pakati pa anthu awiri. Mu filimuyi (*documentary*), amuna akugawana maganizo awo pa nkhanayi: "iwo [amayi] amatulutsa maganizo awo" ndipo "kupanga chikondi kuli ngati kusewera mpira. Muyenera kusewera mwachilungamo kuti nonse muthe goleyi". Wina akuwonjezera osati popanda kunyada: "chonde, auzeni Azungu kuti nawo ayenera kufunafuna izi".

Vestine Dusabe, woulutsa wailesi ndi mphunzitsi wa kugonana yemwe ali ndi cholinga cholimbikitsa ndi kusunga chikhaliidwe cha Rwanda cha chisangalalo cha amayi, nthawi zonse amaulutsa pulogalamu yotchedwa *Happy couples*. "Mchitidwe



Ndinali ndi mwayi wolembedwa ntchito ngati mphunzitsi ku dome, kumene ndinkaphunzitsa akazi a ogwira ntchito m'migodi kuluka. Ngakhale sindinali ndi maphunziro apamwamba, Mayi Anielewicz, yemwe ndinapitiriza kupangira majezi banja lake, anali atandivomereza kwa manejala wa mgodi, mmodzi wa makasitomala ake anthawi zonse. Nolani anali wokoma mtima kuwonjezera kalata yotsimikizira khalidwe kuchokera kwa mwamuna wake. Wake anali mmodzi wa ochepa omwe sanali pa shift usiku woopsawo.

Ndinalembetsa Maria ngati wodalira wanga. Anapitiliza ku sukulu ya pulaimale ya mgodi kumene anachita bwino kwambiri, ndipo anapita ku Mpelembe Secondary School, yosungidwira ana asukulu opambana kuchokera ku masukulu onse a migodi ya Copperbelt. Atatuluka ngati wophunzira wabwino kwambiri pa giredi 12, Maria anakhala mmodzi wa anthu omwe ZCCM inathandizira kukaphunzira ku United Kingdom. Sanabwererense ku Zambia chifukwa anagwa m'chikondi ndikukwatiwa ndi mwamuna wa ku Britain.



Ndi nthawi yokwera ndege tsopano, koma ndikufuna kugula buku lina limodzi, kudya scone ina imodzi. Komabe ndi zovuta kwambiri kuyimirira ndikuyenda mozungulira. Ndipo kuli kotentha. Ndikumva kutopa. Nthawi iliyonse ndikawerenga mabuku achikondi amenewo, ndi Chizu ndi ine m'amasamba amenewo kachiwiri. Ndi njira yanga yolirira. Ndimadabwa kuti angakhale kuti tsopano.

Pamene mwamuna wanga anamwalira, ndinamvadi kuti ndinamupha ndi maganizo. Bwanji ndikanapanda kupanga pempho lija, kodi akanakhalabe pano? Pamene Maria anachoka, ndinaganiza kuti chinthu chimodzi chabwino chingatsutsane ndi choipa. Koma pamene anapita, mtima wanga unayamba kugwera mu dzenje lakuda kachiwiri, ndipo ndinaganiza, mwina, mwina chabe, mu Usisitere (Sisterhood), ndingapeze mtundu wina wa kulapa.

Kulumikiza lamba wanga ndi kuyang'ana pawindo, ndikukumbukira mbalame zosokonezeka zija zam'mawa. Koma nthawi ino ndikuziwona zikuwuluka mu mzere wowongoka, kulemba chinachake mwaudongo mumlengalenga.

"Maria Woyera, Amayi a Mulungu, tipempherere ife ochimwa tsopano ndi pa ola la kufa kwathu. Amen."



Suzyika Nymbili

## **MALO A SEWERO NGATI NJIRA YOSUNGIRA ZIKUMBUKIRO**

**Zidziwitso kuchokera ku Zambia ndi Hungary**

**Kukumana ndi chinthu mu mdima kungakhale chipwirikiti.**

### **MAWU OYAMBA**

Olemba masewero ndi opanga zisudzo amakhala ndi cholinga chopanga ziwonetsero zomwe zimamveka ndi kugwirizana ndi omvera osiyanasiyana. Kuti apange ziwonetsero zotere, ndikofunikira kudziwonetsera nokha ku ziwonetsero m'malo osiyanasiyana, kupitilira malo omwe munthu watsekerezedwamo kapena dera lake. Mu zomwe ndakumana nazo popanga zisudzo, ndayamikira kuti ngakhale pali kusiyana kwa zochitika ndi malo omwe opanga zisudzo amagwirira ntchito, iwo ali olumikizidwa kudzera mu luso la kusimba nkhani. Ngakhale pali malire omangidwa, makoma, ndi zolepheretsa zomwe zilipo, pali kuyandikira kwakukulu ndi kupadera mu zomwe timapanga: sewero (theatre).

M'kuyanjana kwanga ndi opanga zisudzo m'malo osiyanasiyana, kaya ku Lusaka kapena Harare, Vienna kapena Budapest, Austin kapena Atlanta, pa intaneti kapena pamaso ndi pamaso, pali zambiri zomwe zimalumikiza opanga zisudzo: chilakolako ndi chidwi cha kusimba nkhani kudzera mu sewero. Kuitana kwa kumasula ntchito ya opanga luso (deconfining), kuphatikizapo opanga zisudzo, chifukwa chake, ndi kuitana komwe kuli pamtima pa ntchito ya opanga luso. Opanga luso sanapangidwe kuti atsekerezedwe pokhapokha ngati ili mbali ya cholinga chawo cholenga. "Bwalo la zisudzo" (The theatre), monga malo ochitira ziwonetsero, ndi "sewero" (theatre) monga chiwonetsero, sizimangobweretsa ochita sewero ndi omvera pamodzi, koma sewero ndi chilankhulo chomwe chili ndi kuthekera komanga milatho pakati pa mipata yomwe ilipo pakati pa malo osiyanasiyana ndikutikumbutsa za kuyandikira kwathu.

M'pepala ili, ndikugawana zomwe ndakumana nazo ndi kumvetsetsa kwanga kwa kuyandikira ndi kulumikizana kudzera mu sewero. Pogwiritsa ntchito zitsanzo za masewero awiri a pa siteji kuchokera ku Hungary ndi Zambia, ndikutsutsa kuti sewero, lomwe lafotokozedwa m'pepala ili ngati "chilichonse chochitidwa ndi anthu amoyo chomwe chimaphatikizapo chilankhulo pamaso pa omvera amoyo", ndi njira yosungira zikumbukiro (medium of memory) ndipo ndi chida chofunikira pomasulira ndi kufufuza zikumbukiro. Masewero awiri omwe akukambidwa m'pepala ili, Lenshina: The Bloody Truth, kulenga kwanga, ndi Ghetto Sheriff, kulenga kwa ojambula a zisudzo ku Budapest, Hungary, amapereka zidziwitso za kumasula kumasulira kwa ziwonetsero za sewero ndi momwe sewero lilili njira yosungira zikumbukiro yomwe imagwira ntchito ku Africa ndi Europe ndi malo



ena. Monga wopanga zisudzo wochita chidwi kupanga masewero a zikumbukiro (memory plays), ndimaona sewero kukhala njira yosungira zikumbukiro pamene likugwiritsidwa ntchito kudzutsa ndi kufunsa mafunso pa zikumbukiro ndi kukumbutsa anthu za m'mbuyomu. Kuphatikiza apo, masewero angagwiritsidwe ntchito ngati zolemba za tsogolo, motero, kuthandiza gulu la anthu kukumbukira.

Pepala ili likugwiritsa ntchito mlingo wa kasimbidwe ka nkhani wa Stuart Spencer kuti afotokoze zotsatira za sewero pa omvera zomwe zimatsimikizira kupadera kwa sewero pakudzutsa ndi kufunsa mafunso pa zikumbukiro. Spencer amanena kuti pamene mafilimu amadzutsa malingaliro ndi mtima nthawi yomweyo (kukhudza kwachindunji/kwamphamvu), ndipo zolemba (prose) zimakhala zolingalira ndi kusanthula, sewero limaphatikiza zotsatira za filimu ndi zolemba, kupangitsa kuti likhale loyenera kupereka uthenga kwa omvera.

Mu gawo lotsatira, ndidzakambirana lingaliro la kumvetsetsa ndi kukumana ndi sewero pogwiritsa ntchito zitsanzo ziwiri za masewero a pa siteji, Lenshina: *The Bloody Truth*, ndi *Ghetto Sheriff*. Potsatira kukambirana kwa masewero awiriwa, ndidzabweretsa mlingo wa kasimbidwe ka nkhani wa Spencer ndi malo a sewero ndisanapereke mawu omaliza.

### **KUKUMANA NAZO NDI KUMVETSETSA KERA MU SEWERO**

Masewero awiriwa, Lenshina: *The Bloody Truth* ndi *Ghetto Sheriff*, ndi masewero omwe ndakumana nawo ndipo ndikuwona kuti ndi oyenera kugwiritsidwa ntchito muzokambiranazi. Monga wolemba masewero, ndimadziwa nthawi zonse kuti kusewera (*performance*) si lingaliro chabe lomwe limathera pa siteji kapena mu sewero, m'malo mwake limapitilira m'miyoyo ya tsiku ndi tsiku ya anthu. Chidziwitso ichi chimandithandiza kuphunzira kuchokera ku zochitika za tsiku ndi tsiku zomwe anthu sangaziwone ngati zochita zosewera. Zochitika za tsiku ndi tsiku zotere zingaphatikizapo momwe munthu amayendera, momwe andale amalankhulira ndi ovota, ndi momwe mwamuna wa ku Zambia amakhulira pamaso pa apongozi ake. Imodzi mwa mizere yotchuka kwambiri ya Shakespeare ndi "Dziko lonse ndi siteji, ndipo amuna ndi akazi onse ndi osewera chabe" (*All the world's a stage, And all the men and women merely players*) kuchokera mu sewero la *As You Like It*. Ngakhale ndi "mzere chabe" mu sewero, uli ndi tanthauzo pakumvetsetsa zomwe zikuchitika potizungulira. Mawuwa ndi chikumbutso cha chikhalidwe chokhazikika cha kusewera kwa anthu. Kaya mu sewero kapena ayi, pali mlingo wa kusewera (performativity) mu zomwe anthu amachita, ndipo monga taonera ndi Shakespeare, tonse ndife osewera pa moyo wathu wonse. Kukhala pa siteji kapena mu sewero, ndi kukulitsa kwa chikhalidwe chosewera ichi cha gulu la anthu, chomwe chimalungamitsa mtsutso woti titha kuphunzira zambiri kuchokera ku ziwonetsero za zisudzo. Ndikuyamba zokambirana ndi sewero lomwe ndinalamba ndikuchita nawo, *Lenshina: The Bloody Truth*.



### “Lenshina: The Bloody Truth”

Popeza mbiri yakale (*history*) ndi njira yokumbukira, masewero a mbiri yakale ndi njira yokumbukira zakale ndipo, chifukwa chake, ndi gawo la zikumbukiro. Sewero la *Lenshina: The Bloody Truth* lachitidwa katatu ku Zambia. Mtundu woyamba wa seweroli, womwe unachitika pa September 27, 2016, unali ndi mutu wakuti *Lenshina: The Uprising* (Lenshina: Kuwukira). Mu 2017, seweroli linasinthidwa dzina kukhala *Lenshina: The Bloody Truth* (Lenshina: Chowonadi Chamagazi), chifukwa "Kuwukira" (*The Uprising*) kunatanthauza mwanjira ina kuti Mpingo wa Lumpa unali utawukira boma ndipo, chifukwa chake, "unayenera" zomwe zinawachitikira. Kugwiritsa ntchito mawu akuti "Kuwukira" kunagwirizana ndi zikumbukiro zokhazikitsidwa ndi boma za mkanganowo. Kupatula kusintha kwa mutu, seweroli linawonjezera kutalika kwake ndi mphindi makumi awiri ndikupereka maziko ambiri a mkanganowo. Seweroli likuyesa kufotokoza nkhani ya mkangano pakati pa Mpingo wa Lumpa wa eni nthaka a mu Africa ndi boma la atsamunda logwira ntchito limodzi ndi chipani cha *nationalist*, United National Independence Party (UNIP), Zambia isanalandire ufulu mu 1964. Mkanganowo ukukhulupiririka kuti unachititsa imfa za anthu opitilira 1,000, pomwe ambiri adakakamizika kuthawa nyumba zawo.

Mpaka pano pali kumasulira kosiyana kwa zomwe Mpingo wa Lumpa unkayimira ndi zomwe zinachititsa imfa za anthu ambiri chifukwa cha mkanganowo. Pali mbiri yodziwika yotsatira komiti yofufuza zomwe zinayambitsa mkanganowo, yomwe imanena kuti mkanganowo unabuka chifukwa cha kufunikira kwa boma kuletsa kuwukira ulamuliro komwe kungayambire kumayambiriro kwa zaka za m'ma 1950. Kumasulira kwa mkangano uwu ndi zikumbukiro pambuyo pa 1991 kunatuluka komwe kumawona zipolowe za Lumpa za 1964 ngati kupha anthu ambiri (*massacre*) m'malo mwa kuwukira ulamuliro (*rebellion*). Kumasulira kumeneku kwa pambuyo pa 1991 kunatuluka pambuyo poti boma latsopano lokonda ufulu wa msika (*neo-liberal*) linayamba kulamulira, mamembala a Mpingo wa Lumpa omwe anali ku ukapolo anayamba kubwerera ku Zambia, ndipo mwayi wotseguka wopeza chidziwitso ndi ufulu wa kulankhula unakhalapo. Komabe, nkhani yakale ya Mpingo wa Lumpa wopatuka imapitilira ngati chikumbukiro cha gulu (*collective memory*).

Sewero la *Lenshina: The Bloody Truth*, linagwiritsa ntchito zisudzo kupanga zokambirana ndi mikangano, ndi kufunsa mafunso pa chikumbukiro cha gululi. Seweroli likuyesa kumanganso chikumbukiro cha zipolowe za Lumpa za 1964. Kupatula kugwiritsa ntchito sewero kumanganso zakale, lingagwiritsidwe ntchito kukonza zochitika zamakono kuti zimange zikumbukiro zolunjika ku tsogolo. Chifukwa chake, kufunikira kwa kumanganso zikumbukiro sikuthera pa kungokumbutsa anthu za zomwe zinachitika kale komanso kumaphatikizapo



kufunikira kofuna tsogolo losiyana, kutengera nkhaniyo ndi kufunikira kochita zomwe ziyenera kuchitidwa.

Sewero la *Lenshina: The Bloody Truth*, limagwiritsa ntchito zisudzo kuwunikira njira zosiyanasiyana zomwe anthu amakumbukira mkanganowo ndi chifukwa chake umakumbukiridwa choncho. Monga chidutsa cha sewero la mbiri yakale ndi zikumbukiro, limagawana zonse ziwiri: nkhani ya mbiri yakale yodziwika ndi malingaliro a pambuyo pa 1991 omwe amatsutsana ndi nkhani ya mbiri yakale yodziwika ya mkanganowo. Cholinga ndi kulola omvera kulandira mikangano kuchokera mbali zonse ziwiri kuti atsutse chikumbukiro chawo cha zomwe zinachititsa imfa za anthu panthawi yomwe imatchedwa "zipolowe za Lumpa".

Popeza chikumbukiro, ngati lingaliro, chingatanthauze momwe chinthu chimakumbukiridwa, sewero lingakhale njira yokumbukira. Monga anthu payekha, madera ndi magulu a anthu amakumbukira, zomwe zimaperekedwa za m'mbuyomu si zolembe zolondola za m'mbuyomu koma zimakhala ngati kuwerenga ndi kumasulira kosalekeza. Chifukwa chake, sewero lingakhale chida chomwe chingagwiritsidwe ntchito kumasulira chikumbukiro. *Lenshina: The Bloody Truth* imafunsa mafunso pa nkhani yomwe ilipo yokhudza funso la ndani anali mamembala a Mpingo wa Lumpa, ndi momwe ankakhalira. Seweroli likuyesa kubweretsa pachithunzi kawonedwe koonzededwa ndipo, motero, likuyesa kupanga chikumbukiro chatsopano mwa kufunsa mafunso pa chikumbukiro chokhazikitsidwa ndi boma.

Popeza mbiri yakale, monga chikumbukiro, singatengedwe ngati zochitika zosalakwa zopanga zolembe za m'mbuyomu, imafuna kumasulira. Kuphatikiza apo, mbiri yakale simangodutsa mu kumasulira, komanso imadutsa mu kusankha ndi ngale kupotoza. Nkhani ya zipolowe za Lumpa ili ndi kupotoza komwe kulipo mpaka pano, ndipo sewero ndi kusewera kungathe kutenga gawo pafunsa mafunso pa nkhani zomwe zilipo mwa kugawana mawu a iwo omwe sakuyimiridwa mokwanira kapena kumveka. Mogwirizana ndi mtsutso wa Burke woti kupanga zikumbukiro kumadutsa mu kumasulira, kusankha, ndi kupotoza, Carlson amatsutsa kuti chikumbukiro cha chikhalidwe, monga chikumbukiro cha anthu payekha, chimakhalanso panso pa kusintha kosalekeza pamene chikumbukiro chimakumbukiridwa mu zochitika zatsopano.

### “Ghetto Sheriff”

Ndinawonera sewero la *Ghetto Sheriff* ku Budapest, Hungary mu 2019. Seweroli linali la mphindi makumi asanu ndi atatu ndipo linachitikira mu mdima wotheratu. Nthawi zonse ndikamafotokoza zochitika izi, ndimawonetsa kuti "sindinawonere" seweroli, koma kuti ndinakumana nalo (*experienced it*). Sewero lonse linachitidwa mu mdima wotheratu. Tsamba la pa intaneti komwe seweroli



linalengezedwa linaika funso ndi yankho: "Kodi tingalankhule bwanji za zoopsa zazikulu kwambiri za zaka za m'ma 20th century, *Holocaust* (kupha kwa nkha za Ayuda)? Malinga ndi wotsogolera wotchuka, János Mohácsi ndi ophunzira ake akale, tikhoza kutero mothandizidwa ndi nthabwala ndi nyimbo za Chiyuda, zikalata zochokera m'zaka za m'ma 30s ndi 40s, ndi kuzilankhula—mu mdima wandiweyani." Kufotokozera kumeneku kumapatsa owerenga chithunzi cha zomwe seweroli likunena, ndi njira zosiyanasiyana zomwe zimagwiritsidwa ntchito popanga seweroli kuphatikizapo mdima.

Malemba omwe anagwiritsidwa ntchito mu seweroli anali ozikidwa makamaka pa zikumbukiro zaumwini, zomwe zinasankhidwa ndi wotsogolera János Mohácsi ndi ochita sewero. Kuti aphetikize seweroli, malemba ochokera mu filimu ya *Shoah* yolembedwa ndi Claude Lanzmann ndi magwero ena monga "maphunziro a nkhani, umboni wa opulumuka, zolemba zopeka, zolemba za dayale, magwero a mbiri yakale, malipoti aboma ndi zosonkhanitsa zaumwini zokumbutsa nthawi ya mbiri yakale ndi malingaliro a nthawiyo" zinagwiritsidwa ntchito. Zitsanzo za magwero awa ndi mitundu ya njira zosungira zikumbukiro zomwe zimagwiritsidwa ntchito kupanga sewero. Popeza seweroli lapangidwa kukhala chiwonetsero cha zisudzo, seweroli limayimirira ngati kulenga kodziyimira pawokha ndipo limakhala njira yosungira zikumbukiro (*medium of memory*).

Kupatula njira zosiyanasiyana zomwe zinagwiritsidwa ntchito mu *Ghetto Sheriff*, monga nyimbo ndi ntchito zolembedwa, mdima wandiweyani unagwiritsidwa ntchito ngati gawo lofunikira popereka seweroli. Funso limatsala lofuna kudziwa kuti ndi uthenga wanji womwe umaperekedwa pamene sewero lachitidwa mu mdima wotheratu pamene likulankhula za *Holocaust*. Sewero mu mdima lingatanthauze mdima ndi chisoni cha *Holocaust*. Pankhaniyi, njira yomwe yagwiritsidwa ntchito, mdima, ikhoza kukhala gawo la uthenga, zomwe zimagwirizana ndi mawu a Marshall McLuhan akuti "njira ndiyo uthenga" (*the medium is the message*). Wolemba sewero anasankha kuti lichitidwe mu mdima pazifukwa zina. Mdimawo ndi uthenga kapena gawo la uthenga wonse wa seweroli. Zingatsutsidwe kuti mdima mu *Ghetto Sheriff* unali wofuna kuwonetsa zaka zamdima za *Holocaust*. Nthawi ya imfa, ululu, ndi chisoni.

Kuphatikiza apo, mphindi makumi asanu ndi atatu za mdima ndi kumva zokambirana za *Holocaust* zimagwiritsidwa ntchito mu seweroli ngati njira yopangitsa omvera kutchera khutu kwambiri ku zomwe akumva osati zomwe akuwona pa siteji. Mamembala a omvera amapanga zithunzi zawozawo mu mdima, mosiyana ndi masewero kapena mafilimu omwe amapanga zithunzi kwa omvera. M'malo moyang'ana pa kupambana kwa ochita sewero ndi kuyenera kwawo kuwomberedwa m'manja, mdimawo umathandiza omvera kuyang'ana kwambiri pa nkhani yomwe ikukambidwa. Izi sizikutanthauza kuti ochita sewero sanali opambana, komabe, mutu wa seweroli ndi malangizo a mlengi zinayang'ana kwambiri pa uthenga wa seweroli, kusiya wina aliyense mu "mdima".



Kukumana ndi chinthu mu mdima kungakhale chipwirikiti. Nthawi ina ndinadya mu mdima wotheratu pa lesitilanti ndipo odyana ena anachoka chifukwa cha chisokonezo chomwe chinabuka. Ngakhale panali chisokonezo mu lesitilanti, phokoso, ndi kusadziwa zomwe zinali pa mbale yanga ndi komwe galasi langa la madzi linali, ndinali ndi zokambirana zabwino ndi mlendo yemwe ndinakhala naye pafupi. Ndi njira yoyenera, zochitika za mdima zingakhale zopindulitsa. Mosiyana ndi chisokonezo mu nkhani ya chakudya chamadzulo mu mdima, malo a zisudzo ndi *Ghetto Sheriff* anathandiza omvera kuyang'ana kwambiri. Sitinafunikire kuchita zambiri, kupatula kukhala pansi ndikumvetsera. Monga membala wa omvera, ndinakumana ndi seweroli ngati munthu payekha popanda kuyang'ana kwambiri pa zochitika za gulu. Ngakhale ndimatha kuzindikira momwe anzanga opezeka nawo kusewero ankamvera panthawi yachiwonetsero, zochitika zambiri za gulu zinabwera pambuyo pa seweroli pamene tinkatuluka. Kupanda kutero, tinakhala pansi ndikutsatira kusewera kulikonse kumene mawu a ochita sewero ankachokera. Ndawonerapo masewero ambiri a pa siteji. Chodabwitsa, limodzi mwa masewero osaiwalika ndi lomwe sindina "wonere" *Ghetto Sheriff*. Pambuyo pa seweroli, ndinali ndi macheza ndi mmodzi wa ochita sewero, kuti ndiphunzire zambiri za zomwe adakumana nazo. Izi zinandipatsa chidziwitso chochuluka pa njira yawo yopangira zisudzo ndipo chinali chikumbutso china cha chikhalidwe chosatsekerezedwa cha ntchito yomwe timachita: kupanga zisudzo. Nditayang'ana masewero awiriwa paokha, tsopano ndidzabweretsa mlingo wa kasimbidwe ka nkhani wa Spencer ndikukambirana masewero awiriwa ndikuyang'ana pa sewero ndi zikumbukiro.

### **SEWERO, CHIKUMBUKIRO NDI MLINGO WA KASIMBIDWE KA NKHANI WA SPENCER**

Kaya lachitidwa mkati mwa holo kapena lolengedwa pamalo otseguka, ndi *script* kapena popanda, ku Budapest kapena ku Lusaka, changu (*immediacy*) cha sewero malinga ndi momwe limakhudzira omvera limapangitsa kuti likhale lofunikira pazokambirana zathu za sewero ngati njira yosungira zikumbukiro yogwira mtima. Polemba za sewero, Carlson amatsutsa kuti sewero ndi nkhekhe ya chikumbukiro cha chikhalidwe yomwe imapatsa gulu la anthu "zolemba zogwirika kwambiri za kuyesa kwake kumvetsetsa momwe limagwirira ntchito." Kutengera mtsutso wa Carlson, kuwonera ndi kuchita nawo masewero kungakhale njira yophunzirira zambiri za gulu la anthu, mantha ake, zovuta zake, ndi zokhumba zake pakati pa zinthu zina. Njira imeneyi siimathera pa chiwonetsero chokha, njira yolemba, kuyeserera (rehearsal), kutsatsa malonda, ndi zokambirana pambuyo pa sewero ndi mbali ya njira yayikulu yopangira masewero ndi zochitika. Kwa masewero ena, monga *Lenshina: The Bloody Truth* ndi *Ghetto Sheriff*, cholinga sikingokumbukira komanso kulankhula ndi nthawi yomwe ilipo. Masewero otere



amakhudzanso tsogolo chifukwa amawunikira zolakwika za m'mbuyomu ndichiyembekezo kuti zolakwika zotere zidzapewedwa m'tsogolo.

Popanga kachidutswa ka sewero, makamaka ntchito ya zisudzo yomwe si yopeka (*nonfictional*), nthawi yochulukira imatengedwa kuyang'ana njira zosiyanasiyana. Ntchito zolembedwa, mavidyo, zithunzi, ndi zina zotero zimathandiza kupanga nkhaniyo ndikuwonetsetsa kuti nkhani yolondola ikuwonetsedwa. Mu chiwonetsero chenichenicho, kupatula kuwona ochita sewero pa siteji, njira zosiyanasiyana monga kanema, kuyatsa, phokoso, ndi mapangidwe a siteji zingagwiritsidwe ntchito kupereka uthenga. Pankhani ya *Ghetto Sheriff*, wolembe sewero amagwiritsa ntchito mdima ngati njira. Njira zosiyanasiyana zomwe zimagwiritsidwa ntchito popereka uthenga zimathandiza omvera kumvetsetsa uthenga womwe wafunidwa, ngakhale kuti angakhaleenso ndi kumasulira kwawoko.

Momwe siteji kapena malo a chiwonetsero amawonekera amapanga chithunzi cha zomwe seweroli likunena ndi omvera omwe akuwafuna. Uthenga wa luso lonse la pa sitejili ndi wofunikira; komabe, si uthenga wonse, popeza mamembala a omvera angamasulire uthenga wa seweroli mosiyana kutengera zomwe zikuchitika pa siteji nthawi zosiyanasiyana.

Monga momwe zasonyzedwera ndi Spencer, osati kokha kuti sewero lili ndi gawo lalikulu la zowoneka lomwe lili ndi zotsatira zachangu kwa omvera, lilinso ndi zotsatira za zolembe (*prose*); kulingalira ndi kusanthula, zinthu zomwe ndi zaumwini. Sewero lingasiyanitsidwe ndi mitundu ina ya luso chifukwa limakhudza omvera m'maganizo, m'munsi mwa chidziwitso, ndi mwanzeru munjira yachindunji. M'munsi muli mtundu wosinthidwa wa kufotokoza kwa Spencer kwa momwe sewero limagwirira ntchito poyerekeza ndi filimu ndi zolembe.

**FILIMU**

Yachangu  
Yokhudza mwachindunji

**SEWERO**

Yachangu  
Yolingalira  
Yokhudza mwachindunji  
Yosanthula

**ZOLEMBA/NKHANI**

Yolingalira  
Yosanthula

Chithunzi 1 – Kuyerekeza kwa Spencer kwa sewero ndi filimu ndi zolembe; Kusinthidwa kuchokera kwa Spencer, 2002.

Ngakhale *Ghetto Sheriff* sinali ndi zowoneka zilizonse kwakukulu, inali ndi zotsatira zachangu ndi zokhudza mwachindunji. Monga membala wa omvera, inandilola kukhala gawo la chikumbukiro chomwe sindinakumanepo nacho. Kulola mamembala a omvera kukhala gawo la chikumbukiro chomwe sanakumanepo nacho kumagwiranso ntchito ku *Lenshina: The Bloody Truth*. Kusiyanana kwake ndi kwakuti nkhani ya Mpingo wa Lumpa mu *Lenshina: The*



*Bloody Truth* libe nkhani yogwirizana ndipo ikadali yotsutsana. Pakadali kusagwirizana kwakukulu, monga momwe zikuwonekera kuchokera ku nkhani ya nyuzipepala yomwe imathirira ndemanga pa seweroli:

"Sewero la munthu wotsutsana ngati Lenshina (dzina loyambirira kukhala Regina) nthawi zonse lidzagawa maganizo a anthu, ndipo kumapeto kwa chiwonetsero Lachisanu, munatha kumva mamembala ena a omvera akufotokoza maganizo amphamvu mu foyer ndi zomwe ankaganiza kuti zinali zolakwika mu seweroli. Onse wolembe ndi wotsogolera ayenera kuti ankayembekezera izi; chikhalidwe cha nkhaniyi nthawi zonse chikanakopa kawonedwe kena."

Cholinga cha *Lenshina: The Bloody Truth* chinali, chifukwa chake, osati kutenga mbali, koma kulola omvera kukhala ndi zochitika za mikangano yosiyanasiyana, ndi kufunsa mafunso pa zomwe akhala akudziwa nthawi zonse ngati maloolondola pa zomwe zinachitika ndi Mpingo wa Lumpa.

Pamene sewero lachitidwa, wolembe sewero, wotsogolera, ndi ochita sewero si okhawa omwe amayang'anira kumasulira. Omvera ali ndi gawo pamasulidwe, powona kuti sewero ndi lamoyo, chinthu chomwe chimalola omvera kulingalira ndi kusanthula zinthu panthawiyo. Palibe mawu olamulira nkhani, m'malo mwake pali njira zosiyanasiyana zowonera zinthu. Pankhani ya Ghetto Sherriff, kugwiritsa ntchito mdima kunachepetsanso mphamvu ya zithunzi, chifukwa mamembala a omvera amagwiritsa ntchito kulingalira kwawo kwambiri. Ngakhale malingaliro a kusewera (*performative theories*) amakonda kuyang'ana kusewera kwa chikumbukiro ngati kusewera kwa moyo weniweni, monga kudzera munjira zochitira zinthu tsiku ndi tsiku osati kutenga mawonekedwe a chikumbukiro chochitidwa pa siteji mu sewero, ndikutsutsa kuti sewero ndi njira yabwino yothandizira kuyimiridwa kwa anthu mu chiwonetsero, ndi kuwapangitsa kufunsa mafunso pa njira zawo zoyembekezeredwa za kusewera m'gulu la anthu. Mwa kusewera m'gulu la anthu, ndikutanthauza njira za tsiku ndi tsiku za moyo. Ngati anthu angathe kufunsa mafunso pa njira zawo zoyembekezeredwa za kusewera kwa iwo okha, ndi za gulu la anthu, angathe kufunsa mafunso pa zikumbukiro chimodzimodzi.

Sewero limadziwika popereka kumasulira kwatsopano chifukwa lingagwiritse ntchito njira zosiyanasiyana kumasulira zakale ndi script kukhala malo oyamba a kumasulira. Pamene wolembe seweroamaliza script ndipo kuyeserera kumayamba, kuyeserera kumaphatikizidwa ndi kumasulira. Ngakhale n'kofunika kwambiri mu sewero, script imakhala yotseguka ku kusintha ndi kumasulira ndi ochita sewero ndi otsogolera, komabe, chilolezo cha wolembe sewero chimafunika. Ndongomeko ya kuyeserera imapatsa ochita sewero ndi wotsogolera mwayi wopanga chidutswa cha ntchito chomwe chingathe kutsutsa omvera omwe akuwafuna kuti akatuluka mu bwalo la zisudzo kapena malo a chiwonetsero, akhale ndi zochitika zomwe zimawalola kutsutsa malingaliro awo. Ndongomeko ya kuyeserera imasinthanso malingaliro a ochita sewero ndi wotsogolera. Mu ntchito



yanga ngati wopanga zisudzo, ndakakamizika kusintha mayendedwe a sewero nthawi zingapo kutsatira zokambirana ndi malingaliro omwe anagawanyidwa panthawi ya kuyeserera.

Pankhani ya sewero la Lenshina ndi Mpingo wa Lumpa, mkangano suli kokha pa momwe otsatira a Mpingo wa Lumpa amatchulidwira, komanso pa mfundo yakuti anthu opitilira 1000 anamwalira mu mkangano womwe unabuka mu 1964. Pakadalibe mafotokozedwe awiri ofanana a zomwe zinayambitsa zipolowezo. Pankhani ya *Ghetto Sherriff*, seweroli silikutsutsa nkhani yomwe ilipo kale ya Holocaust, m'malo mwake limayifotokoza kuchokera ku malingaliro osiyanasiyana pogwiritsa ntchito zochitika za opulumuka ndi njira yosiyana kwambiri: sewero mu mdima wandiweyani. Ngakhale zingakhale zovuta kulankhula, sewero, mu mdima, limapanga malo omwe nthawi yamdima m'mbiri ingakambidwe ndi kukumbukiridwa. Imodzi mwa nthabwala mu *Ghetto Sherriff* inali, "Kodi ana achiyuda amasewera bwanji hide and seek? Kulowa pakhomo, kutuluka pa chumuni." Ngakhale nthabwalayo ingamveke ngati "yopanda chifundo", ndi chikumbutso chowopsa cha *Holocaust*. Kuphatikiza apo, ikuwonetsa momwe nthabwala zingagwiritsidwire ntchito kuwunikira zikumbukiro zamdima. Nthabwala zinagwiritsidwa ntchito m'masewero onse awiri, ndipo panali nthawi zina pamene omvera anali kuseka, koma zikumbukiro zomwe zili mkati mwa masewero awiriwa sizimayenera kukhala zoseketsa. Ngakhale palibe chizindikiro chomveka bwino kuti masewero awiriwa anathandiza madera kukumbukira kapena kufunsa mafunso, kupitilira omwe adawonera masewero, zochitika zokhalapo m'masewero otere zimalola kukumbukira kwa gulu.

### MAWU OMALIZA

Masewero awiriwa, *Lenshina: The Bloody Truth* ndi *Ghetto Sherriff*, ngakhale kuti anaganiziridwa m'malo awiri osiyanasiyana, Zambia, ndi Hungary motsatana, amalankhula chilankhulo cha sewero ndi kusimba nkhani chomwe opanga zisudzo ndi omvera m'malo osiyanasiyana angadziwike nacho. Olenga a masewero a zikumbukiro awiriwa amagwiritsa ntchito sewero ngati njira yosungira zikumbukiro mwa kulankhula ndi mitu yomwe imadzutsa chikumbukiro. Masewerowa amaphatikiza njira zosiyanasiyana kuti apange njira imodzi (sewero) kudzutsa chikumbukiro komanso kufunsa mafunso pa chikumbukiro, monga momwe zilili ndi *Lenshina: The Uprising*. Izi zikuwonetsa kufanana mu momwe masewero a zisudzo amapangidwira. Muzochitika zonsezi, njira, yomwe ndi sewero, sikuti ndiyo uthenga, zomwe zili mkati mwa sewero, ngakhale zitakumana nazo mosiyana, ndizo uthenga. Malingaliro awa angathe, chifukwa chake, kugwiritsidwa ntchito mu nkhani za ku Africa (Zambia) ndi Europe (Hungary). Ndi chikumbutso cha kuyandikira kwa ojambula, omvera, ndi nkhani zomwezo,



ngakhale pali kusiyana komwe timakuwona chifukwa cha mtunda, malo, malire, ndi zoikamo zina zomwe zimatilekanitsa.

Kufanana mu malingaliro a zisudzo ndi uthenga wonse wa masewero kungakhale polowera pa kugwirizana popanga ntchito za zisudzo zomwe cholinga chake ndi kumasula malingaliro athu a dziko. Nditakumana ndi Lenshina: *The Bloody Truth ndi Ghetto Sherriff*, mapeto anga ndi akuti malingaliro m'masewero onse awiri a zikumbukiro angagawidwe mu nkhani ziwirizi chifukwa amalankhula ndi mitu yofanana ya kuponderereza ndi zoopsa (trauma).

### MNDANDANDA WA ZOLEMBA

Ajsi, T., *Footprints without Feet: Theatre as Recourse to Collective Memory in Kashmir. Research in Drama Education, The Journal of Applied Theatre and Performance*, 2023, nr 28, s. 414–427.

Burke, P., *History as Social Memory* [w:] *Memory: History, Culture, and the Mind*, red. T. Butler, Oxford 1989, s. 97–113.

Carlson, M., *The Haunted Stage: The Theatre as Memory Machine*. University of Michigan Press, 2003.

Erll, A., *Memory in Culture*, Londyn 2016.

Gordon, D. M., *Rebellion Or Massacre? The UNIP-Lumpa Conflict Revisited* [w:] *One Zambia, Many Histories*, red. J. Gewald, M. Hinfelaar, G. Macola, Boston 2008, s. 45–76.

Hutchison, Y. *South African Performance and Archives of Memory*, Manchester 2013.

Kachingwe, K., *Two Historical Plays in Town*, Zambia Daily Mail (blog), 7 kwietnia 2018 r. <http://www.daily-mail.co.zm/two-historical-plays-in-town/>.

Llewellyn, N. *Honour in Life, Death and in the Memory: Funeral Monuments in Early Modern England*, Transactions of the Royal Historical Society, 1996, nr 6, s. 179–200.

McLuhan, M., *Understanding Media: The Extensions of Man*, Nowy Jork 1964.

Nyimbili, S., *Lenshina: The Bloody Truth*, The Hub Theatre Zambia, 2016.

Plunka, G. A., *Holocaust Drama: Theater of Atrocity*, Cambridge 2009.

Shakespeare, W., *Jak wam się podoba*, tłum. Leon Ulrich [w:] *Dzieła dramatyczne Williama Shakespeare (Szekspira): wydanie ilustrowane ozdobione 545 drzeworytami*, tłum. Stanisław Koźmian, Józef Paszkowski, Leon Ulrich, z dodaniem życiorysu poety i objaśnień pod red. Józefa Ignacego Kraszewskiego, T. 3, Komedye, Spółka Wydawnicza Księgarzy, Warszawa 1877.

Spencer, S., *The Playwright's Guidebook: An Insightful Primer on the Art of Dramatic Writing*, Nowy Jork 2002.

Színház, Ö., „Ghetto Sheriff”, <https://www.orkenyszinhaz.hu/en/2012-09-17-12-53-31/repertoire?view=szinlap&id=1674>.

Violi, P., *Landscapes of Memory: Trauma, Space, History*, Bristol 2017.



Klara Wojtkowska

## **MOMWE NDINAPHUNZIRIRA KUPEMPHERA**

### **Mbiri yopeka za moyo wanga**

Mosiyana ndi abale anga anayi, ndinabadwa ndili mlendo (*immigrant*), mtundu wachilendo, mukudziwa. Ndinabadwira pakati pa mayiko, m'chibelekero cha adani a anthu anga, m'malo mwa kukhala m'malo awo othawirako. Ndinabadwira pakati pa Ajeremani, omwe nthawi ina anayesa kupha agogo anga a ku Poland. Ndinakhala kumeneko kwa milungu iwiri yokha, ndili pakati pa chikondi ndi mantha a makolo anga, ndikugona ndi kudyetsedwa ndikumwa nkhawa za banja langa la ku Poland, ndisanatengedwe kuoloka malire ena m'malo ozizira, amdima a bokosi la makatoni. Osadziwa, opanda thandizo, okutidwa, ndinatengedwa kupita ku dziko lina lomwe silinali langa. United States. Ndinabadwa nzika ya Poland, kwa makolo a ku Poland, komabe, kuyambira pachiyambi, zikuooneka kuti ndinalibe nyumba.

Alendo (*Immigrants*) amalankhula chilankhulo chimodzi. Timawerenga zizindikiro, kutola zilankhulo zingapo, kumva malo ndi mphamvu yachisanu ndi chimodzi, osati kuyesetsa kuti tikwanire, ayi, koma kuyenda pa chingwe chopyapyala chokhala iwe mwini ndi kukhala munthu. Kukhala iwe mwini - mlendo. Kukhala munthu watsopano - kukhala odziwika mokwanira ku malo omwe uli kuti akupatseni ulemu waumunthu womwe mukufunikira kuti mukhale ndi moyo.

Ife alendo timabwera m'maonekedwe ndi kukula kosiyanasiyana, zoono, koma sitimaganiza kuti tili kunyumba. Kutu malo omwe tili mwathupi ndi athu. Sitimatenga "kunyumba" mopepuka. M'malo mwake, timakufunafuna nthawi zonse, m'mphindi, m'zokoma, m'fungo, m'chilankhulo cha kubadwa kwathu. Tikudziwa kuti kunyumba ndi chinthu chovuta kupeza, ndipo izi zingatipangitse kukhala ndi mantha pang'ono (*paranoid*). Kuphatikiza apo, wailesi ndi nkhanu za anthu osamukira kumayiko ena zimabweretsa mtundu wina wa mantha, makamaka pamene chiwerengero cha osamuka chikuonjezeka chifukwa cha nkondo kapena njala.

Koma tikakhala omasuka ndi kumva kuti tili kunyumba, pamene mantha sakudya m'mphepete mwa maloto athu a nkhawa, ndiye kuti ndife anthu otseguka ndi ochezeka kwambiri omwe mungawapeze. Tili ndi diso ndi khutu lapadera lolandira wina aliyense. Tikudziwa kuti ndikofunikira. Sitikuopsezedwa nazo. Ndiye chifukwa chake, m'kufuula konse kwa nthawi ino, zithunzi zobwerezabwereza pa TV, mitu yankhani m'manyuzipepala ndi mau monga Osamuka! Othawa kwawo! Ofunafuna chitetezo! ndi zopusa zonsezo – ndimapitiriza kunena kuti alendo ndi



mphatso ya Mulungu ku fuko. Tikhoza kukhala mphatso yovuta, inde, koma mphatso ngakhale zili choncho.

Palibe amene angatumikire ngati mneneri ku fuko, kupatula uyo yemwe choyamba – ali ndi maso ndi makutu omwe amaona anthu kuchokera kunja, omwe ali ndi masomphenya apadera ndi kuoona zonse popanda khungu lomwe kukhala mkati kwambiri kumakupatsani. Ndipo kachiwiri, timakonda chikhalidwecho mokwanira kuti tichiphunzire, kuchimvetsetsa, kuiikamo ndalama. Ife alendo, kuposa wina aliyense, tikudziwa momwe tingakondwerere chikhalidwe chomwe chatipatsa nyumba. Chifukwa tapatsidwa nyumba ngati mphatso, osati kubadwiramo. Monga otembenuka kulikonse, tikadziwa kusiyana pakati pa kukhala ndi nyumba ndi kusakhala nayo. Timapereka zomwe tili nazo, chifukwa chimenecho ndi maziko a nyumba.

Nzosadabwitsa, chifukwa chake, kuti ndinamva kuti dziko la Zimbabwe ndilo nyumba yanga kuyambira nthawi yoyamba yomwe mapazi anga anakhudza nthaka yake. Zaka khumi zapitazo, pamene ndinadutsa m'dzikoli paulendo olumpha kuchoka basi kupita basi - kuchokera ku Bulawayo, kupita ku Victoria Falls, ku Harare, mpaka ku Maputo. Panthawiyo, ndinkaimbira gulu la *Diaspora* la ku Poland ku South Africa. Nyimbo za alendo, ndithudi! Kwa ine, Zimbabwe ndi Poland zinkamveka chimodzimidzi, mbalame zakuda zikuuluka mozungulira nyumba za mzinda za kalembedwe ka Soviet zinkalira mofanana mumlengalenga, dzuwa lam'mawa linkanunkhira chimodzimidzi, mitengo inkamwetulira ndikuponya manja a akorona awo obiriwira, kuno ndi uko mofanana.

Apa ndipamene ndinakumana ndi *mbira*, makiyi asiliva akunyezimira nyimbo zao mwachimwemwe, kudzutsa Makolo omwe ali m'tulo. Tili ndi miyambo za Makolo ku Poland komanso, ndinaganiza, pamene ndinkaphunzira nyimbo zanga zoyamba za *mbira*. Tili ndi nyimbo zomwe zimadzutsa Makolo, ndi zisudzo (masks) zomwe timavala tikamavina nao mu Mwambo – monga momwe ku Zimbabwe, timamenya zikopa za ngoma ndi makiyi a *mbira* ndikuvina kuvina kwakuthengo mpaka Makolo atafika.

Tsiku lomwe ndinafika, ndina pitaku msika ku Bulawayo. Pansi pa thambo la buluu Lowala, ndinayang'ana milu za *mopane worms* (ifishimu/ vikhubala) zouma, ndipo ndinalankhula ndi azimai ogulitsa pa za umoyo yao. Ankamwetulira kwambiri, kuseka kwambiri. Mitengo ndi mbalame zozungulira zinkaoneka ngati zikumwetulira ndi kuseka komanso. Chilengedwe chinkakonda anthu ake, ndipo anthu anakakonda chilengedwe. Ndinaona *mbira* kwa nthawi yoyamba. Inkaoneka yachilendo kwambiri, thabwa lokhala ndi makiyi – komabe nthawi yomweyo, inali yodziwika kwa ine. Ngati kuti ndinkaidziwa kuchokera ku umoyo wakale. Inakwana bwino ndi mofunda m'manja mwanga, monga kalimba kapena *violin*.

Ndinagwa m'chikondi ndi Zimbabwe, chifukwa ndimakonda Poland. Mayiko awiriwa ali ndi mzimu wabwino omwewo pamaziko awo - mzimu olemekeza ndi kukonda nkhalango ndi maphiri ndi madzi. Mzimu wolemekeza *ma*



*njuzu*(mermaids), omwe ali ochuluka ku Poland. Mzimu wa kusimba nkhanu ndi mafanizo ndi kufunikira kwa chilankhulo. Ndimakonda Poland, ndipo chifukwa chake ndidzakonda Zimbabwe nthawi zonse. Mayiko aya awiri ali ofanana ndipo ali pafipi ndi mtima wanga.

Sindinkadziwa panthawiyo, kuya kwake, kutali kwake, komwe miyeso ndi nthawi ndi malo izi zingapite. Kuti Makolo anga a ku Poland anali kundidikira ku Zimbabwe, limodzi ndi *njuzu* ndi mkango waukulu. Akuyembekezera kuti ndibwerere.

\*\*\*

WARSAWA, POLAND

ZAKA ZIWIRI M'MBUYOMO

Masiku a July ndi achilendo, ndikuganiza ndekha, ndikutulusa thukuta, pamene mapazi anga akuponda msewu mwamphamvu, ndipo ndikunyamula violin yanga, yomweikadali kuvutika kwa wokonzanso zida (*luthier*) ku Warszawa. Ndikukana kuitcha *War-saw* (Macheka a Nkhondo) – inde, taona nkondo, koma palibe chifukwa chogogomezera zoopsa zathu. Dzina la Warszawa limachokera ku Wars ndi Sawa, ndi chikondi pakati pa msodzi ndi *njuzu* chomwe chinabereka mzindawu.

Ndikudutsa munthu wachikulire, oswinyala ngati chinkhupule chouma, akuyimba *violin* pakona. Akuoneka osakhutira ekha, zala zake zikugwa mwamwayi pa manotsi opanda tanthauzo – kubwerera m'mbuyo, kubwereza manotsi omwewo. Kodi akuyeserera? Akuyesera kukumbukira? Ali kuti akatswiri a *violin* a lero? *Violin* yatchuka, kukhala chida choyimbidwa ndi anthu ngati osowa pokhala m'mbali mwa mtsinje wa Wisła. Chinkakhala chida chamwambo. Chinkadziwika kuti chimabweretsa mizimu... monga *mbira*. Ndikuzizira ndi njala, ndikuyang'ana ku *coffee shop*, ndikulowa m'matumba anga. Ndi kuwerenga *zlotys* makumi awiri.

Nditani?

Ndipite kuti?

Palibe chomwe chayenda bwino pamoyo wanga. Ndili ndi zaka makumi atatu. Ndiliba luso lililonse kupatula kuyimba *fiddle*; palibe ndalama, thupi losadziwika bwino kuti ndipite Kumadzulo kukagwira ntchito yamanja—mwina kuthyola *strawberries* kapena kusamalira okalamba. Chinachake mkati mwanga chikuyankha ku kumva koyipaku ndi chilakolako chofuna kufa chodziwika bwino. Mwina sindiyenera kukhala pano nkomwe? Sindikudziwa wina woti ndikhale. Akale anati tsogolo lathu linalembedwa mu nyenyezi. Nthawi zonse ndinkalingalira kuti lidzakhala lalikulu, lodabwitsa ndi lohandiza. Koma tanthauzo la moyo wanga lili kuti tsopano?

Ndikulowa mu *coffee shop* kukafunsa za ntchito. Kachiwiri.

Munthu wokhala ndi thaulo pamapewa ake akupukusa mutu, ndipo ndikumva minyewa m'mimba mwanga ikuwawa mosasangalatsa, kenako kukhala



yopanda kanthu ngati kuti chinjoka chachikulu changotenga kuluma kwakukulu kuchokera m'matumbo anga.

*Ma coffee shop* sakufunanso oimba *violin*.

Oimba violin ali paliponse masiku ano, ndipo palibe amene akudziwa cholinga chawo. Ndaphunzitsidwa nyimbo, inde, koma ndikulakalaka mphamvu yake.

Ndinaphunzitsidwa kuti nyimbo ndi chinthu chabwino, ndipo ngati uli wodziwa, ukhoza kupanga kukhala ntchito yako, ndikulipidwa ndalama ndi kukhala ndi moyo Ndinayimba m'miseu za Warsaw ndi Sweden ndi UK ndipo na Ireland konse, ndipo ndinasonkhanitsa ndalama mu bokosi la violin yanga; ndinaphunzira m'masukulu a nyimbo ndi kuchokera kwa aphunzitsi ndipo ndinaiimba 'Legend' ya Wieniawski pa maliro a mchimwene wanga ndi a azakhali anga. Ndinaphunzitsidwa kuti nyimbo inali yofunikira ndi yokongola mu chikhalidwe – koma sindinaphunzitsidwe za mphamvu yake.

Panali zizindikiro zochepa, zedi. Zochepa ndithu.

Munkhani za Beethoven sindinaphunzitsidwe za mphamvu za nyimbo zake, koma mphamvu ya munthu yemwe anagonjetsa kulumala, kuti adzisunge pafupi ndi nyimbo. Munkhani za *Legend* za Wieniawski, ndinaphunzitsidwa kuti nkotheke kusuntha munthu kudzera mu nyimbo kwambiri kotero kuti asinthe maganizo ake pa nkhani yofunika.

Koma mphamvu za nyimbo nzotani? Chinachake chomwe chimapangitsa kukhala koyenera kuloŵeramo; kuposa bizinesi, kapena zamalamulo, kapena zamankhwala? Chifukwa chiyani wachinyamata angatule pansu foni yake m'malo mwa *violin*? Kodi foni si njira yolankhulirana? Ndipo zonsezi si zida chabe zosangalatsira? Zosangalatsa ndi zabwino, zedi. Koma si mphamvu. Sizofanana ndi kuponya mabomba m'dziko, kapena kukhala mtsogoleli wa dziko kapena pulezidenti, kapena kukhala ndi anthu akuchita zomwe ukunena. Kuyimba nyimbo sikuoneka ngati bizinesi yaikulu. Kwenikweni, chikuoneka ngati chinthu chomwe dziko lonse lalengetsa kuti likhoza kukhala popanda icho – onani momwe oimba samawatsamalira, osalipidwa, ndiponso osalemekezedwa.

Mu chikhalidwe chopanda mwambo, oimba sangathe kudziwa mphamvu yao.

Mbalame ikugunda mwadzidzidzi pawindo. Palibe ntchito kwa ine pano. Ndiliba mphamvu.

Miyendo yanga ikufoka, ndipo ndikukhala pansu kwakanthawi. Kamphindi pambuyo pake, mai wamtali wa ku Africa akundiyanakira. Woonala. Palibe mau ena angathe ofotokoza. Kukongola kwake kuli kowala kwambiri, kotero kuti kwakanthawi, ndikukaiikira kuti ndi mzimu. Ndikumva kuseka kwake, ndipo kumandipangitsa kuyang'ana mozungulira. Kodi wayankha ganizo langa?

Atsitsa mutu wake podutsa. "Pali malo omwe akukudikirirani..." akutero.

Kodi wanong'oneza izi?



"Pali malo omwe akukudikirirani... funsani Makolo anu komwe mungapite. Adzakuuzani."

Akubwereza yekha. Odekha ndi otsimikiza. Kenako wapita. Mawindo osatsukidwa akuthwanima ngati magalasi otopa a oyang'anira laibulale odabwa.

Kufunsa Makolo anga? Malinga ndi ine, Makolo ndi a anthu omwe ali ndi mabanja abwino. Banja langa ndi lowawa ngati apulo logwa msanga. Lowola. Lochedwa kwambiri kuti likule kukhala lokoma. Liwiro kwambiri kusunga ziyembekezo zathu za moyo otsatira. Omwazikana padziko lonse lapansi, ovulazidwa ndi zowawa ndi nkhanza za ubwana othera kuphunzitsidwa kuonongana wina ndi mzake, tilibe ntchito yochepa, kufunikira, kapena chilakolako cholumikizana. Izi ndazona – anthu a Slavic ali ndi mwambo wamphamvu wa Makolo, komabe mabanja ovulazidwa ndi achisoni kwambiri omwe sindinawaonepo kulikonse.

Ndiye, Makolo awa ndi ndani?

Ndikuganizira mozama, pamene dzuwa likulowa, ndipo mawindo amafuta akuwala ndi chisangalalo chofiira.

Ndikutseka maso anga...

Makolo a *Slavic*, omwe ali amoyo mu zidole zathu za *Motanka* zomwe zimateteza nyumba, ndi munthu aliyense kapena chilakolako kapena tsogolo lomwe mwasankha. Makolo a *Slavic*, akuvina m'mbali mwa mtsinje, asanaponye chidole cha Marzanna kuti atsimikizire chonde kwa anthu ndi chilengedwe. Makolo a *Slavic* okhala mwa *Mokosz*, mfumukazi ya Dziko Lapansi, onyowa, Amai Aakulu...

Kodi amatanthauza kalikonse kwa ine? Kodi akudziwa kuti ndine ndani? Kodi ndingathe – Ine, mbadwa wao kulankhula nao? Kuwapempha?

Ndikuphumanso m'pemphero, "Kodi ndipite kuti?"

Belu pakhomo likulira, ndipo mwamuna wantali akulowa mu *coffeeshop*. Manja ake ali odzaza ndi foni, mau ake ali okweza ngati alamu yam'mawa, ndipo masitepe ake ndi olimba kwambiri kotero kuti maloto amasungunuka ngati nkhungu mu mpweya wa dzuwa. Ndadzidzimuka. Operekera zakudya akutsamira kuti apukute tebulo langa, "Mungakonde kuitanitsa chilichonse?" Akudziwa kuti ndinena ayi. Kachiwiri konse.

Mwamuna wantali akumenya counter mopanda chipiriro, akutembenukira kwa ine pang'ono. Akupuputa diso kwa ine ndipo ndikumva manyazi. Sizofala pano, kulankhulidwa momveka bwino choncho. Pa T-shirt lake, mau akuti "Göttingen, Germany" akundifikira. Mpweya wanga ukugwidwa.

Malo anga obadwira.

Makolo ali pano. Akugogoda.

\*

Azakhali anga ankandiwerengera nkhani za *Msodzi ndi Nsomba za Golide*. Ndikali mwana, ndinkaikonda nkhaniyo. Buku linali ndi chikuto chakale kwambiri kotero kuti chithunzi chinali chosaooneka bwino. Nsomba? Zeze? Palibe? Ulusi wa



bukhuunali omasuka, ngati nkhani zofunafuna mathero abwino. Ndinkapempha nkhanayi mobwerezabwereza, nthawi zonse ndikuyembekeza kuti pamapeto, nthawi ino, mkaziyo adzapeza mgwirizano. Mkazi waumbomboyo mwina, sakanakhala mulungu, koma akanakhalabe ndi nyumba yabwino. Akanakhalabe osangalala.

Aha! Kodi ndingadzakhale osangalala? M'dziko la imvi ili? Kodi ndinali mkazi amene ankafuna zambiri?

"Ndiuzeni nkhani!", mwana akulira pa sitima. Ndili munjira tsopano. Ndili munjira opita ku muzu wa muzu, ndi pakamwa pa mtsinje wanga oopsa. Ndikupita kumalo komwe ndinabadwira.

"Ndiuzeni nkhani!", mwana akuliranso.

Nkhani? Ndikudziwa nkhani...

Kalekale...

Ndipo ulusi ukulukidwa, kusungidwa bwino mu nkhani za msodzi ndi nsomba za golide yomwe imamupatsa zokhumba, ndipo tsiku lililonse amabwerera ndi chokhumba china, chapamwamba kwambiri kuchokera kwa mkazi wake waumbombo...

Mwanayo akugona. Amai ake, mai wa nkhope yotopa ndi ndolo zofiira, akuooneka kuthokoza chifukwa cha mpumulo, ndipo akutseka maso awo.

Ndikuyang'ana pawindo la sitima. Nkhanayi si okhudza umbombo ayi. Nkhanayi ndi ya mkazi yemwe amazindikira pamene akunyengedwa. Chifukwa chiyani? Chifukwa wakhala akudyetsedwa zonyenga nthawi zonse. Chifukwa chiyani? Chifukwa sanali iye amene ankalenga moyo wake. Ndipo motero, kumapeto kwa nkhanayi, pamene mkazi wa Msodzi akupempha kuti akhale Mulungu, amabwezedwa mu moyo wake – pamalo omwewo pomwe anali kale—kuti iye mwini tsopano athe kuupanga. Kuti mzimu wake uthe kulenga, ndikukhaladi Mulungu, osati chabe olandira madalitso kuchokera kwa omasulira zokhumba zake yemwe sali wangwiro, mwamuna wake. Ndipo ngakhale Milungu za Nyanja inkadziwa izi. Inayang'ana mkazi wa Msodzi, ndipo inati: "Dalitsikani, dalitsikani, dalitsikani, Mfumukazi."

Mkazi ameneyo analidi mkazi wanzeru.

Monga iye, ndikupita tsopano kukachita malonda ndi makolo omwe anandilowetsa m'dziko lino, *mbira* yanga yopepuka, yaying'ono ndi yamphamvu m'dzanja langa, nkhu ni chitsulo cholimba ndi chotsimikizira—poyerekeza ndi *violin* olemera, koma ofooka. Kayendedwe ndi nyimbo za chida ichi cha ku Zimbabwe ndi zachilendo kuno, ndipo kuchiyimba kwandipezera ntchito zochepa.

Mitengo ikudutsa mofulumira kunja, ngati kuti ndi iwo omwe ali pa sitima ndipo ine ndine amene ndakhala chete, pakati pa dziko lapansi. Ndikuyimba manotsi ochepa, ndipo mpweya ukusintho; kunyezimira, mitundu. Mzimu wina ukudzuka. Tsopano ndikudziwa zomwe ndidzapempha: nyumba, malo omwe ndingalengere.



Ndikugona, kutonthozedwa ndi kayendedwe ka mawilo achitsulo akuyenda pa njanji zachitsulo. M'maloto anga akutali, zithunzi zikuwoekera. Mitundu yonse. Akazi, amuna, zolengedwa zowala. Kuseka kwawo kumamveka ngati mbira zambiri zopangidwa ndi mtundu, zopangidwa ndi kuwala. Phokoso likukulirakulira, mpaka ine ndekha ndikumva kuti ndasanduka mbira yaikulu, kusewera nyimbo ndi kayendedwe ka mzimu wanga ndikuwaphatikiza ndi nyimbo ndi kayendedwe ka Chilengedwe (*Universe*). Thupi langa likuyamba kunjenjemera. Pamene ndikuganiza kuti ndiphulika chifukwa cha mphamvu ya kunjenjemera, ndikumva mau awa:

"Ndiwe sing'anga."

Ndine chiyani?

"Ndiwe wa mwambo (*ceremonialist*)."

Mwanjira yanji?

"Pita ku Zimbabwe. Adzakufotokozerwa zinthu kumeneko..." Dzanja langa, litamasuka ndi tulo, mosadziwa likumasuka, ndipo *mbira* ikugunda pansi pa kapeti ya sitima—makiyi akulira.

Zimbabwe.

Chabwino, chabwino. Ndikuti, chabwino.

Göttingen, Germany. Chifukwa chiyani Göttingen? Mzinda womwe dzina lake sindingalitchule nkomwe? Ndili pano kwa milungu iwiri yokha. Osati nthawi yayitali yokwanira kuphunzira chilankhulo chilichonse, kupatsidwa nzika iliyonse, kapena kupatsidwa mwai weniweni. Chifukwa chiyani ndinabwera kuno momwe ndinachitira? Ngati palibe chomwe chimangochitika mwamwai m'moyo, ndiye kuti njira yofikira m'dziko lino, ndi malo obadwira sangakhale achisawawa.

Pamene tikuyandikira tsopano, kumalo amatsenga awa pamene mawilo a sitima akuluka tsogolo langa monga Mulungu Wamkazi Wamkulu amaluka tsogolo, m'pamenenso mpweya ukuooneka kuti ukukhazikika mkati ndi kunja kwa ine. Ngati kuti ndaooloka malire kupita ku dziko lokongola lomwe limakhalapo nthawi zina zokha, m'mphindi, pamene dziko likutseka maso ake, ndi kuphuma mwamtendere. Obiriwira ndi obiriwira kwambiri pano, maluwa amphamvu kwambiri. Ndikumva ngati ndikusambira mu ubwino.

Ku Africa, ndizodziwika bwino kuti kuchita malonda a moyo wanu sikutheka popanda kukhalapo kwa mizimu yomwe inakuoonani kudzera pakhomo (*portal*). Ku Africa, malo omwe tonsefe tinachokera, izi zimadziwika bwino. Ndiye chifukwa chake, munthu aliyense ayenera, panthawi ina, kubwerera ku chiyambi chao. Monga sing'anga yemwe anasintha zonse pambuyo pake anandiuza: "Nyumba yako ili kwina."

Choonadi ndi ichi: Ndikupita kukachita malonda a moyo wanga tsopano. Chimenecho ndi cholinga changa. Ndiliba kanthu kokopora nako: matumba a zovala zonyansa, mbira, thupi lotopa, mantha a maulendo anga, mantha a moyo wanga. Ndipite kuti tsopano? Ndikufunsabe. Malo anga ali kuti padziko la pansi pano?



Kodi alipo? Kapena ndili ngati mamiliyoni a ena, achinyamata, okhumudwitsidwa ndi ndale, miyambo, chipembedzo, ntchito, psychology, ndi ndale zambiri, miyambo zambiri, zipembedzo zambiri, ntchito zambiri ndi ma *pop-psychologies ambiri*.

Komabe, kutopa komwe ndimamva paubwino wa moyo wanga; kuterereka pamwamba pa malo oonda, kusowa kwa mizu ndi kukhazikika, kudzipatula kodabwitsa pakati pa ine ndi ena, kusowa kwa nyumba, kusungulumwa kodabwitsa komwe kukuyamba kukhazikika mu mpweya womwe ndimapuma, chakudya chomwe ndimadya, zotengeka maganizo, chisoni, chilakolako chodabwitsa cha imfa chomwe chandivutitsa kwa zaka zambiri tsopano, nthawi ndi nthawi – zonsezo, ndithudi zingathe kukambidwa. M'malo a kubadwa kwanga. Mwina mizimu kumeneko yakhala ikufufuza mwana wao zaka zonsezi. Mwina akundidikira. Ku Jeremani, kapena mwina ku Zimbabwe? Mwina ndi omwe angandipatse moyo, popeza tsopano zikuooneka kuti chinthu chokha chotheka m'moyo wanga ndi imfa.

Ndataya dzanja lililonse lomwe ndasewera. Africa imandiphwanya nthawi zonse zomwe ndapita – ndipo inde, ndakhalako. Pali chisoni china mwa ine chomwe sindingachigwedeze, ndi zongopeka zina zodzipha zomwe zikungokula. Chisoni chomwe ndikuoona pankhope za anthu ondizungulira—m'masitolo, m'mpheapete mwa misewu, m'masukulu, pazithunzi... chisoni chomwe ndikuoona m'dziko langa lomwe, lolimbikitsidwa ndi nkondo ndi zikumbukiro za nkondo. Chifukwa chiyani amatcha 'Warsaw', pambuyo pa zonse? Chifukwa chiyani sangathe kuiitcha Warszawa, monga nkhani imapita, za msodzi ndi *njuzu* ndi chikondi chao chachikulu chomwe chinabereka mzindao... Chifukwa chiyani ayenera kuiitcha machekeka-a-nkondo (*war-saw*)? Ngati kuti tikufunikira chikumbutso. Mizimu za makolo anga akufa zandivutitsa kuyambira ndisanabadwe. Ndi anthu angati m'dziko langa, a msinkhu wanga, angathe kunena zomwezo?

Zilakolako zimandivutitsa. Zilakolako zomwe ndimadzida chifukwa chazimenezo, chifukwa cha kulephera kwanga kuzikwaniritsa, kapena kuzisiya – kudzipatula kwa Mulungu ndi Mzimu. Nzoona kuti moyo sikanthu, mwina, koma ndikufuna moyo, ndimatero. Ndikufuna moyo; moyo weniweni waumunthu. Izi, kapena imfa. Sindikufunanso pakati-ndi-pakati podabwitsa ayi. Choncho ndikupita kukachita malonda a moyo wanga. Kunena mau anga ndi kupemphera mapemphero anga ndi kuyesetsa kwambiri kuti asamveke ngati kudandaula.

Kuti ndikope mizimu za dziko losungulumwa lomwe ndikupitako, kumene kuli sikulu la pamwamba kapena university yakale kwambiri ndi yotchuka. Sindinamvepo za mizimu za Göttingen, ayi. Ndimamva za akatswiri a zakuthambo ndi masamu ndi *physicists*. Pali zochepe chabe zomwe ndikudziwa za malowo.

Ndani akundidikira kumeneko, mbali inayo ya Nthawiyo?

*Sindikudziwa kupemphera. M'dziko langa, pemphero ndi la okonda kwambiri, la opupuluma, la mpingo wankhanza ndi wandale. Komabe tsopano, ndikufunika kupemphera mapemphero a mwambo womwe wayamba. Ndipo*



*ndikupempha Mzimu Oyera: chonde, lolani mapemphero anga akhale abwino ndi okongola ndipo lolani mau anga ndi nyimbo zanga zikhale zoona. Ndipo ndiloleni ndinene zinthu zomwe ziyenera kunenedwa, zonse popempha ndi kuthokoza mofanana, kuti mizimu yomwe ndikuipempha moyo, mizu, Nyumba – imvengo ndi kudziwa kuthokoza kwanga chifukwa cha moyo womwe inandiweta zaka makumi atatu mphambu ziwiri zapitazo.*

\*\*\*

"Mwambo?"

Ili ndi funso lomwe munthu wachikulire ochokera ku Zimbabwe akundifunsa, pamene ndakhala pansu pa mtengo ku Göttingen.

Ndi tsiku lachisanu. Ndikuyimba *mbira*, ndikutuluka thukuta ndi kudziwa kuti anthu omwe akudutsa akuyangana. Nyimbo zamoyo zongochitika zokha pansu pa mitengo zikuooneka kukhala mlendo masiku ano monga ine ndemwini wamatsenga – ndithudi, palibe zochitika mwamwayi. Ndithudi, pemphero lililonse limayankhidwa musadafunse funso. Ndithudi, *mbira* yomweyo yomwe imandipanga kukhala wina ndiyo yomwe imakopa Tendai, pakuti ilo ndi dzina la munthuyo. Akufunsa ngati angakhudze *mbira*, ndipo nditamupatsa chilolezo, akutsamira kuti asisite makiyi ndi zala zake zolimba. Akuseka mwachisangalalo. Ndikuganiza kuti ndine ofunika, koma mwachioonekere...

Tendai akukhala pansu, akusisita manja ake pamodzi. Kuchokera m'thumba mwake akutulutsa kachidebe kakang'ono kooneka ngati *pyramid*, komwe kuli ufa wa bulauni (*bute*), ndipo popanda mau, akuuponya pansu.

"Pali pemphero lako!" akutero, atang'ung'udza mau ena.

"Koma pemphero sili pemphero popanda nkhani... Makolo anatipatsa nkhani kuti tithe kupemphera ndi kalembedwe kotheratu, kosanjikizana, kofotokoza zosafunikira. Choncho, mwina tikhoza kuyamba nkhani yokhudza mwambo ndi nkhani yokhudza zodabwitsa." Akusuntha chiuno chake kutali ndi muzu womwe ukatuluka pansu, ndikukhala bwino. Ndimamutsanzira, ndikukonzekera kumva nkhani yake.

"Pa tsiku lomwe Agogo anga aakazi okha omwe anali moyo anamwalira," Tendai akundiiza, "pa tsiku lomwelo, mmodzi wa abale anga apamtima anagunda ndi galimoto ndipo anatsala pang'ono kufa. Ndinali ku Harare panthawiyo, ndipo ngakhale agogo anga anali atamwalira kuno, ndipo ndinali kukonzekera kupita ku maliro a agogo anga, ndinalandira foni kuchokera kwa apolisi ena akunena kuti apeza msumbali wanga uyu pa njinga, kuti analibe chikope kapena ID, koma kuti kudzera mu chozizwitsa china adatsata foni yomwe idayimbidwa ku foni yanga m'mawa womwewo. Umu ndi momwe Makolo amagwirira ntchito – kudzera mu zochitika mwamwai-

...ndithudi palibe zochitika mwamwayi...



Tendai akupitiriza, "Choncho m'malo mopita kumpoto, ku Poland, kukhala ndi akufa, ndinakhala m'malo, kukhala ndi banja lamoyo. Zinandiwawa, koma Agogo anga akhoza kumva nyimbo zanga, kuchokera pomwe ndinali, izi ndimadziwa.

M'malo awa pakati pa moyo ndi imfa, pamene sindinkadziwa kuti ndine uti – wamoyo, kapena wakufa - abambo anga anandiimbira foni kuchokera ku South Africa. Sakanatha kugula tikiti kuti abwere kudzaika amayi ake, ndipo ululu wa izounapita mozama kwambiri ndi kutali kotero kuti sitinalankhule kanthu za izo."

Ndikufuna kunena chinachake, kuvomereza tsatanetsatane owawa uyu, komabe sindikufuna kusokoneza nkhaniyo. Tendai akundiyang'ana, ngati akuvomereza ganizo langa, ndiyeno akupitiriza.

"Zowawa zazikulu sizitchulidwa mayina, ndikutsimikiza mukudziwa. Mukuooneka ngati munthu yemwe wadziwa ululu."

Sindikugwedeza mutu. Akupuma pang'ono, koma akupitiriza, "Choncho, abambo anga anandiimbira foni, ndipo sanalankhule za amai ake akufa, koma m'malo mwake za mwala ochokera kuthambo (meteorite) omwe unagwa Padziko Lapansi ku Russia panthawiyo. Chinali chochitika chodabwitsa. Komabe tonse tinali kulira. Tonse tinali ndi chidwi. Tonse tinali achisoni. Tonse tinali otengeda. Abambo anga pafoni anali kunena kuti ankafuna kuti achinyamata azitha kuiimirira mwachidwi ndi chinsinsi cha chinachake—zinsinsi za Chilengedwe—m'malo modabwa momwe angapezere ndalama ndi kukhala oyang'anira mabanki. Ndimakumbukira momwe ankalankhulira, mau omwe ankwiritsa ntchito..."

"Chidwi (*Awe*). Zozizwitsa. Mzimu. Kudzipereka. Kukongola. Matsenga. Chinsinsi. Ukulu. Moyo."

"Mu Chipalishi, munganene kuti, *zachwycić się wreszcie*," ndikumuuza.

Amamwetulira, "Ndipo ndimakumbukira momwe zinkamveka zoona, ngakhale abambo anga eniwo amavutika kukhala ndi chidwi ndi moyo, ndipo amaoneka ngati okaikira kwambiri. Maphunziro omwe ndinaphunzira kuchokera kwa abambo anga, nthawi zambiri ndinkayenera kuzembetsa pakhomu lakumbuyo, kumasula myala zamtengo wapatali kuchokera ku kukaiikira kwa mtima osweka ndi nkhanza za munthu yemwe anaona zinthu zonse zolakwika asanasangalale ndi chilichonse chomwe chingakhale chabwino."

Mphepo inali itayamba m'mitengo, ndipo gologolo ofiira anaima pafupi nafe, akudabwa ngati tinali kudya. Mphepo, mtengo, gologolo... mwamtendere kwambiri. Ndinamva tsamba likutembenuka, ndipo chidwi chomwe Tendai anali atangolankhula kumene chinagwira paphewa panga.

"Izi ndinaphunzira kwa abambo anga, ndiye: kuthamangitsa zinthu zomwe zimatidabwitsa. Nthawi zina zimafuna kukhala osweka kwambiri, nthawi zambiri – myala zochokera kuthambo zomwe zimagwa padziko lapansi zimagwa mwamphamvu. Imang'ambika, kudziphwanya yokha ndi zinthu zomwe zogunda. Komabe, ndi kusesa kokongola kwa moto kudutsa thambo. Komabe, timadzitsegula



tokha ku matsenga. Moyo ndi waufupi kwambiri kuti tikhale ndi nthawi yotopa nawo. Chinthu choterocho ndi matenda a mzimu—chinthu choterocho ndi njira yomwe sitisuntha ndi Mizimu zathu, ndipo sitingabwere ndi kudzichepetsa koyenera ndi kudzitsegula tokha ku Chidwi, mu mwambo."

Tendai anamwetuliranso. Anali ku Poland kwakanthawi asanabwere ku Göttingen kudzachita nao *graduation* ya mwana wake. Adzakhala akubwerera ku Poland m'masabata ochepa, kenako kubwerera ku Zimbabwe, posachedwa. "Kukuzizira kwambiri kwa iye," anatero. Zomwe sananene, kapena kufunikira kunena: "Kutali kwambiri ndi kunyumba."

Tinakhala pamenepo kwakanthawi, tikuyang'ana dzuwa lam'tendere likugona m'manja mwa horizon yodekha. Ndinaganizira nkhani ya Tendai, momwe inaliri yokongola, ndi yoopsa komanso. Momwe imfa imagwetsera chidwi m'mitima zathu nthawi zina, monga momwe moyo umachitira. Momwe moyo wakhalira wovuta, momwe waliri kutali ndi kuphweka kwa kugwira *mbira*. Momwe tonse talandilidwa, kuponderezedwa, ndi kugonjetsedwa ndi zosankha zauzimu ndi zaluso za lero. Tikufunika—tonsefe—kukhala akatswiri otsatsa malonda, kudziwa momwe tingauzire anthu ena zomwe akupeza kuchokera kwa ife. Ife – tonsefe, tsopano - tikuuzidwa kupatsa anthu zomwe akufuna. Ndipo anthu akufuna chiyani? Mkate ndi Zisudzo (*Bread and Circuses*), zikuooneka choncho. Sitingadziwe momwe tingapemphe matsenga – sazili m'dera lathu. Ndi chisomo. Amaperekedwa. Momwemonso zikuooneka zopusa kupita ku Mizimu nthawi zonse, ndi kupempha zomwe tikufuna, kulirira zomwe tikufunikira: m'malo mwake, zikumveka bwino kupita ku Mizimu ndikunena kuti: tigwetseni ndi Chidwi. Menyani Chidwi m'mitima mwathu. Gwedezeni Mzimu wathu.

Kenako, pansu pa mtengo, titazunguliridwa ndi ophunzira otanganidwa akuyenda m'njira zokhala ndi mitengo, Tendai ndi ine tinapemphera. Timapemphera zenizeni. Magalimoto akudutsa mofulumira mumsewu. Nkhunda ikulira patali. Thambo ndi laling'ono, ndipo tsopano, pamene kuwala kukufa, likukhala laling'ono kwambiri. Ndipo tikugwirana manja, onse alendo, ndipo mau okha omwe ndingaganizire, ndi:

"Chonde, inu nonse Aakulu ndi Okongola... chotsani m'kulankhulana kwanga mau alioonse aumunthu osafunikira, ndipo onjezerani chilichonse chomwe mukudziwa, chomwe chiyenera kunenedwa. Ndithandizeni kulumikizana ndi kudzichepetsa kofunikira kumeneku, kopanda mau. Ndithandizeni kumva."

Tikuthera pamenepo. Mwambo watha. Mitengo ikumwetulira, thambo lili lo biriwira lozama, logona, ndipo ndikutsimikiza komwe ndikufunika kupita. Ndikuiimirira, ndikudziwa izi:

Kukambirana ndi Mzimu ndi kulankhulana. M'lingaliro limeneli, Mwambo si wa anthu okha.

\*\*\*



*Panthawi ina pakulira kwanga chifukwa cha kutaiika kwa kuya m'zilankhulo za dziko lapansi – zoterereka pamwamba, zophwanyidwa, zofinyidwa ndi kupsinjidwa ndi lilime la ulamuliro wa Chingerezi - ndinazindikira kuti palibe chinthu chonga kutenga popanda kupereka, ngakhale mu kusakaniza kwa zilankhulo. Kalembedwe ka chilankhulo chachibadwile kadzasakanizidwa nthawi zonse ndi lilime la watsamunda watsopano, ndichifukwa chake zilankhulo za Chingerezi za ku Africa ndizo zomwe zimandisuntha kwambiri, kuposa cha ku Britain chomwe chimaganiziridwa kuti chikuoonetse chilankhulo chifukwa chokhala ndi mau ambiri mmenemo. Ndiye chifukwa chake Chingerezi cha ku Zimbabwe chili ndi kuya komwe Chingerezi cha ku America chilibe – ndi chifukwa cha kulemera kwa mau, ndipo kulemera kwa mau kumaperekedwa osati kuchokera ku chilankhulo cha Chingerezi, koma kuchokera ku chilankhulo cha kunyumba, chomwe ndi Shona kapena Ndebele, kapena chilankhulo china. Ndiye chifukwa chake Chingerezi changa sichidzakhala Chingerezi monga Chingerezi chikuyenera kukhalira, monga momwe chikanakhala ngati chilankhulo changa choyamba sichikanakhala Chipalishi. Chipalishi ndicho chimapatsa mau anga a Chingerezi kulemera. Choncho mwina pofika pano ndikuyandikira ndi kukayikira kwakukulu chilichonse chomwe ndikuganiza kuti akatswiri a zilankhulo akunena za kukhala kapena kusakhala olankhula zilankhulo zambiri – zomwe ziri kapena ayi. Inde, zilankhulo zambiri zingayambitse chisokonezo m'mitu zathu, koma choonadi ndichakuti mitima zathu siimasokonezeka, ngakhale ndi zokoma zosiyanasiyana za mau ndi zilankhulo zosiyanasiyana. Zomwe zilinso chifukwa chake chilankhulo chokha sichikhala ndi zambiri zochita ndi kulankhulana, koma ndi kukoma, ndi kukonza, ndi kukhala ndi moyo. Mau ayenera kupezedwa, asanapatsidwe mphamvu za moyo zamaw.*

*Komabe, monga alendo odabwitsa amakono, tili pachiwopsezo chogwera pakati pa ming'alu za zilankhulo, zikhaliidwe, mayiko, ndi zochitika, mpaka tili pachioopsezo chosamveka ndi aliyense. Apa ndipamene ndikudziyeza ndekha tsopano ndikupita ku Zimbabwe... mlendo okaona malo, mlendo osaloledwa, chilichonse, murungu (Mzungu), mlendo, mlendo—kuyenda tsopano, kuouluka, ku Zimbabwe, kukokedwa ku dziko losweka, ndipo ngakhale sindikudziwa panobe—ndidzakhala ndi zochitika za kuthyoka nalo mobwerezabwereza, mpaka zikuooneka kwa ine kuti kuthyoka ndi njira yokhayo yomwe ndingadzifotokozere, moyo wanga, cholinga changa; mpaka kumva kuti chinthu chokha chomwe ndingachite tsopano, ndikubadwanso, moyenera, moyenera nthawi ino—Mu mwambo, ndi anthu onse akuvina, ndi kuyimba, ndi kumenya ngoma. Kubadwanso kwanga tsopano – ndi nthawi ya kubadwanso kwanga!*

*Ndi nthawi tsopano.*

*Ndikumva okalamba kwambiri, kwambiri...*

*Zimatheka bwanji kuti moyo ndi wautali komanso waufupi nthawi yomweyo? Waufupi kwambiri kuti umwe ubwino onse, wautali kwambiri kuti upulumuke zowawa za mtima osachedwa kumva.*



\*\*\*

#### HARARE, ZIMBABWE

Tendai ananditsimikizira kupita ku Zimbabwe.

Pemphero lake – osati langa - linagwira ntchito.

Nyimbo yake – osati yanga - inanjenjemera mwa ine.

Maloto anga – a palibe wina - anatsoka mgwirizano, ndipo ndinali pano, ku Harare, likulu la Zimbabwe.

Ndafika masana, ku dzuwa lotentha lomwe landidzutsa pambuyo pa maulendo angapo a ndege. *Billboards* zazikulu zolembedwa “HIFA – the Harare International Festival of the Arts” zikuwunikiridwa ndi ilo. Mitundu yake ndi yowala kwambiri, ngati majini ovina omasulidwa m'mabotolo awo.

Ndangothera kumene miyezi ingapo ku Peru, kuphunzira nyimbo ndi kuchita nao zakudya za zomera (*plant dietas*) (“sama” mu Shipibo, zomwe zimatanthauza “wekha” mu Chipalishi, ndipo ndizomwe dieta imatanthauza kukhala—ndondomeko ya kukhala wekha, kudulidwa kuchokera kunja, kumanga maubwenzi ndi mizimu za zomera kudzera mu nyimbo ndi mwambo), ndipo tsopano ndatera kumene maloto anga anandiuza kuti ndikuyenera kukhala. Chikundidikira n'chiyani kuno?

Billboards zikundiitana mogwira mtima. Ndikupita ku Harare Gardens, pakati pa mzinda, kumene Chikondwerero chikuchitikira – mu May, kumayambiriro kwa dzinja. Kumeneko ndikukumana ndi mwamuna yemwe akugulitsa *nyunga nyunga*: “yowala, yonyezimira, nyenyezi” *mbira*. Ndikuzikonda kwambiri, ndipo, olimbikitsidwa ndi Chiooniso Maraire ndi nyimbo zake, ndikugula imodzi. Ndikufunsa mwamunayo ngati akudziwa za myambo ina iliyonse ya *bira* (Miyambo ya Makolo) yomwe ikuchitika, popeza ndili kumeneko kufunafuna izo. Nditakumana ndi myambo za zomera zopatulika komanso myambo za nyimbo za Mphunzitsi wanga wa Nez-Perce, Phil, ndili ndi njala za mwambo. Ndikufuna kukumana, mozama, ndi nyimbo mu nkhani zopatulika iyi – kuno, ku Zimbabwe.

Kutchula kwanga *bira* kukusinthika kaonedwe ka mwamuna uyu kwa ine. Kuchokera ku mlendo wokaona malo ochezeka, ndikusintha kukhala wina yemwe amadziwa chinachake. Akumasuka, ndikulankhula zambiri, ndipo ndipamene, akundiuzza chinthu chochititsa chidwi kwambiri ichi: “Ngati achinyamata athu akanadziwa m'phamvu za chida chomwe muli nacho m'manja mwanu, ndiye kuti akanakhala akuyenda ndikuyimba mbira m'malo mosewera ndi mafoni awo. Akanakhala akunyamula *mbira* m'matumba awo, ndikugwiritsa ntchito zala zawo zazikulu ndi zala kuziimba pamayendedwe ndi m'mizinda, m'malo molemba nthawi zonse m'makina awo.”

Ndaganizira mau olimba mtima awa nthawi zambiri kuyambira pamenepo, ndikuwona dziko lathu likutsikira kukhala skrini pambuyo pa skrini, maso athu



akufa dzanzi ndi kuwala kochita kupanga kwa zosangalatsa za *Frankensteins* zomwe tadzipangira tokha.

Ndafika ku Zimbabwe ndi zida zisanu ndi chimodzi: *djembe* yanga, mbira yanga, *violin* yanga, *karimba* yanga, zitoliro zanga, ndi rattle. Mbira, cholowa chazimu cha Zimbabwe, chinali gao limodzi lalikulu la kukhala kwanga pano. Ndinkafuna kuphunzira kuyimba "moyenera" monga amanenera. Pakadali pano, ndinaphunzira nyimbo kuchokera kwa munthu yemwe anandigulitsa karimba kanga komanso kuchokera ku YouTube, ndipo ndinapanganso nyimbo zanga mu mwambo, monga momwe zinkabwerera. Ngakhale ndinaphunzira nyimbo zachikhalidwe, ndi mphamvu zake, nyimbo zanga zinabweranso, ndi mphamvu zonse, nthawi zambiri zopanda mau – nthawi zina kungokhala kusokonezeka kwa phokoso komwe sikunakwane m'gulu lililonse. Nyimbo zomwe zinabwera zinali zophweka, nthawi zambiri zolunjika pa mau amodzi, choonadi chimodzi, lingaliro limodzi, chilakolako chimodzi cha mtima wanga, ndipo nthawi zina nkhani imodzi. Umu ndi momwe ndinaphunzirira kuyimba. Zoyesayesa zonse, zoyambirira ndi zomaliza, zodziika ndekha mu nkhangungu zinalephera.

Ndinaphunzira mkati mwa myambo, ndiyeno mwamsanga ndinatembenezira chilichonse chomwe ndinaphunzira ndikuchita mwanjira yanga. Panthawi ina, ndinalungamitsa izi kudzera mu kufotokoza kuti ndinali mkazi, ndipo aphunzitsi anga anali makamaka amuna, nthawi zina ozama kwambiri mu myambo zolamulidwa ndi amuna. Koma pali kufotokoza kwina, kosakhudza jenda, ndi kumasuka kwambiri, komwe kuli kuti asing'anga onse achikhalidwe ndi osiyana: sing'anga aliyense wachikhalidwe ali ndi njira yake. Tikhoza kuphunzira, tikhoza kubwereka, tikhoza kugwiritsa ntchito, tikhoza kulowa m'maparadimu a chikhalidwe, koma pamapeto pake, sing'anga aliyense ali ndi njira yake, mizimu zake, Makolo ake, alonda ake, kuyenda kwake. Munkhani zachikhalidwe, izi zimamveka bwino: sing'anga sanapangidwe kukhala kope la munthu wina. Sing'anga amapangidwa kukhala oyambirira kotheratu. Sing'anga amapangidwa kulandira malangizo kuchokera ku Mzimu.

Asing'anga – kaya akhale *shamans*, *masvikiro* kapena *ng'anga* oimba kapena onse—ndi mphatso ku gulu lao, osati chifukwa akukwana, koma chifukwa makutu awo ali okonzeka kumva phokoso lomwe limachokera kunjira. Choncho kusakaniza ndi kufananiza kwa omwe tingakhale sikuwoneka chimodzimodzi, ndipo anthu akale m'mudzi amadziwa kuti pamene munthu achita zinthu mwanjira inayake, ndi maziko, kapena chilimbikitso kuseri kwa khalidwelo chomwe chiyenera kumveka koyamba ndi kuthandizidwa, m'malo moti khalidwe lonse litayidwe, kuchititsidwa manyazi, ndi kulangidwa.

Monga Akulu Anzeru Pathisa Nyathi amanenera mobwerezabwereza: "Mfundo zauzimu zomwe zimalamulira myambo zonse ndi zofanana. Zofanana, zofanana, zofanana."



Masabata angapo pambuyo pake, ndikuitanidwa ku Mwambo wa Makolo. Kumeneko, pakati pa kuyimba mbira, ngoma, kuvina, mowa wachikhalidwe ndi changu chambiri, ndikukumana ndi mzimu wa makolo.

"Pali chinachake chosiyana pa iwe", *Svikiro* akundiiza. "Makolo ako sanachitepo chowawa kwa Makolo anga."

Akuooneka odabwa. Sanadziwe kuti mukhoza kukhala munthu oyera popanda kunyamula pamsana panu abale atsamunda akufa, koma kuchokera ku kaonedwe ka Mwambo wa mu Africa, izi n'zofunika kwambiri. Tikakumana, zomwe Makolo anga anachita kapena sanachite zili ndi ntchito, zimaluka mu nsalu za kuyanjana kwathu. Ngozi, mizimu zanjala, ziyenera kudyetsedwa – koma ziyenera kudyetsedwa mwachilungamo.

Kuti a Slavs ali ndi mwambo wa Makolo wapafupi kwambiri ndi a Shona, ndi kuti sitinapangane utsamunda wina ndi mzake – izi zikuooneka kuti zikutithandiza kulowa mu mtsinje ozama wa kulumikizana omwe umapitilira malingaliro apamwamba, achangu, ndipo m'malo mwake ndi mau a Mzimu m'Miyoyo Zathu.

\*\*\*

ZAKA ZIWIRI PAMBUYO PAKE...

HARARE, ZIMBABWE

Zonse zikuooneka ngati masewera, mwanjira ina, panthawiyi, zaka pambuyo pake, nditapita ku Zimbabwe, nditadulidwa kudzera mu chopera nyama cha magawo angapo a kuyambitsidwa (*initiation*). "Unalidi juga," anthu amanena. "Chifukwa chiyani Zimbabwe?" amafunsa. Samvetsa msewu womwe uli mndandanda wa zizindikiro, koma ndikudziwa zizindikiro zinachokera kwa Makolo anga a ku Poland, zinabwera zitadindidwa ndi chivomerezo ndi aja a tsitsi lakuthengo, oimba, a Slavic. Ngakhale sanali Makolo okhawa okhudzidwa, ndithudi. Munthu sapita ku Zimbabwe pa zofuna za Makolo a ku Poland. Makolo a ku Africa ayenera kukhala okhudzidwa kwambiri—ofunikira, kwenikweni. Zotsatira zake ndizakuti ine—monga ambiri ena m'dziko lino – ndaika moyo wanga pa loto, ndipo ndikuyang'anabe zotsatira za juga imeneyo. Sizinamveke ngati inali juga yanga. Zinamveka ngati zopanda chisankho, komabe ndili pano, osatsekerezedwanso mu zoopsa za moyo wanga. Ndili pano, bwenzi la Mizimu wanga tsopano. Ndili pano, umboni kuti zozizwitsa zimachitika – wathanzi, wathunthu, ochiritsidwa, ndi wamwambo oyenera pamenepo.

Choonadi ndichakuti m'zaka zanga zochepa padziko lapansi lino, ndaphunzira pang'ono chabe kupemphera.

Pali Choonadi chobisika pakona ya maso athu onse: ngati mumvetsera mosamala mukhoza kumva maganizo a mitengo – ndi chisamaliro chachikulu, mukhoza kumva chomwe chili kuseri kwa maganizo a anthu ndipo mukhoza kuwaona, ngati kwanthawi yoyamba. Ndipo mukamva maganizo kuseri kwa



maganizo, mukhoza kumva chikhalidwe cha chinthu kuseri kwa maganizo, nyimbo yomwe ilipo, yomwe imawakulunga – mukhoza kuoona, ngati mumva nyimboyo. Chilichonse m'moyo chiri mu utumiki wa Msewu, ndipo ngati mumvetsera mosamala, mukhoza kumva maganizo a Msewu, ndipo ngati mumvetsera kwambiri, kwambiri mosamala, mukhoza kumva chikhalidwe cha chinthu kuseri kwa maganizo a Msewu.

Ndipo chiyani, pempherani, ndi chikhalidwe chodabwitsa cha chikondi? Ndiuzeni Choonadi, chonde, ngakhale chitakhala chovuta. Nthawi zambiri ndimamva ngati mai okalamba tsopano, ndipo ndingakonde – kwambiri - kumva chinachake choona, kuposa chinachake chochititsa chidwi.

Komabe tsopano, ndikuyang'ana mmbuyo pa zaka izi za kuyambitsidwa (*initiation*), chinachake mkati mwanga chakula kunyadira njira yomwe ndinasankha kutenga – ngakhale nthawi zambiri ndinkamva kuti ndinalibe chisankho nkomwe. Ndikuyang'ana mmbuyo, zikumveka ngati ndinathera nthawi yanga yambiri mwanjira ina pansi pa mitengo, m'maphiri – obisika poyera, ndikuyimba karimba, mbira, violin. Tsopano, ndikatembenezira nkhope yanga kubwerera ku gulu lomwe ndikumva liyenera kukhala pamenepo, ndi nkhani zanga zochepa ndi nyimbo zomwe ndiyenera kupereka ndi kupatsa. Ndili ndi violin. Ndicho chinthu chokha chomwe chingandilankhulire ndipo osati mu luso (technique), ayi, osati nkomwe mu luso. Kuyimba violin si luso, chinthu ichi ndachiphunziranso. Kuyimba violin ndi phunziro la kumvetsera mau owona a zolengedwa zonse. Kuyimba violin ndi mwambo opatulika.

Tiyeni tiyambenso, nthawi ino ndi nkhani ina. Ngakhale malingaliroosalumikizana ndi osokonezeka ngati anga, amafunikira nkhani, pambuyo pa zonse. Ndinali kusala kudya m'phanga ku Domboshawa, Zimbabwe. Limodzi mwa maphanga omwe anthu a tchire – a San - anasiya zojambula zao. Ndinkadziwa zochepa panthawiyo za maphangawo, koma ndinali nditangotuluka kumene mu nthawi yowawa, yopweteka, moto wakuthupi kuchokera kuyenda kwanga ndi Makolo ndipo ndinali ndi nkhangole ya kupepesa kwa iwo. M'mimba mwanga munandiuza kuti njira yabwino yopepesera ndikumvetsera mosamala, ndipo njira yabwino yomwe ndaphunzira kumvetsera ndikupita ku chilengedwe ndikusala kudya. Choncho ndinali pamenepo, ndikusala kudya, osokonezeka za chomwe chinachitika – mimba, kugwetsedwa ndi moto wa Makolo, kupita padera, ndi mkwiyo wao pakhungu langa.

Ichi ndi chinthu chomvetsetsa za ife Ochita Mwambo (*Ceremonialists*)—sitipanga zisankho zounikiridwa, ayi. Timatsatira chilankhulo chophimbidwa cha Auzimu Akuthengo (*Wild Spirited Spirit Ones*). Tili mu kumasulira kosalekeza, tcheru ku chilankhulo cha Mzimu m'miyoyo yathu. Timapita komwe tikuitanidwa. Si chinthu choipa. Si chisankho, komanso, osati chaumunthu. Chisankho chokhudzidwa ndi chisankho chotsatira chikhalidwe chathu. Ndiye chifukwa chake ndimapeza chilankhulo cha "chisankho" chomwe



chikugwiritsidwa ntchito panopa mu chikhalidwe chapamwamba cha kumadzulo kukhala cholakwika kwambiri: kusankha kutsatira chikhalidwe changa, ndi kusankha kutsatira mau a Mzimu wanga ndi zosankha zokha zomwe zilipo. Zakhala zovuta kwambiri, ndipo mwa izo, ndimanyadira nazo. Vuto ndilakuti mukuganiza kwa Chitukuko (*Civilisation*), sitipatsidwa mwayi osankha kuchita zinthu molingana ndi chikhalidwe chathu; timapatsidwa gulu la zosankha ndi gulu la zotsatira zotheka ndi zodziwikiratu ku zosankha zija, ndipo motero timatsekerezedwa mkati mwa gulu la maparadimu omwe amaganiza za moyo mwanjira inayake, njira imodzi yokha. Iyi si njira yomwe Aakulu omwe amakhala mu Mitengo amatifunsa kuti tidziwe tokha. Choncho chisankho ndi lingaliro lonyenga, lonyenga. Osachepera lakhala kwa ine.

Pankhaniyi, ndinasankha kupita ku Domboshawa, kunja kwa Harare, Zimbabwe. Koma ngakhale chisankho ichi, chonde mvetsetsani, chinakonzedwera ine. Mukasankha kupita ku Tchire, ku Chilengedwe, ku Phiri, kukasala kudya, chisankho chimenecho chimabwera zokha mwa kuitanidwa ndi Mizimu yomwe imakhala kumeneko. Choncho tiyenera kusankha tonse, ndipo mu matsenga ndi chinsinsi chimenecho chomwe ndi msewu otseguka wa Mzimu, timasankha kupita nthawi yomweyo pamene iwo amasankha kutiitana. Chisankho changa chimakhala chao—ali owolowa manja choncho, Okongola Awo omwe chilankhulo chaumunthu chilibe chingwe chowapatsa nyumba yoyenera mokwanira.

Ndinadzipeza ndili m'phanga ku Domboshawa. Masana, ndinkabisala momwe ndingathere, kuti anthu ochepe omwe ankabwera asandipeze kumeneko. Komabe, limodzi mwa masiku amenewo gulu la ana asukulu linabwera ndi otsogolera. Ndinali nditakhala kuseri kwa mtengo m'mphepete mwa phanga, ndipo ndinamva zomwe otsogolera ankanena: "anthu omwe anajambula zithunzi pakhoma la phanga anali *masvikiro* kapena *mashamanas* - (*mashamansingakhale* njira ya Chi Shona yonenera shamans ambiri). Ankaloŵa mu mzimu kapena trance ndipo ankajambula zithunzi zomwe mukuzioona pano." Ana ndi otsogolera anachoka. Posakhalitsa pambuyo pake, ndinapeza mkanda ojambulidwa m'dothi kuseri kwa mtengo, osiyidwa pamenepo ngati kwa ine. (Chilankhulo cha Mzimu nthawi zonse ndi chaumwini, ndipo kusala kudya m'Chipululu ndi malo omwe chilankhulo chakuya chamaphanizo chimatigunda mwachindunji – palibe zochitika mwamwayi, ndipo makamaka osati pamene mukusala kudya pansu pa mtengo. Ndi njira yonolera makutu athu, ndi kumvetsetsa mwatcheru.)

Apa panali kumva kwanga, ndipo sindinkadziwa nkomwe izi pamene ndinafika koyamba ku Zimbabwe: kukhala sing'anga (*mediumship*) wa mtundu womwe a Shona amadziwa bwino, ndichifukwa chake ndinaitanidwa kumeneko. Kuitana kwauzimu kozama kunkafuna kunenedwa kudzera mwa ine, kudzera m'thupi langa, kudzera m'mau anga, kudzera mu kaoonedwe kanga. Mzimu wina unandiitana kunyumba ku dziko lomwe nthawi zonse limagwedezeka ndi kusakhazikika, dziko lomwe kuukira boma, kukwera mitengo, kusowa kwa mafuta



ndi chakudya kunali kwachilendo – kumalo komwe banja ndi maziko a moyo, ndipo komwe ine ndemwini ndinalibe. Komabe pamenepo panali, pansu, mkanda – kundioonetsa ine kuti kuvala mikanda, kutanthauza ntchito yochiritsa, chinali chifukwa chake ndinali pano. Maganizo anga aumunthu anachita zinthu zambiri momwe angathere ku chidziwitsocho kuti achipotoze – chifukwa sichikhala momwe timaganizira kuti chidzachitikira – koma pamapeto pake, kuyambitsidwa pamilingo yonse ndiko komwe ndinadutsamo kuti ndipeze chikhalidwe changa chenicheni, monga ochita mwambo (*ceremonialist*). Ndi bwino lomwe ndingabwere nalo, malinga ndi mau. Inde, ndingadzitche *Shaman*. Inde, chimenecho chingakhale choona. Inde, ndingadzitche *Svikiro*. Inde, pamlingo wina chimenecho chingakhale choona. Inde, ndingadzitche wauzimu, ndipo inde, chimenecho chingakhalechoona. Koma *Ceremonialist* kumamveka bwino—ndi kwachindunji, kolunjika, ndipo kumapereka chithunzi cha chikhalidwe cha mphatso yanga yapadera. Palibe njira imodzi yokhala *shaman*, palibe njira imodzi yoyambitsira, palibe njira imodzi yolankhulira ndi Mulungu kapena Kholo kapena anthu ang'onoang'ono mu Chilengedwe. Koma mukagwidwa mwamphamvu kwambiri ndi dzanja la Mulungu Wamkazi ndipo potsiriza kupeza lilime lanu ngati njoka yotaiika, ndipo mukagwira diso la Aakulu Okongola Awo, ndiye mumamva mwa inu nokha kukula kwa chidziwitso – ichi ndi chomwe ndiri pano kuti ndichite. Ndipo ndiye mukufuna kunena chinachake. Ine ndithudi. Ndiye mutha kukhala ndi chinachake choti munene. Kapena kuyimba, ngale. Kapena mwina zingakhale chinthu chimodzi – nyimbo, nkhani, mau, ndi mau. Pambuyo pa zonse, kusakaniza (*alchemy*) kwa zonsezo pamodzi kumapanga matsenga.

\*\*\*

#### HARARE AVENUES

Chilungo (*flu*) chinkayenera kuyembekezeredwa, koma sichinatero. Ndinkaganiza kuti malungo (*malaria*) anali omveka, koma ayi—Harare sili yodzaza ndi malungo, ili yodzaza ndi chilungo cha dzinja, ndipo ngakhale ine—ndi khungu lokhuthala la ku Poland—sindinali otetezedwa.

Kwenikweni, monga mmodzi wa aphunzitsi anga anandiuza, shamans amadwala kwambiri. Ndipo sangathe kudzichiritsa okha. “Ng’anga hazvirapi”, umatero mwambi wa Chi Shona. *Shaman*—wauzimu—sing’anga—sangadzichiritse yekha.

Choncho, nayi choonadi chokhudza *shamans* chomwe ndinaphunzira pamene ndinkagona pabedi, kukhala m'chipinda ku Avenues ku Harare, osatha kuiimirira popanda kugwa (izi zinali zoyamba): *Shamans* amadwala, kwambiri, chifukwa nthawi zonse amadzichiritsa okha, ndi dziko lapansi. Zizindikiro zao zimanthauza chinachake. Koma sakuuzani za izo. Osati kwenikweni.

Maloto anga panthawiyo anali odzaza ndi *njuzu*, ndi madzi, ndi amuna okhala ndi mipeni, ndi mikango zazikulu, ndipo panali maloto ena omwe anandichititsa mantha kwambiri ndikufuna kudzuka, ndi kugona



kwamuyaya—kuoona zinthu zosakhalapo tsopano, ndikuoona amuna okhala ndi mipeni akutuluka m'makoma kuyesa kundilasa. Izi, ndinaphunzira, zinali zachilendo. "Mantha ayenera kugwedzedwa kuchoka mwa iwe, kutulutsidwa ngati thukuta kuchoka mwa iwe," anatero mmodzi wa aphunzitsi anga pambuyo pake, mu dare lake, kanyumba kozungulira, kozunguliridwa ndi zitsamba, nsalu zopatulika, zipolopolo, miyala, mafupa, ndi ndodo zoyendera zopatulika (*tsvimbo*). Anandipatsa zitsamba ndikundipangitsa kutuluka thukuta kwambiri, pansu pa chivundikiro cha pulasitiki.

"Uyenera kutuluka thukuta ndi mizimu za zomera."

Agogo anga aakazi anakonda kunena zomwezo. "Tulutsa thukuta!" Nthawi iliyonse malungo akabwera. Ankawunjika mabulangete pabedi langa ndikunena, "Tulutsa thukuta."

Tsopano ndinali pano, ndikuchitulutsa – kutulutsa chilichonse thukuta, kudzifinya ndekha, kufinyidwa - ku Southern Africa, kutali ndi komwe agogo anga aakazi ankachitira thukuta lawo.

Mantha anali owunikira.

"Mantha ndi chinthu choyamba chomwe chiyenera kuchoka, ndipo ichi ndi chinthu chovuta kwambiri," ndizomwe mphunzitsi wanga ananena. "Mantha ndi chinthu chomwe chimakulepheretsani kuoona, kumva, kudziwiratu moyenera. Dziko lino sili monga likuonekera nkomwe, ndipo tonsefe tikanadziwa izi, ngati tikanatha kutsegula maso athu... ndipo tikanatha kutsegula maso athu, ngati tikanatha kudzuka ku mantha."

Kupotoka pakati pa mapepala, oviikidwa mu thukuta ndi misozi, ndinali kudzuka ku mantha.

Mantha ndi chinthu chovuta kwambiri kugonjetsa pambuyo pa zoopsa (*trauma*). *Trauma* imadula zidutswa za iwe, ndipo ndiye umakhala ogontha, wakhungu. M'njira zambiri chitukuko chatu chili chokhudzidwa ndi zoopsa – sitikufuna kuoona zomwe ziri zoono. Timadula mitengo, anzathu, abwenzi athu. Timawononga Dziko Lapansi ndi makina, kupha. Timanamizira kuti akufa alibe chochita ndi ife. Timaganiza kuti maloto sioona. Timatcha mizimu *psychology* ndikuyesa kuiichotsa ndi ndodo za DSM. Sindikufuna kuoona, kumva, ndipo chifukwa chake sindikufuna kulankhulanso. *Trauma* imatisokoneza koterokuti sitidziwanso chomwe chili choona, ndi chomwe chili bodza. *Trauma* imadula mbali za ife tokha: umunthu wathu, mphamvu yathu yodziwiratu (*intuition*), kulingalira kwathu – ndipo ndiye timabisa mitu yathu m'mchenga, tikuyembekeza kuti titsamwe ndikupita ku zinthu zabwino. Kukhala olimba mtima moona kumakhala kovuta kwambiri, osati kosavuta. Moyo ofooka kwambiri. Zambiri zili pachiopsezo. Kufooka kwa kukhalapo kwathu kukukhala kowopsa kwambiri.

Ndikudzuka kachiwiri, nditanyowa.



"Ndi mzimu oipa. Udzapita," akutero mphunzitsi wanga, akumwetulira. Palibe chomwe chimumsuntha. Palibe chomwe chimamudetsa nkhawa. Ndi shaman, kotheratu.

Chinthu choti mukumbukire za zikhhalidwe zachikhhalidwe ndikuti ndizochita zinthu mwanzeru (*pragmatic*). Anthu kumeneko amakhala miyoyo zovuta, ndipo sachita nao zinthu ndi mtima onse zomwe sizigwira ntchito, zopanda zotsatira. Ku nzeru za zikhhalidwe zachikhhalidwe, zozikidwa pa dziko lapansi, ndife omwe tili amisala, chifukwa ndife omwe tili ndi chidwi ndi lingaliro la "chikhulupiriro mwa Mulungu". Chikhulupiriro. "Chikhulupiriro mwa Mulungu", mosiyana ndi "kukhala mu chikhulupiriro", kutanthauza kwambiri "kukhala mu kudalira", ndi lingaliro chabe, ndipo ziribe nzeru. Lilibe kulumikizana ndi dziko lakuthupi, kugwiritsa ntchito chidwi chathu ndi kugawikana ndi kulekana, "kupereka kwa Mulungu zomwe ziri za Mulungu ndi kupereka kwa Kaisara zomwe ziri za Kaisara" – m'malo moluka uzimu m'miyoyo zathu. Onani, ngakhale mau amenewo ndi opusa. Lingaliro ili lakuti ndife omwe timasankha kuluka uzimu m'miyoyo zathu, ngati kuti ndi chisankho, ngati kuti moyo omwe si mphatso kale yochokera ku mzimu, yomwe ikuyenda kale mwachimwemwe kudzera mu zonse.

Chimodzi mwa zinthu zomwe asing'anga amaphunzira msanga, ndikuti kuchiritsa kulikonse ndi kusintha, chisomo, mchitidwe olenga. Choncho kuchiritsa chilichonse kumafuna njira yatsopano, yolenga, yomwe idzakhala yosiyana ndi zomwe zinachitika nthawi yapitayo. Ogwiritsa ntchito aliyense ndi otenga nao mbali mu mwambo amadziwa izi – kuti mwambo ulionse ndi osiyana kwambiri ndi omwe unabwera kale ndi omwe udzabwera pambuyo pake, ngakhale ngati ndondomeko, kalembedwe, mwambo, chinthu, otenga nao mbali ngakhale cholinga cha mwambowo ziri zofanana. Ndipo chifukwa cha izi, nthawi zambiri, kuyandikira vuto lomwe likuwoneka kuti likuchita chimodzimodzi, ndi mayankho omwe anagwira ntchito kale sizimveka kwa sing'anga wachikhhalidwe. Zili ngati misala zotchuka zobwereza chinthu chomwecho mobwerezabwereza. Lamulo, mu zomwe ndakumana nazo likuwoneka kuti liri – ngati linagwira ntchito kamodzi kale, silidzagwiranso ntchito. Zovomerezeka, ndinathyola khosi langa pa lamulo ili nthawi zambiri—ndinagunda mutu wanga pakhoma mobwerezabwereza, kumva otetezeka ndi njira zina, kufuna zotsatira zomwezo, kuyandikira mavuto obwereza ndi kutalikirana kwachipatala. Iyi si njira yomwe kuchiritsa kumagwirira ntchito. Nthawi zonse ndi vuto, nthawi zonse ndi latsopano, nthawi zonse ndi vuto latsopano, lofunana yankho latsopano – chifukwa ndife omwe tikufunika kuphunzira chinachake chatsopano, chinachake chomwe sitinkachidziwa kale.

M'lingaliro limeneli, kuchiritsa kwachikhhalidwe ndi njira yophunzira yeniyeni – kuphunzira kukhala ndi chidwi nthawi zonse, kukhala wasayansi nthawi zonse munjira. Njira yasayansi yachinsinsi yophunzira, kumene nthawi zonse timayamba: "Sindikudziwa, sindikudziwa, sindikudziwa". Ndipo pemphero, lomwe



limalunjika pempho, limatsegula chidebe cha chikondi kunena: chonde, ndiwonetseni. Chonde, khalani nane. Chonde, ndithandizeni.

Tili tsopano, tonsefe; myambo zachibadwidwe, ndi anthu a kumadzulo chimodzimodzi, mu zochitika zatsopano. Kugawikana sikungathandizenso aliyense wa ife. Kuiuika malingaliro ena, kapena anthu, kapena zikhaliidwe pamapulatifomu sikungatithandize. Tikukumana ndi mavuto omwe sanachitikepo. Tonsefe tikupempherera mayankho atsopano, olenga, omwe adzachokera ku kuphatikiza kwakukulu kwa mavuto ndi anthu omwe akuwanyamula. Tonse tili m'mene muno limodzi.

\*\*\*

Titapulmuka dzinja loopsa lija, miyezi pambuyo pake, mlongo wanga akundipempha mwambo wamapemphero womveka bwino. Chinthu chophweka, njira yoyambira yomwe ingathandize kukulitsa mchitidwe wake. Timakhala ndi manyazi bwanji, polankhulana ndi Mzimu. Timakhala apamwamba bwanji. Timafunafuna bwanji mau olondola, njira yolondola. Tikudziwa kuti m'pemphero timaonedwa, komabe sitikudziwa momwe tingaonedwere. Timabwera bwanji mu ubale ndi mzimu? Tiyambire kuti? Timayamba m'pemphero. Ndi kukhazikika kwa malo, kutsegula kwa malo opatulika, ndi mphatso. Timapereka kuthokoza. Kenako timapempha kumvetsetsa. Timaperekanso zikomo. Kenako timamvetsera. Kutsegula maso athu, makutu athu, mitima yathu. "Ndiloleni ndikuwoneni. Ndiloleni ndikumveni. Khalani nane, m'zinthu zonse. Gwirani dzanja langa, gwirani mtima wanga. Chitani chimodzimodzi kwa iwo omwe amadana nane, kuti asamvenso kufunikira kodana. Chiritsani miyoyo za iwo omwe andilakwira, kuti asamvenso kufunikira kolakwira wina aliyense. Ndinu chikondi. Ndisungeni mu chikondi chomwe muli. Zikomo. Tionana mawa. Tionana lero. Tionana pamene ndikuchoka pano. Ndinu chikondi changa. Ndine chikondi chanu."

"Wow. Zoonadi, ku Zimbabwe, waphunzira kupemphera," mlongo wanga akundiiza.

\*\*\*

Ngoma, kuvina ndi anthu. Mwambo ndi olemkezeka! Mzimu umabwera, umalankhula Choonadi, ndipo Choonadi chimalandiridwa. Mapazi anga akuvina mpumulo mu nthaka, chifukwa ndikudziwa, potsiriza, chifukwa chake ndili pano – cholinga changa sichikuzemba.

Pulofesa kapena Professor wa *Anthropology* ku Poland nthawi ina ananena chinachake chomwe chinapangitsa zomwe ndakumana nazo kukhala zomveka pang'ono – "*Shamans* amabadwa ndi mphatso. Ali kunyumba mu dziko la Mzimu. Ndipo akapita kumeneko, kaya Mizimu zakwiya nao kapena kaya akusangalala limodzi, chomwe chiri chofunikira ndichakuti *shamanali* kunyumba kumeneko – Mizimu singathamangitse *Shaman*. Angachite zimenezo kwa anthu ena, koma osati kwa shaman. Iyi ndi mphatso yomwe *shaman* amabadwa nayo. Si njira (*technique*)."



Pamene nyenyezi za ku Africa zikundi yang'ana pansi, ndikudziwa *shamans* amabadwa, osapangidwa. Opatsidwa mphatso ndi mizimu, osati ndi anthu. Moto ukugawanika kukhala kumwetulira kowala, kutumiza zothetheka mumlengalenga ndi kuwunikira nkhope za anthu akuseka, kuyimba, kuvina. Komabe, *Shamans* omwewo amavomerezedwa ndi anthu – ayenera kutero, m'moyo uno, kuti kumanga milatho kukhale ndi nzeru.

Ndikuganiza izi zikupita kutali kufotokoza zomwe zikuchitikira anthu ambiri padziko lapansi masiku ano, pamene *shamans* ambiri akudzuka ndi kubadwa kuti alipirire onse omwe gulu lathu limawapha, monga zikhalidwe za utsamunda zinachitira myambo zachibadwidwe kapena kuwotcha kwa mfiti ku Europe kapena kusaka ndi kupha shamans ndi Boma la Soviet; izo, kapena amaikidwa m'zipatala ndi kutchedwa amisala – masomphenya awo ndi kuitanidwa kwao kupotozedwa mu matenda a maganizo.

*Shamanism* si njira. Palibe amene angakuphunzitseni. Koma ndi chinthu chenicheni ndi chofunikira. Kuitanidwa koono.

\*\*\*

Pamapeto, izi ndi zomwe mphunzitsi wanga akundi uza:

"Makolo ako andipatsa uthenga umodzi kwa iwe – pambuyo pa zomwe tachita pano, wamaliza, usapitenso kwa asing'anga alionse, tsopano uyenera kulankhula ndi mizimu zako mwachindunji, kulankhulana kwako kwambiri kuyenera kukhala nao. Uyenera kukhulupirira mizimu zako. Chifukwa ikuongolera ntchito zako, choncho si chisankho chako—uyenera kubwera kwa iwo ndi chilichonse, kuwafunsa, kudzipatsa wekha nthawi ndi chisankho chilichonse. Ayenera kukuuza tsopano, choti uchite, komwe uyenera kupita. Anthu ngati iwe – anthu omwe amachita mwambo – alibe malo okhazikika okhala. Monga Chaminuka, Ambuya Nehanda, ankayenda kuchokera kudera kupita kudera kuchita mwambo ulionse omwe unali wofunikira – osati zambiri, osati zochepa. Mnzako wa moyo ayenera kumvetsetsa zimenezo, ngati upeza mnzako wa moyo – ngati amvetsetsa, zidzakhala bwino. Kumvetsetsa ndi chisomo chomwe chimaperekedwa – makolo ako komanso, maso awo ali otsekedwa ku ntchito zako, koma si lioongo lao. Maso awo adzatsegulidwa ndi Makolo. Izi zidzachitika pambuyo pake. Msewu wa Mzimu ndi opanga Mtendere si ophweka. Ndiwe mtumiki wa Mzimu, mkulu – ndi bwino kuti uli pano. Otumidwa ndi Mzimu. Pemphera kwa iwo pa chilichonse. Ukabadwa Svikiro, sungathawe zimenezo. Kodi ungathawe mthunzi wako? Umakutsatira nthawi zonse– chifukwa cha ubwino wako. Makolo ndi amithenga ochokera kwa Mlengi, ndi omwe timawafunsa. Izi zitanenedwa, Mzimu ndi wachinsinsi. Masiku ano anthu amaganiza kuti uyenera chabe kugula nsalu, ndodo yoyendera ndi bute ndipo wamaliza, koma sizili choncho. Mzimu sukhalala mu nsalu. Thupi langa ndi nsalu yao. Amakhala m'thupi. Chilichonse chiyenera kuchitidwa ndi mtima oyenera, ndi cholinga choyenera, ndipo ndife anthu ndipo sudziwa zomwe zimakhala mu mtima wa sing'anga. Ndipo tonse timalakwitsa ndipo tsopano



ndikhoza kulemba nkhani zatsopano zopanda zolakwika – nkhani zako, nkhani za moyo wako zilinsu nkhani zochiritsa. ... Chinanso chiyani? Yenda ndi mankhwala, nthawi zonse. Mawa tikuyamba ntchito. Pempherera adani ako, apatseni mphatso, kenako choka. Sitinatumizidwe kuno kukonda anthu abwino okha kapena anthu omwe amatikonda. Kuuluka ndi njira yoyendera, si koipa. Ngakhaleenso kukhala ndi ana. Mzimu tsopano ukugogoda pakhomu pa aliyense ndipo ayenera kuyankha tsopano. Osati pamene ali ndi nthawi kapena pambuyo pake, koma tsopano. Ndipo tiyenera kumvetsetsa kuti chilankhulo cha Mzimu chimakhalanso mu zotsutsana—ndi chinsinsi. Ndipo ndi chikondi, zonse ndi chikondi, ndipo tili pano kukondana wina ndi mzake ndi dziko Lapansi komanso. Dziko Lapansi likufunika kuchiritsidwa. Tikufunika akulu kuti ayambitse moyenera. Tapatsidwa mphatso zosiyana, sitingakhale ofanana tonse—tonse ndife osiyana, ndi mphatso zosiyana.

Tengera chilichonse kwa Makolo. Chilichonse. Adzalankhula nawe.

Usiku, ndikudzioona ndekha, mwana yemwe ndinali, mu bokosi. Ndege ikunditenga mmwamba, mmwamba, mu thambo la usiku. Bokosi likukhala dengi. Ndege ikusungunuka, ndipo dengi likuyenda, kuyandama, m'mbali mwa mtsinje wa nyenyezi. Ndipo ali pamenepo, nkhope zomwetulira za mikango, *njuzu*, anthu, agogo aamuna ndi agogo aakazi. Ndili kunyumba.



Karolina Bieniek  
Urszula Markowska-Manista  
Paulina Brelińska-Garszka

## LUSO NGATI KUKUMANA

### **Njira zofotokozerera zotsekera ndi kutsegulira zatsopano**

### **Kuwunika kwapafupi kwa malingaliro a Fifi Mbogho, Samba Yonga, Natasha Omokhodion-Kalulu Banda ndi Lilian Hippolite Mushi**

### **MAWU OYAMBA – Nkhani za amayi mkati ndi kudzera mu luso**

Luso limagwira ntchito ngati chopatsira chidziwitso, makamaka chifukwa "limakhala" (*becomes*) osati chabe "lilipo" (*is*) kumene chatsopano chimasokoneza chakale, ndi kumene umunthu umakhala m'malire kapena kukhalira limodzi ndi chilengedwe, pakati pa "zinthu zogwirika" ndi "zinthu zosagwirika", mu zokambirana. Ndi lothandiza pakupeza kulumikizana pakati pa zochitika zomwe anthu amakumana nazo m'mbiri yakale yomwe imawazungulira komanso mbiri ya malo omwe amakhala. Limathandizira maulendo opita m'mbuyomu ndi mtsogolo, kupereka malo a kupezeka, kusokoneza ndi kumanga tanthauzo.

Zotsatirazi ndi zigawo za nkhani za amayi anayi omwe akukhudzidwa ndi luso lamakono m'malo osiyanasiyana ku Africa ndi Europe. Iwo amapeza mphamvu mu ntchito yawo kuchokera ku kuzindikira kwa kuthekera kobadwa nako kwa luso, kukhala kwake kwa onse (*universality*) ndi kuwoloka malire komwe kumathandizira kusinthana kwa chikhalidwe ndi pakati pa makontinenti. Kuchokera ku kawonedwe aka, amawona luso ngati chida chokulitsira luso la kuganiza mwaluso ndi kulingalira, zinthu zomwe ndi zofunika kwambiri popanga mayankho atsopano ndi kubweretsa kusintha kwa anthu. Njira zawo zotulukira sizili kudzera mu kuchita monga kafukufuku wawo kokha komanso kudzera mu kusintha kwa digito, komwe kumathandizira kuthekera kogawana zochitika ndi malingaliro.

Kwa amayi ambiri omwe akukhudzidwa ndi ntchito zothandiza anthu kudzera mu luso, lusoli limawonetsa mbali imodzi mafunso osatha, osadziwika, zovuta ndi zopinga za gulu la anthu pamene, mbali inayi, limatenga mawonekedwe a malo okhala ndi mbali zambiri omwe munthu angafunefune mayankho a mafunso awo ndi mafunso a ena ndi kuwakambirana pamalo ndi padziko lonse lapansi.

Mawu a amayi omwe akufuna kulemeretsa kuthekera kwa anthu kudzera mu luso lamakono akuchulukirachulukira kumveka. Amayi ndi oyambitsa machitidwe,



kuyanjana ndi mgwirizano m'munda wa luso lamakono, kupanga chimango cha kukumana komwe cholinga chake ndi chidziwitso ndi kusinthana kwa luso.

Nkhani zawo zikuwonetsa kuti kumasula (*deconfining*) kumangotumikira ngati chiyambi mu ndondomeko yopeza, kumasulira ndi kutanthauzira matanthauzo. Ndi ndondomeko yomwe imayambitsa kupanga ndi kupanganso chidziwitso ndi kulingalira kwa luso monga zomwe zimalola anthu kupitilira malire komanso kukhala oyambitsa, ogwira ntchito, ndi otenga nawo mbali. Ndi chitsimikizo kuti ndondomeko yotsatira imabweretsa zovuta zomwe zimalimbitsa kupirira kwa kulenga limodzi mu polojekiti.

Ndi ndondomeko yopeza zodziwika bwino komanso nthawi yomweyo zatsopano, zotsekedwa mu zokambirana zambiri ndi zochitika zosiyanasiyana, zomwe zikuwonetsa kuti pophunzira zochitika zosiyanasiyana za luso, ndi kuwona kuthekera kwake, n'zotheka kupanga zatsopano ndi kugwirizana mphamvu kuti apange malo a luso lamakono amphamvu ndi mitundu yolemera ya kufotokoza. Kumasula kumalolanso machitidwe a chidziwitso chachibadwidwe kubwezeretsedwa ndi mtengo wawo wa luso kuwonetsedwa.

"Kumasula (*Deconfining*) kumangotumikira ngati chiyambi ndipo m'tsogolo, padzakhala zambiri zomwe tingagawane, kuphatikizapo zikondwerero ndi mapulogalamu ambiri osinthana m'malo mongokhala malo okhala (*residencies*). Ndikuganiza kuti tikhoza kufika pofika poti tikhoza kuchita malo okhala a osunga ndi ofufuza, chifukwa ndikukhulupirira kuti tili kale ogwirizana pang'ono kulinga ku cholinga chomwechi." (Fifi Mbogho 2023).

Muzopereka zawo, onse akuwonetsa (m'malingaliro awo) magulu ofunikira omwe amamanga njira yomvetsetsa luso. Kwa ife, magulu awa akhala magulu a nkhani zamoyo za kufunsa kwapakati pa maphunziro m'munda wa luso. Palibe chomwe chiri chodziwikiratu mu luso. Zimakhudza zamoyo, zinthu, dziko lopanda moyo, malo, mipata, zolengedwa ndi zochitika zosonkhanitsidwa. Luso ndi lotenga nawo mbali. Ndi ndondomeko, mndandanda wa zochitika ndi zokumana nazo momwe kutenga nawo mbali kuli gwero la chidziwitso, kukumana kwatsopano, zovuta ndi zopinga. Nthawi yomweyo, zimabwera ndi kuzindikira kuti mukakumana ndi luso, kulisanthula, kulitanthauzira, ndi kulingalira pa ilo, palibe chomwe chidzakhale chimodzimidzi kachiwiri. Luso limapangitsa kuti zitheke kuwoloka malire owoneka ndi osawoneka.

Mbiri ya dziko yozikidwa pa maubwenzi a mphamvu ikuwonetsa kuti, mwachitsanzo, panthawi ya ndondomeko za kugonjetsa ndi utsamunda, nkhani zambiri zachibadwidwe, zigawo zofunika za chidziwitso chopangidwa ndi amayi,



zayiwalika kapena kuzulidwa pamene amayi nawonso afafanizidwa ndi kusiidwa m'nkhani zofunika za mbiri yakale.

"Mukaganizira za mabungwe a chidziwitso ndi momwe chidziwitso chimapangidwira – chimalembedwa m'mabuku, kaya ndi mapepala, kaya ndi zida zamaphunziro ndi ntchito za akatswiri - koma m'machitidwe athu a chidziwitso chachibadwidwe, chidziwitso chochuluka chinalembedwa kudzera mu luso, kudzera mu kusimba nkhani, kudzera mu nkhani za makolo athu, ndipo zambiri za izo zinatengedwa ngati zopanda ntchito monga chidziwitso. Kuti sizinembedwe pamapepala, zinawonedwa ngati zoipa kwambiri – ndiye sizimawonedwa ngakhale ngati dongosolo la chidziwitso" (Samba Yonga 2023).

Masiku ano, amayi akugwiritsa ntchito mwanzeru ndi mwaluso matekinoloje atsopano, kugwirizanitsa kuchuluka kwa mitundu ndi masitaelo poyesetsa kubwezeretsa zopereka za amayi ku chidziwitso ndi kuziphatikiza mu njira zazikulu ndi zofunika zachilungamo cha anthu.

Kulenga, kudzifotokoza wekha kudzera mu kuchuluka kwa mawonekedwe (komwe luso lili nako) ndiko kuphunzira milingo yosiyanasiyana ya kulankhulana ndi mayankho ku kulankhulana m'maiko omwe nthawi zambiri amakhala osagwirizana ndi otsutsana ndi zenizeni zanthawi zonse zomwe tadziwika nazo, komanso ndi maphunziro omwe talandira ndi zomwe timadziwika nazo. Chifukwa chake luso ndi chida cha kulankhulana ndi kudzifotokoza. Limadzifotokoza lokha kudzera mwa wotumiza—wojambula—ndi wolandira—wowonera, owerenga—omwe ali olenga nawo omasulira ndi kubweretsanso chidziwitso. Motero amatenga nawo mbali mu ndondomeko yotseguka ya kusinthana chidziwitso, malingaliro ndi nkhani, zomwe ndi gawo lofunikira la ndondomeko yomanga maubwenzi ndi malo osiyanasiyana ndi ntchito zaluso ndi kuthana ndi mikhalidwe ya chikhalidwe, chipembedzo, chikhalidwe cha anthu, chilengedwe, nyengo, ndale ndi zina.

## **Nkhani 1**

### *KULEMERETSA KUTHEKERA KWA MUNTHU KUDZERA MU NJIRA YA LUSO LAMAKONO*

